KMN No. 1
OMBA LIPENGA
W J. Kirkpatrick
Doh is Bflat

1. Mlonda lalika uthenga, Chenjeza anthu onse,
   Iye wakumva adzetu, Nakhale nawo moyo.

   CHORUS
   Omba lipenga mlonda'we, Anthu onse, amvetu,
   Lalika atero Mulungu! Onse amasulidwe.

2. Lalika m'mapiri monse, M'mkhalango ndi m'madambo;
   Lalikiranso m'zinyanja, Ndi nyimbo yokondwera.

3. Lalikira ponse ponse, Kumene kuli mdima;
   Amve kuti zones zapsya. Atate alindira.

4. Lalikira kwa othodwa, Akufuna mpumulo;
   Yesu ali kuitana, Idzani kwa Inetu.

No. 2

# INDETU PAKHOMO

F.E. Belder

Doh is G

1. Mfumu yathu iri kudza, Yomwe inafera ife;
   Koma olungama okha, Adzapita nawo.

   CHORUS:
   Indetu pakhomo Ali pafupitu pakhomo.
   Ali kudza (inde) ali kudza ( Mbuye) Inde ali pakhomo.

2. Zizindikiro Zakezo, Ziri kukwanitsidwatu,
   Posachedwa tidzam'ona, Akudza m'mitambo.

3. Musayang'ana pa dziko, Kupeza mtendere wathu,
   Mpaka Yesu adzabwera, Kudzachotsa imfa.

4. Pompo m'dziko latsopano, Tidzakhalamo kosatha,
   Imfa sidzakhala uko, Ku nthawi zosatha.

No. 3
MASO NDI MASO
Grant Colfax Tullar
Doh is B flat

1. Maso ndi maso ndi Khristu, kodi ndidzachitanji?
   Mmene ndidzaona Yesu, Yemwe anandifera.

   CHORUS:
   N'dzamona maso ndi maso, Kuseri kwa mitambo :
   Posachedwa ndidzamona, Mulemerero Wake!

2. Tsopano ndimona Iye, Mwa chizimezimetu,
   Tsiku lija ndidzaona, ulemerero Wake.

3. Pamene zowawa zones, Nthenda ndi imfa zitha,
   Dziko likadzakonzedwa, Ndidzakondwa koposa!

4. Lodala tsikulo m'mene! Ndidzamuona Yesu;
   Mpulumutsi wanga yemwe, Anandikonda ine.

No. 4

ALI KUDZA

Arranged

Doh is e flat

1. Timamva uthenga wabwinotu, M’mene tiri kunka kwathu!
Msanga Mpulumutsi adzabwera, Kukhala Mfumu yathu.

CHORUS:
Ali kudza posachedwa, Inde, ali kudza pa dzikoli;
Ndipo tidzapita tonse kumwamba, Pakubwera Yesuyo.

2. Manda a anthu oyera mtima, adzatsegulidwa ndithu;
Ndipo onse ogonera m’mandamo, Adzakhalanso moyo.

3. Sitidzalekananso kkwathu’ko, Tidzayimba za chombolo;
Anthu a mitundu yonse adzadza, Kupembedza Mfumuyo.

4. Tidzayimba aleluya, Amen! Msanga tikasamalira;
Dikirani ndi kupemphera nonse, Tidzabvala korona.

No. 5

KULI BWANJI KWATHU?

Arranged

Doh is E flat

1. Kuli bwanji kwathu? Ndinafunsa, mlonda iye nati:
   Usiku wapiti ndithu, kwayandika kucha.
   Usalire, yendabe ndi chiyembekezo chodala,
   Mpaka udzafika m'mwamba pa tsiku losatha.

2. Ndafunsa mslikari wa Khristu, iye nayimba nati:
   Ndidzamenyanatu nkhondo patsala pang'ono.
   Usalire, pirira kufikira nkhondo idzatha,
   Pakuti olakika adzalandira mphotho.

3. Ndinafunsa dziko, Nyanja ndi dzuwa izo zinati:
   Nthawi iri kutha Yesu ali pafupitu,
   Usalire- zizindikiro ziri kuonekatu,
   Chilengedwe chonse chilindira kudza kwake.

4. Kwathu mpafupitu! Mau osangalatsa mtima'nga,
   Omwe adapukuta misonzi ya olira,
   Usalire tidzakomanatu osalekananso,
   Zobvuta zitatha m'nyumba ya Atate wathu.

No. 6
YESU AKUDZA
Wm J. Kirkpatrick, by per
Doh is D flat

1. Yang'anirani Akhristu; Zammwamba zigwedezeka,
Yatsani nyali zanuzo, Kukomana naye Mbuye.

CHORUS:
Onani Yesu adza; Akudza mulemerero,
Adzakhala mfumu yathu, Onani! Ali kudza.

2. Ona lonjezano Lake, Wakhulullukira tchimo,
Mwazi nutsuka minjiro, Nena nthano ya chombolo.

3. Mafumu anjenjemera, Imva! Ali kudza ndithu
Nena za chisomo Chake, M'mene lipenga lilira.

4. Mitundu yonse idzatha, Khristu wafulumiratu;
Dziko liri kutha ndithu: Mbuye wathu ali kudza.

5. Yesu aitana nonse, Akupembedzera inu;
Kangaza nthawi ikutha, Ungadzatsaletu kunja.

No. 7

## YESU ADZA KUWERENGA

Geo. F. Root

Doh is E.  Moderato

1. Yesu adza kuwerenga Ana ‘ke abwino,
   Ngale zake zowalitsa, Okondwedwawo.

   CHORUS:
   Ana omwe angonga Nyenyezi za mmwamba,
   Nadza naye mokondwa , Onyezima nye.

2. Yesu adzasonkhanitsa oyera mu mtima
   Ana ake onyezima, Okondedwawo.

3. Ana, inde, ana Ake Ndi  nyenyezi Zake;
   Adzakhala owalitsa, Okondedwawo.

No. 8
PAKWITANA MBUYE WANGA
J. M. Black
Doh is A flat

1. Pakwitana mbuye wanga potsiriza dzikoli,
Pakufika tsiku la kuwalalo,
Posonkhana akumvera,pakuona Yesuyo,
Ndidzakondwerera naye komweko

CHORUS:
Pakwitana Mbuye Wanga ( Mbuyanga),
Pakwitana Mbuye Wanga (Mbuyanga),
Pakwitana Mbuye Wanga,
Ndidzakondwerera naye komweko.

2. Poturuka m'manda mwawo, anthu Ake onse
Tidzaganatu nawo nthawiyo.
Pakuuka osankhidwa, kunka naye Yesuyo,
Ndidzakondwerera naye komweko.

3. Tisaleke kugwirabe ntchito ya Mulunguyo,
Tibukitse mbiri Yake m'dzikolo,
Ndi podzatha moyo wathu ndi zintchito zathuzo
Tidzakondwerera naye komweko.

CHORUS(lotsiriza)
Pakwitana Mbuye wathu (Mbuyathu),
Pakwitana Mbuye wathu (Mbuyathu),!
Pakwitana Mbuye wathu,
Tidzakondwerera naye komweko.

No. 9

## OMBA LIPENGA

Geo. E. Lee

Doh is A

1. Omba lipenga, limveke pone; Yesu adzabweranso!
   Kondweranitu, yimbani nyimbo; Yesu adzabweranso.

   CHORUS:
   Abweranso, abweranso, Yesu adzabweranso!

2. Lalikirani m’phiri ndi m’dambo; Yesu adzabweranso!
   Adzadza m’ulemerero Wake; Yesu adzabweranso!

3. Lalikirani m’zinyanja monse; Yesu adzabweranso!
   Lalikirani ponseponsepo; Yesu adzabweranso!

4. Zibvomezi zimanena kuti; yesu adzabweranso!
   Namondwe ndi mafunde zinena; Yesu adzabweranso!

5. Mitundu yakwiya tidziwatu; Yesu adzabweranso!
   Zizindikiro zakwanitsidwa; Yesu adzabweranso!

No. 10

## KODI TIDZASONKHANADI?

Rev. Robert Lowry

Doh is E flat

1. Kodi tidzasonkhanadi, Pali mtsinjewo wa moyo,
Wakuyenda nthawi zones, Kwa Mulungu m’mwambamo.

CHORUS:
Inde tikomana komwe, Ku mtsinje wakukoma wa Mulungu;
Titsagane ndi olungama, Pa mtsinje m’mwambamo.

2. Pa magombe apa mtsinje, Tidzayendayenda komwe!
Tidzalemekeza Mlungu, Nthawi zones zonsezo.

3. Tisanadze pa magombe, Tidzatula akatundu.
Yesu adzatilandira, ‘Dzativeka tonsefe.

4. Msanga tikomane komwe, Potsiriza pa ulendo,
Msanga tidzakondwerabe, Timyimbire Mlunguyo.

No. 11

## NDIDZAKUTSATANI

James Lawson

Doh is A flat

1. Ndidzakutsatani Mbuye, Kulikonse mupita;
   Ndidzakutsatani Mbuye; Inde n’dzakutsatani.

   CHORUS:
   Ndidzakutsatani Mbuye, Yemwe munandifera;
   Ngakhale akukaneni, Ndidzakutsatani’ Nu.

2. Nkana njira ndi ya minga Yopanda matakadzo,
   Mukandikonzera Ine, Mokondwa n’dzatsata’nu.

3. Nkana chisautso chidza, Kapena ndiyesedwa;
   Mbuyenso anayesedwa koopsya Ndidzamtsata mokondwa.

4. Nkana ndipeze mabvuto, Sindidzakukanani;
   M’nazunzidwanso koopsya Ndidzamtsata mokondwa.

5. M’mafunde ndi mozamamo, Mudzanditsogolera;
   M’nayenda m’mafunde kale, Ndidzakutsatani’ Nu.

No. 12
KASUPE ALI WODZAZA
Unknown
Doh is C

1. Kasupe ali wodzaza, Ndi mwazi wa Yesu;
   Omwe asamba mwa uyu Ataya zoipa.

2. Woba wakufa napenya, Kasupe nakondwa;
   Ndi ine enso mwa uyu, Ndisamba ndiyera.

3. Mwazi wa Yesu wokondwa, Ukhala wamphamvu.
   Kwa ana onse a Mlungu Uchita kuombola.

4. Mmene ndapenya mwazi wa Mabala Anuwo,
   Kukonda kwanu nditama Kwa kutha kwa moyo.

5. Ndikhulupirira kuti Mwakakonza malo
   Ndipo ndidzalowa ine ku moyo wosathat.

6. Kumwamba ndikayimbanso Zimphamvu za Mlungu,
   Zopulumutsa onsewa Omvana ndi Yesu.

No. 13

# NDIYERETU MBU

WM . G. Fischer

Doh is A

1. Ambuye ndifuna nditsuketu, Mukhalitse ndine mu mtima'ngamu;
   Muthyole zonsezo zodetsa'netu, Musambitse ine, ndiyeretu mbu!

   CHORUS:
   Ndiyere mbu, E, ndiyere mbu,
   Musambitse ine, ndiyeretu mbu.

2. Ambuye taonani pansi pano, Kuti m'ndithandize kudzipereka;
   Ndileke zangazo zoipsya'netu, Musambitse ine, ndiyeretu mbu.

3. Chifukwa cha ichi ndipempheratu, Ndidikira Inu Ambuyanga'Nu;
   Ndikhulupirira pa mwaziwo pyu, Musambitse ine, ndiyeretu mbu.

4. Ambuye muona ndidikira'Nu, idzani kukonzetsa mtima wanga;
   Omwe akutuna simuwakana, Musambitse ine, ndiyeretu mbu.

No 14.
IMVA ATAMBALA
Wm. J. Kirkpatrick
Doh is C

1. Imva makobidi, tiri kuponya!
   Tiri kupereka onse kwa Yesu.

   CHORUS:
   Ngwingwi, ngwingwi, Ngwingwi, ngwinhwi;
   Tiri kuponya! Tiri kupereka, Onse kwa Yesu.

2. Tonse tipereka, kobidi lathu
   Kuti anthu ena amve za Yesu.

3. Pakuperekatu tiri kusunga;
   Pakubwera, Mbuye adzatipatsa.

4. Makamaka Yesu afuna ife;
   Kuti tipereke mitima yathu.

No. 15

## YESU ANDIKONDA ‘NE

W. B. Bradbury

Doh is E flat

1. Yesu andikonda ‘ne, Amatero m’bukhumo.
   Akafo’ka mwna ‘ke, Amlimbitsa Yesuyo.

   CHORUS:
   Yesu akonda, akonda ine,
   Akonda ine, Atero m’bukhumo.

2. Nandifera Yesuyo, Nagonjetsa tchimolo,
   Natsegula khomolo, Kuti ndinke kwawoko.

3. Yesu andikonda ‘ne Nkana ndikudwalatu,
   Mmene ndifookanso, Andisamalira ‘ne.

4. Yesu andikonda ‘ne, Ndikamkonda Iyeyo,
   ‘Dzanditenga inetu, Ndikakhale nayedi.

No. 16

## TIMAPAZI INU, SAMALIRANI

J. H Rosecrans

Doh is A flat

1. Ndasamba m'manja mwanga, Mwayeretsedwatu.
   Ndi kwapereka iwo, Ku ntchito ya Yesu.

   CHORUS:
   Timapazi inu, Samalirani,
   Musanditengere, Kuli zoipa.

2. Makutu amvetsere Pa tsiku lonseli,
   Ntchito yonse yabwino, Manjawa achite.

3. Maso anga aone, Ntchito zawo zones,
   Kutitu asachimwe, Chifukwa cha Yesu.

No. 17
CHIKONDI CHITIKONDWETSA
F.E. Belden
Doh is B flat

1. Chikondi chikondwetsa, Nichikonza njira;
   Chimatisangalatsa ife, Kukonda anzathu.

   CHORUS:
   Mulungu ndiye chikonditu, Ndifetu ana Akewo
   Chikondi chikondwetsa, Nichikonza njira;
   Chimatithangata ife, Kukonda anzathu.

2. Dzikoli nla chisoni. La imfa ndi nthenda,
   Tidzachita mbali yathu, Kuthangata ena.

3. Moyo uno ukatha, Tikadzanka m’mwamba,
   Tidzayimba kosaleka, Za kukonda Kwake.

No. 18
USAMALIRE MOYO WANGA ‘ WE
Lowell Mason
Doh is C

1. Usamalire ‘we Adani akowo,
   Ngambiritu mu dzikoli, Angakugwetse ‘we.

2. Limbika nkhondoyo, Masiku onsewo,
   Nupemphe Mlungu wakoyo Kukuthangata ‘we.

3. Usaganize ‘we Kusiya nkhondoyi;
   Sudzapumula mpakatu, Ambuye abwera.

No. 19

## AKHRISTU TIYENI

Sir Arthur Sullivan

Doh is E

1. Akhristu tiyeni! Nkhondo tigwire,
   Yesu Mbuye wathu, Atitsogoza.
   Ona Mbuye yekha, Atithandiza.
   Ndi mbendera Yake, Tiyitsatira.

   CHORUS:
   Akhristu tiyeni! Nkhondo tigwire,
   Yesu Mbuye wathu, Atitsogoza.

2. Nkhondo ya satana, Msanga ithawa,
   Akhristu tiyeni, Tidzapambana;
   Mphamvu zake ziha, Yesu titama;
   Yimbani anzathu, Nyimbo tikweza.

3. Gulu lalikuru, Adza Akhristu.
   Titsatana nawo, Ana a Mlungu.
   Sitipatukana, Tonse tikhala,
   Ndi mtima umodzi, Timakondana.

4. Zonse za pa dziko, Zidzatheratu;
   Koma mpingo Wake, Ukhalitsabe;
   Mphamvu ya Satana Idzalefuka;
   Yesu nalonjeza, Ndidzalimbitsa.

5. Idzani Akhristu, Kutithandiza;
   Nyimbo za Mulungu, Tidzayimbitsa;
   Khristu ayenera, Ndiye Mfumuyo
   Tidzamlemekeza, Nthawi zonsezo.

No. 20
MOYO WANGA DZUKA
Thos. Arne
Doh is G.

1. Moyo wanga dzuka limba, Thamanga ndi mphamvu;
   Korona wosatha ali, Kulindira iwe.

2. Mau a Mulungu wako, Akuitana'we;
   Dzanja Lake likufupa,Ngati ufunitsa;

3. Mtambo wa mboni wozinnga, Uyang'anira'we;
   Iwala zonse za m'mbuyo, Pitabe mtsogolo.

4. Mpulumutsi tikokeni, Tiyambe liwiro;
   Tidze pa mapazi anu, Kutula katundu.

No. 21

## NDIRI KUDZA KWA YESU

W. G. Fischer, by Per.

Doh is G

1. Ndiri kudza kwa Yesu, Ndasauka ndachimwa;
   Zonse zanga ndisiya, Kukapeza moyotu.

   CHORUS:
   Yesu ndikhulupira, Munafera inedi,
   Mwa  umphawi ndipempha, Mundipulumutsetu.

2. Inde, Inu ndifuna, Ndinachimwa kwambiri;
   Yesu ati Ndichotsa, Zakuipa zakozo.

3. Yesu zonse ndipatsa, Ziri zanu tsopano,
   Mtima wanga wonsewu, Muli mwini waketu.

4. Ndikhulupirani, Mwazi Wanu ndidziwa,
   Wayenetsa inenso, Ndapachikwa ndi Khristu.

5. Yesu adzandidzaza Mtima wanga wonsewu,
   Ine ndiri woyera, Yesu wanga nditama.

No. 22
INENSO
W. B. Bradbury
Doh is G

1. Mbuye ndamva muchitira, Anthu ena zabwino;
   Muli kuwadalitsira, Mudalitse inenso.

   CHORUS:
   Inenso, inenso, Mudalitse inenso.

2. Tate m’sandipitirire, Ndimaipa mtimamo;
   Ndiyenera imfa, Koma Chitirani chifundo.

3. Ndinagona mwa zoipa, Ndinakunyozanitu,
   Dziko lino ndinakonda Mundikhulululukire.

4. Mzimu m’sandipitirire. Mupenyetsa akhungu;
   Mumapatsa ena mphamvu, Mpatse mphamvu inenso.

No 23

## MUNDIFUNGATIRE INE

Jno.R.Sweney

Doh is G

1. Mundifungatire ine, Mzimu wakuyera ‘nu,
   Munditsuke mtima wanga, Inde, mudze leroli.

   CHORUS:

   Mudzetu, mudzetu, Mzimu wakuyera mbu.
   Munditsuke mtima wanga, Inde, mudzze leroli.

2. Mzimu, mudidzaze ine, Ndisowatu nzeruzo.
   Ndisowanso Inu, Mbuye Mundidzaze mtimanga.

3. Ine ndine wolefuka , Ndikugwadiranitu.
   Mzimu Inu mundidzaze Ndi chikondi Chanucho.

4. Dalitseni ine, Mzimu, Sambitseni mtimanga.
   Inu, Msangalatsi wanga, Mudze inde, leroli.

No. 24
NDIFUNA YESUYO
Rev. R. Lowry
Doh is A flat

1. Ndifuna Yesuyo, Ambuyanga,
   M'mtendere ndinkemo, Mwa Iyeyu.

   CHORUS:
   Ndifuna Inu, Yesu, Nthawiyi ndifuna,
   Kwa Yesuyo, Mbuyanga,Ndifunako.

2. Ndifuna Yesuyo, Mobvutamu,
   Ndipulumukemo Mwa Iyeyu.

3. Ndifuna Yesuyo, Mokondwa ndi
   Mowawa, adzemo ndi moyodi.

4. Ndifuna Yesuyo, ndichite 'ne
   Zofuna Zakezo, Ndidzazebe.

5. Ndifuna Yesuyo Woyeratu,
   Ndikhale Wakeyo, Wa Iyeyu.

No. 25

NDIPEREKA ZONSE

W. S. Weeden

Doh is D. Duets-S. & T.

1. Ndipereka zonse kwa Yesu, Zonse mwa ufulu;
   Ndidzamkonda Iye koposa, Tsiku liri lonse.

   CHORUS:
   Ndiperekatu, zonse kwa Yesu
   Zonse kwa Nu ndipereka dalitsenitu.

2. Ndipereka zonse kwa Yesu, Pa mapazi Ake;
   Zadziko ndazikana zonse, Nditengeni Yesu.

3. Ndipereka zonse kwa Yesu, Ndikhale wanutu,
   Ndimve Mzimu Wanu ndidziwe, Kuti Ndinu wanga.

4. Ndipereka zonse kwa Yesu, Wandipatsa mphamvu,
   Ndikondwera chipulumutso! Nditama dzinalo!

No. 26

NDISAUKA NDINACHIMWA

W. B. Bradbury

Doh is E flat

1. Ndisauka ndinachimwa, Koma Inu mwandifera,
   Ndipo ndamva mundi'tana, Mwana Mlungu ndingobwera.

2. Ndisauka, ndimasowa, Mphamvu ya kuyera mtima,
   Mwazi wanu unditsuka; Mwana Mlungu ndingobwera.

3. Ndisauka, sindikhoza Kwiletsa nkhondo mumtima,
   Ndi chisoni, mantha, nkhawa, Mwana Mlungu ndingobwera.

4. Ndisauka sindiona, Ndimadwala ndilefuka,
   Zonse ndizitaya kwa "Nu, Mwana Mlungu ndingobwera.

5. Inde, Yesu mulandira, Muchiritsa M'pulumutsa,
   Mau Anu ndibvomera, Mwana Mlungu ndingobwera.

6. Inde, Yesu, mundikonda, Zonse zina ndazitaya,
   Tsono kukakhala Wanu, Mwana Mlungu ndingobwera.

No. 27
M’TITSITSIMUTSE
J.J Husband
Doh is G

1. Tiyamika’ Nu Mulungu wokonda,
   Chifukwa cha Yesu Mwana wanuyo.

   CHORUS:
   Haleluya, tidzamtama, Haleluya, Amen;
   Haleluya timpembedza, Mulungu wathu.

2. Tiyamikira, Mulungu wamphamvu,
   Chifukwa cha mzimu Wanu Woyera.

3. Tiyamikira, Mwana wa Nkhosayo,
   Yemwe anafera zoipa zathu.

4. Tiyamika’ Nu, Mlungu wa chisomo
   Munatigula ndi mwazi wanuwo,

5. M’titsitsimutse, Ndi chikondi chanu,
   M’tiyatse ndi moto wa Mzimu Wanu.

No. 28
KHALATU WOYERA
Geo. C. Stebbins
Doh is F

1. Khalatu woyera, Pemphera mtseri;
   Werenga mau'ke, Masiku onse;
   Thangatani omwe Ali ofo'ka,
   Madalitso Ake funafunani.

2. Khalatu woyera, Dziko laipa;
   Pemphera kolimba, kwa Yesu Mbuye.
   Yang'anitsa Yesu, Ndi kumtsatira
   Kuti anthu ena Aone Yesu.

3. Khalatu woyera, Akutsogoze,
   Usamtsogolere, M'njira zakozo;
   M'nsoni ndi pokondwa, Tsata Mbuyako
   Khulupira Yesu Ndi mau Ake.

4. Khalatu woyera, Khala wofatsa,
   Alamulire 'Ye, Ganizo lako;
   Utatsogozedwa ndi Mzimu Wake,
   Msanga udzagwira ntchito ya mmwamba.

No. 29
MUKHALE NDINE
Wm. H. Monk
Doh is E flat

1. Mukhale ndine dzuwa lalowa, Wagwa usiku bwenzi lisowa,
   Ndiribe wina wondithandiza, Wa mphamvu ndinu, mkhale ndinetu.

2. Kamoyo kanga katha leroli, Zidzachokanso zinthu za dziko,
   Zimasinthika zoonekazo, Simusinthika mkhale ndinetu.

3. Koma kale mnakhalitsa pano, Mukhale ndine musachokenso,
   Sin'pempha kuti Mbuye mutsotse, Komatu mukhalitse ndinetu.

4. Ndifuna Inu tsiku lonsolo, Ndi mphamvu Yanu ndidzasungika.
   Mukatsogola sindiopai, Msana, usiku, mkhale ndinetu.

5. Adani sindiopa mulipo, Muletse tsoka ndi chisonichi,
   Ikadza imfa n'dzalimba mtima, M'imfa ndi moyo mkhale ndinetu.

No. 30
DZUWA LIRI KULOWA
W. F. Sherwin
Doh is A flat

1. Dzuwa liri kulowa; Mlungu atipumitse:
   Linda ndi kupemphera mmene nyali ziri kuwala m'mwamba.

   CHORUS:
   Woyera Ambuye wa makamu!
   Za m'mwamba ndi za dziko zitamanda Inu,
   Mulungu Wamkuru.

2. Ambuye wamoyo' Nu, ife tasonkhanatu
   Kufuna nkhope Yanu; mutifungatire'fe mkhola Lanu.

3. Pamene mthuzi ugwa, Mumatifungatira;
   Mwa chisomo chanutu, Mitima yathu ikwera kwa Inu.

4. Tikamwalira ife osaona za dziko,
   Ambuye wachifundo, mutidzutsenso tsiku lotsiriza.

No. 31
MOMBOLO WANGA, DZUWATU
Peter Ritter
Doh is F

1. Mombolo wanga, dzuwatu,
   La mtima wanga ndinudi,
   Palibe mdima mgatitu
   Mukawalira inedi.

2. Muchotse zonse zoti bii,
   Zobisa nkhope yanuyo;
   Mudzazetu mtimangawo,
   Ndi kuunika kwanuko.

3. Madzulo ano mkhaletu,
   Pafupi ndine Yesudi.
   Ndisanagone tuloto,
   Ndilingalira Inudi.

4. Kapena wina leroli,
   Wasocherera m'njirayi,
   Ya Inu, Mbuye,mbwezetu.
   Mumpulumutse iyedi.

No. 32

## NDIYE POTHAWIRA PATHU

F.E Belden

Doh is F

1. Mbuye ali thanthwe lathu, Ndiye pothawira pathu;
   Atipulumutsa m'zonse, Ndiye pothawira pathu.

   CHORUS:
   Ndiyetu thanthwe lolimba Ndi mthunzi nthawi yotentha;
   Mtsogozi wa aulendo, Ndiye pothawira pathu.

2. Pa nthawi ya usikuwo, Ndiye pothawira pathu;
   Palibe wotiopsya'fe, Ndiye pothawira pathu.

3. Nkana chigumula chidze, Ndiye pothawira pathu;
   Mwa Mlungu tipeza bwino, Ndiye pothawira pathu.

4. Inu thanthwe lokondedwa, Ndinu pothawira pathu;
   Khalani mthangati wathu, Ndinu pothawira pathu.

No. 33
MULUNGU ATSOGOZA ‘NE
Wm. B. Bradbury
Doh is D

1. Mulungu atsogoza ne Ndapuma m’mtima mwangamo.
   Ayang’anira m’njiramo, Poyenda ine konseko.

   CHORUS:
   Mulungu atsogoza ‘ne, Ndi dzanja-dzanja Lakelo.
   Ndidzamtsatira Mbuyanga, Poyenda ine konseko.

2. Masiku ena mdima bi, Ndimabvutika m’mtimamo.
   Pa nthawi zina nkondwadi, Popeza zokondwetsazo.

3. N’dzagwira dzanja Lanulo, Osang’ung’udza konsei,
   Ndidzanka mokondweratu, Pomtsata Mbuye wangayo.

4. Podzatha ntchito yangayi, Podzagonjetsa tchimolo,
   Kumene ndidzakhalatu, Sindidzaopa imfayo.

No. 34

# POKHALA MTENDERE

P.P Bliss

Doh is D flat

1. Pokhala mtendere mu mtimangamu, Pamene ndisaukanso,
   Pamene mabvuto ndi akurudi, Moyo wangawu ngwabwinotu.

   CHORUS:
   Moyowu uli phee. Moyo wangawu ngwabwinotu.

2. Ngakhale Satana atizunza ‘fe, Chiripo chitonthozo;
   Chifundo cha Khristu anafera ‘fe, Kundipatsa ‘ne moyo Wake.

3. Uchimo unapachikidwa pomwe, Pa mtanda wa Yesu Mbuye;
   Machimo angawo anatherapo, Mbuye wanga ndiyamika ‘ Nu.

4. Ambuyathu tikhumba tsiku Iija Limene tidzaona ‘Nu;
   Lipenga limveke, tidzakondwatu, Pakukomana ndi Yesuyo.

No. 35
CHIDZAKHALA CHIMWEMWE
A.J Showalter, by Per.
Doh is A

1. Chidzakhala chimwemwe choposa,
   Potsamira m’mikono Mwake;
   Kuli dalo kwa Mlungu wangayo,
   Potsamira m’mikono Mwake.

   CHORUS:
   Potsamira, Adzandipulumutsatu;
   Mwa zoopsya, Potsamira m’mikono Mwake.

   Bass and Tenor:
   Potsamiratu, Potsamiratu, Adzandipulumutsatu;
   Mwa zoopsyazo, Mwa zoopsyazo,
   Potsamira m’mikono Mwake;

2. Nkwabwinotu kuyenda m’njirayi
   Potsamira m’mikono Mwake.
   Njowaladi koposa njirayi,
   Potsamira m’mikono Mwake.

3. Ndiopanji ndi kuda nkhawanso,
   Potsamira m’mikono Mwake?
   Mbuyanga al inane pafupi,
   Potsamira m’mikono Mwake.

No. 36

NDIKHULUPIRA ‘NU

Lowell Mason

Doh is E flat.

1. Ndikhulupira ‘Nu, mwana wa Mlunguyo,
   Mbuyanga ‘Nu;
   Mumve popempha ‘ne, Tchimo muchotsebe,
   Lero ndikhale ‘ne, Wa Inuyo.

2. Mzimu mndipatseko, Wondilimbitsayo,
   Mu mtimamo;
   Munandiferadi, Ndiyambe leroli,
   Inu kukonda ndi Mtimangawo.

3. Poyenda m’mdima bii, M’mtimamo nsonizi,
   Mndigwiretu;
   Mdima uchoke zi, Msozi ulekedi,
   Ndisasocheneyi, Kwa Inuko.

No. 37

## NDIZE PAFUPIPA

Lowell Mason

Doh is G.

1. Ndidze pafupipa Mlungu wanga,
   ‘Ngakhale ndi tsoka Mundibweza,
   Koma ndiyimbabe, Mbuye m’ndikhalitse
   Mbuye m’ndikhalitse, mfupi Ndinu.

2. Ngakhale ku thengo Ndasochera,
   M’mdima ndinagonapo, E pa mwala,
   Koma m’kulotako, Ndiyandikizanso,
   Ndiyandikizanso, M’fupi Ndinu.

3. Pajapo ndipenya Pokwerapo,
   Angelo atsika Kumwambako,
   Ndiwo akodola Kuti ndibwerere
   Kuti ndibwerere M’fupi Ndinu.

4. Tsono poukanso Wokondwatu,
   Ndipeza pomwepo Pali Mlungu;
   Ndipo masautso Andisendezanso
   Andisendezanso M’fupi Ndinu.

5. Podzabwera Iye N’dzanka naye,
   Dzuwa ndi nyenyezi Zitsalira;
   Pomwe ndiyimbanso, Ndidza pafupipo,
   Ndidza pafupipo, Mlungu wanga.

No. 38
LIMBIKANI MWA MULUNGU
W. H Doane
Doh is E flat with spirit

1. Limbikani mwa Mlungu wanuyo, Nkana mdziko muli mabvutowo;
   Khristu ndiye thanthwe lolimbalo, Ndi la mphamvu zonsezo.

   CHORUS:
   Tilimbike kuima pa thanthwe lija, Thanthwe ndilo Khristuyo;
   Ngati tipiriratu tidzankako, Kuli mpando wa Mlunguyo.

2. Limbikani ndi mtima woti nji, Inde mwa chikhulupirirocho;
   Khristu ndiye thanthwe la mphamvulo, Agonjetsa tchimolo.

3. Limbikani mwa choonadicho, Chikuthangatani koposatu;
   Khrustu ndiye thanthwe lopumamo, mmene bvuto latha phe.

No. 39
THANTHWE , LOLIMBA
Wm. B. Bradbury
Doh is G.

1. Chiyembekezo changatu, chiri mwa Yesu Woyera;
   Sindikhulupira wina Koma dzina la Yesuyo.

   CHORUS:
   Ndaima pa Khristu thanthwe Nthaka yonse ndiyo mchenga.
   Nthaka yonse ndiyo mchenga.

2. Pondiphimba ine mdima, Ndipumula mwa Iyeyo.
   M’namondwe ndi m’mphepo zonse Ndithawira kwa Iyeyo.

3. Pangano Lake ndi mwazi, zinditchinjiriza ine;
   Ndikalepheratu pena, Ndidzakhalatu mwa Iye.

4. Pamene Iye adzadza, Ndidzapezeke mwa Iye;
   Ndiri m’chilungamo Chake, Wopanda naye chifukwa.

No. 40
POYENDA NDI MBUYE
D. B. Towner, by Per.
Doh is F

1. Poyenda ndi Mbuye mkuwala kwakeko, Aunikira m'njira mwathu;
   Pakugwira ntchito amakhala nafe, Ndi onse amene amvera.

   CHORUS:
   Khulupira, palibenso njira yakukondwa mwa yesu,
   Komatu kumvera.

2. Mthuzi sungagwetu, pena mtambo mmwamba Komatu azipirikitsa;
   Nkhawa ndi chisoni zidzachoka ngati Tikhulupira ndi kumvera.

3. Chifukwa cha ntchito ndi zisoni zathu, Adzatilipira mokwana;
   Kopandanso imfa, kapena kukwiya, Tidzadalitsika pomvera.

4. Sitingadziwetu zachikondi chake, Mpaka titadziperekatu;
   Chifukwa chifundo ndi chimwemwe Chake Amapatsa anthu omvera.

5. Pompo mchiyanjano tidzakhala naye, Kapena kuyenda ndi Iye;
   Ndipo tidzachita chifuniro Chake, Tidzakhala omvera ndithu.

No. 41

## MULUNGU AKHALE NDI INU

W.G. Tomer

Doh is D flat

1. Mulungu akhale ndi inu; Mpaka tidzaonananso,
   Atsogoze, asunge ‘nu; Mulungu akhale ndi inu.

   CHORUS:
   Asunga nonsenu, Tikomana ndi Yesu,
   Asunga nonsenu, Mulungu akhale ndi inu.

2. Mulungu akhale ndi inu; Ndi mapiko akubisa,
   Masiku onse kudyetsa; Mulungu akhale ndi inu.

3. Mulungu akhale ndi inu; Ndi pamene mubvutika,
   Adzakuthangatani ‘nu; Mulungu akhale ndi inu.

4. Mulungu akhale ndi inu; Ndi chikondi Chake chonse,
   Asunge m’zoopsya zonse; Mulungu akhale ndi inu.

No. 42
SITIDZALEKANANSO
J.H TENNEY
Doh is B flat.

1. Tikakhala ndi abwenzitu, Mdziko lathu lino,
   Posachedwa timalekana Nawo mwa chisoni.

   CHORUS:
   Sitidzalekana m'mwamba, sitidzalekana,
   M'dziko lokometsetsalo Sitidzalekana.

2. Timakhala ndi ch'yembekezo, Pakufa anzathu;
   Kuti pakutha dziko lino, Tidzakhala nao.

3. Sitidzalekananso ai, M'dziko lokomalo,
   Nyimbo za chimwemwe, mtendere, 'Dzayimba kosatha.

No. 43

# WOGONA MWA AMBUYE

W. B. Bradbury

Doh is D

1. Wogona mwa Ambuyeyo,
   Podzuka sadzaliranso.
   Mpumulo wa mtenderetu,
   Wosaletseka ndi mdani.

2. Wogona mwa Ambuyeyo,
   Wopanda mantha ndi ‘mfayo.
   Chodala ch’yembekezocho
   Cha moyo wa kumwambako.

3. Wogona mwa Ambuyeyo,
   Akhala mu mtenderewo;
   Chisoni chonse chatha phe!
   Pobwera ‘Ye adzauka.

4. Wogona mwa Ambuyeyo,
   Adzamvatu lipengalo;
   Adzadzutsidwa m’mandamo,
   Kupita kwa Ambuyeyo.

No. 44

NDIDZAMDZIWA MOMBOLO WANGA

John R. Sweney

Doh is A flat

1. Pamene nditatha zintchito zanga zonsezo,
   Nditaoloka pa tsidya la Nyanja;
   Chakufachi chikadzabvalatu chosafanso;
   Pompo ndidzamdziwa Mombolo wanga.

   CHORUS:
   Ndidzamdziwa, ndidzamdziwa, Podzaima pa mbali pakepo,
   Ndidzamdziwa, ndidzamdziwa, Ndi misomali m’manja Mwake.

2. Moyo wanga udzakondwera pakumuona,
   Ndi kuona nkhope yake yowala;
   Ndidzamyamika Iye ndi mtima wanga wonse,
   Malo adandikonzera kumwamba.

3. Ee! Ndidzakondwa pakuona okondedwawo
   Omwe ndalekana nawo m’dzikoli;
   Koma n’dzayamba ndaonana naye Yesuyo,
   Wokondwdwa wanga wopambanayo.

4. Kupyolera pa zipata kunka ku mzindawo,
   Iye adzanditsogolera ine,
   Nyimbo ya nthawi zonse ndidzayimba mokondwa;
   Nditamuona Mpulumutsi wanga.

No. 45
PATSENI BAIBULO
E. S. Lopenz
Doh is A flat

1. Patseni Baibulo ndilo ndikufuna, Ndi chotitsogolera njirayo;
   Monga mapiri oonetsa kwathu, Obweza anthu osocherawo.

   CHORUS:
   Patseni Baibulo ndilo mau Ake, Mau oyera a Mulunguyo,
   Ndilo pangano la chikondi Chake, Ndi nyali m’njira yonka mmwambamo.

2. Patseni Baibulo ndil ndikufuna, Mmene usweka mtima wangawo;
   Patseni Mau a Ambuye Yesu, Mau okondweretsa mmtimanga.

3. Patseni Baibulo ndilo ndikufuna, Nyali ya kusonyeza njirayo,
   Mmene ndingagwe lindipulumutsa, Lindisonyeza tchimo langalo.

4. Patseni Baibulo ndilo ndikufuna, Liunikira a mu mdimawo,
   Ndilo chiyembekezo kwa olira, Ndi nyali mnjira yonka mmwambamo.

No. 46

YIMBIRANSO KWA INE

P.P Bliss

Doh is G

1. Yimbiranso kwa inetu, Mau a Moyowo;
   Ndionenso za iwotu, Mau a moyowo.
   Mau abwinowo, Andiphunzitsatu,

   CHORUS:
   Mau Ake ozizwitsa, Mau a moyowo
   Mau Ake, abwinowo, Mau a moyowo.

2. Khristu apatsa onsewo, Mau a moyowo;
   Wochimwa ‘we akwitana, Mau a moyowo.
   Angoperekatu kuti tinke mmwamba,

3. Uitana uthengawo, Mau a moyowo;
   Adzakhulululukira ‘we, Mau a moyowo.
   Yesu  Mpulumutsi Ayeretsa iwe.

No. 47
NDAIMIRIRA PA GOMBE
T.C O'kane
Doh is G

1. Ndaimirira pa gombe, ndiyang'anitsitsa
   Ku Kanani wabwinoyo, Komwe ndidzalowa.

   CHORUS:
   Tidzapumula mdziko lokondwa (lokondwa)
   Kuoloka pa gombe lija (lowala)
   Tidzaimba nyimbo ya Mose,
   Ndikukhala ndi Yesu nthawi zonse.

2. Pa madambo akuruwo 'Dzawala tsikulo,
   Khristu adzalamulira, Nadzachotsa mdima.

3. Ndidzafika uko liti, Ndikudalitsidwa,
   N'dzamona liti Atate, Kuti ndikapume?

4. Moyo wanga ukondwera , Kusiya dzikoli;
   Nkana namondwe aombe, Sindiopa konse.

No. 48

CHIMWEMWE POSACHEDWA

F. E Belden

Doh is C

1. Chimwemwe podzatha nthcitoyi, Podzasonkhana okunkha,
   Alikudza ndi zipatso, Ku Yerusalemuko.

   CHORUS:
   Kudzakhala chimwemwedi,
   Chimwemwe cha nthawi zonse,
   Chifukwa nthawi yafika,
   Yosonkhana okunkha.

   Bass and Tenor :

   Chimwemwe posachedwa,
   Chimwemwe cha muyaya,
   Chifukwatu nthawi yafika, Yosonkhana okunkha.

2. Tidzayimba nyimbo zabwino, Tidzayamika mokondwa,
   Tidzatama Khristu Mfumu, Mu mzinda watsopano.

3. Chimwemwe chitidikirako, Ku malo a chikhuduwo;
   Yesu ali kuwakonza, Mu Mzinda watsopano.

No. 49

GANIZO LOKOMA

Phillip Phillips

Doh is B flat

1. Ganizo lokoma, Limadza m'mtimamu;
   Ndiri  pafupi ndi kwathu, Koposa kalelo.

   CHORUS:
   Pafupitu, Ndi kwathuko;
   Ndiri pafupi ndi kwathu Koposa kalelo.

2. Kufupi ndi Tate, Komwe kuli malo;
   Ku mpando wa Yesu Mbuye Ku Nyanja yoyera.

3. Ndiri kupitatu, Nditula katundu;
   Ndisiya mtanda wangawo, Kubvala korona.

No. 50
BWINOLI TIPITA
J. P Webster
Doh is G

1. Kuli dziko labwino m'mwamba,
   Lakuwala koposa dzuwa,
   Ndi Atate akonza malo,
   Pokhalira ife komweko.

   CHORUS:
   Bwinoli tipita,
   Tikomana ku dziko lija (lijalo).

2. Tidzayimba komweko nyimbo,
   Za abwino omvera Yesu.
   Sitidzamvatu zisoninso,
   Tidzakondwa masiku onse.

3. Tidzatama Atate wathu,
   Kuti Iye 'napatsa Yesu,
   Kuchotsera zochimwa zonse,
   Ndi kutidalitsira ife.

No. 51
MUTIBATIZENSO
W.A Ogden , by per
Doh is A flat.

1. Mutibatize ndi mphamvu Yanu,
   Mutitsitsimutse mwa nsoni Zanu.

   CHORUS:
   Tikupemphani Mbuye wathu Yesu,
   Mutibatizetu ndi Mzimu wanu.

2. Osayenera ndi ochimwa'fe,
   Mutitsuke ife m'zoipa zathu.

3. Tifuna nkhunda ya m'mwamba idze
   Idzatidalitse mwa nsoni Zanu.

4. Imvani mau ochoka m'mwamba,
   Ndiwe Mwana wanga wokondedwayo.

   CHORUS: (wotsiriza):
   Tigwadira Inu Mwana wa NKhosa,
   Tikupembedzani kosatha, Amen.

No. 52
KASUPE WA MADALITSO
Nettleton
Doh is E flat

1. Idzani ndi madalitso, Mtima wanga uyimbe;
   Nsisi zanu zisaleke, Kuti tiyamike’Nu,
   Phunzitseni kumvera’ Nu, Kuti ndikudziweni,
   Pamene chiyembekezo chidzaza mtima wanga.

2. Ndinutu thandizo langa, Mwandifikitsa pano,
   Ndipo mwa chifundo Chanu Ndikafika kwathuko,
   Anandifuna Yesuyo, Posochera mtarimo;
   Anakhetsa mwazi Wake Kundiombola ine.

3. M’ndipatse chisomo chanu, Pakuti ndi chisowa!
   Mundikokere kwa Inu Ndi chikondi chanucho.
   Sindifuna kusochera, Kukusiyani Inu,
   Tengani mtima wangawu;ukhale wanu konse.

No. 53

MZIMU NDI MTSOGOZIYO

M. M Wells

Doh is G

1. Mzimu ndi mtsogoziyo M’njira ya Chikhristuyo,
   Mtitsogoze ndinutu, Pa ulendo wathuwu.
   Myoyo ikondweratu, Pomva mau Akewo;
   Pakunena mzimuwo, “Osochera, bwerani.”

2. Bwenzi lathu ndinutu, Mkhale mfupi nafetu,
   Msatisiye tokhafe, Pakuyenda mmdimamu.
   Pakuomba mphepozo, Timaopa mtimamo,
   Tsono timva mauwo, “Osochera, bwerani.”

3. Mmene ntchito yathatu, mmene tidikira ‘Nu,
   Pakukhumba mmwambamo, Tsono tipempherabe,
   Nthawi ya mabvutowo Tikhulupirira ‘ Nu,
   Tsono timva mauwo, “Osochera, bwerani.”

No. 54

## NDIFUNA INU, MBUYANGA

Fred H. Byshe

Doh is B flat

1. Ndifuna Inu, Mbuyanga, Chifukwa ndagwa mthopemo,
   Ndi madzi pena motowo, Mnditsuke ‘ne, mndtitsuke ‘ne.

   CHORUS:
   Mnditsuke ‘ne mu mtimamo, Ndi madzi pena motowo.
   Mnditsuke ‘ne machimowo, Achoketu mu mtimanga.

2. Mukatsegula masowa, Ndidzakuyamikani ‘Nu.
   Komabe mtima woyera Udzapambana zonsezo.

3. Ukatsukidwa mtimawo Adzatseguka masowo.
   Chifukwa kuti mwa Inu, Ndionamo za mmwambamo.

4. Ndayesa kudzikonzatu, Kuchotsa tchimo langalo.
   Ngakhale ndayesetsatu, Zoipazo ziripobe.

No. 55

KODI MWALANDIRA YESU?

Rev, E A. Hoffman

Doh is A flat

1. Kodi mwalandira Yesu Mbuyeyo? Kodi mwasamba mmwazi Wake?
   Mwakhulupirira mwa chisomo ‘ke? Kodi mwasamba mmwazi Wake?

   CHORUS:
   Kodi mwasambamo, mmwazi  wabwino wa Yesuyo?
   Kodi mwayeretsa mtima wanuwo? Kodi mwasamba mmwazi Wake?

2. Kodi mukuyenda ndi Ambuyeyo? Kodi mwasamba mmwazi Wake?
   Mwapumula mwa Wopachikidwayo? Kodi mwasamba mmwazi Wake?

3. Kodi mwakonzeka pa kubwera ‘Ye? Kodi mwasamba mmwazi Wake?
   Kuti mukalowe m’malo abwino, Kodi mwasamba mmwazi Wake?

4. Tayanitu zakunyansa zanuzo, Kodi mwasamba mmwazi Wake?
   Wakuchotsa tchimo lanu lonselo, Kodi mwasamba mmwazi Wake?

No. 56

## AMBUYE, NDIRI KUDZA

Wm. J. Kirkpatrick

Doh is A

1. Ndasocherera kutari, Mbuye ndibwera;
   Ndayenda m'njira za mdima; Mbuye ndibwera.

   CHORUS:
   Ndidzako! Ndidzako! Ndiri kudzako!
   Ndi chifundo cha Mbuye; Ndiri kudzako.

2. Ndamwaza zaka zambiri, Mbuye ndibwera,
   Ndilapa ndithu machismo, Mbuye ndibwera.

3. Ndatopa nazo zoipa, Mbuye ndibwera,
   Ndimvera mau anuwo, Mbuye ndibwera.

4. Mtima wanga uwawadi, Mbuye ndibwera,
   Mundichiritsa Mbuy'anga; Mbuye ndibwera.

5. Ndisowa mwazi wanuwo,Mbuye ndibwera;
   Munditsuke ndiyere mbu, Mbuye ndibwera.

No. 57
YEMWE AFUNA
P.P. Bliss
Doh is D. joyfully

1. Yemwe alikumva! Pfuula mau:
   Tumizani mthenga mdziko monsemo;
   Lalikani mthenga kuli konseko:
   Yemwe afuna adze.

   CHORUS:
   Omwe afuna, omwe afuna
   Uza za chimwemwe m'dambo ndi m'phiri;
   Atate wokonda aitana'ke
   Omwe afuna adze.

2. Yemwe alikudza, asachedwe,
   Pakhomo patseguka,lowa msanga;
   Yesu ndiye njiratu yakuona
   Yemwe afuna adze.

3. Yemwe afunitsa za mtendere,
   Yemwe afunitsa adzakhalabe;
   Yemwe afunitsa moyo wosathat:
   Yemwe afuna adze.

No. 58

MUBVEKE MBUYEYO

Oliver Holden

Doh is G

1. Tamani mphamvu ya Yesu angelo agwade;
   Turutsanitu korona mubveke Mbuyeyo.
   Turutsanitu korona mubveke, Mbuyeyo

2. Inu osankhidwa Ake, Oomboledwa'nu,
   Tamani Mpulumutsiyo, mumbveke Mbuyeyo;
   Tamani Mpulumutsiyo mubveke Mbuyeyo.

3. Anthu onse ndi mitundu, Pa dziko linotu,
   Am'lemekeze Mfumuyo, mumbveke Mbuyeyo;
   Am'lemekeze Mfumuyo, mumbveke Mbuyeyo

4. Tifuna kuti komweko, Tikamgwadire' Ye;
   Tidzayimba kosaleka mumbveke Mbuyeyo
   Tidzayimba kosaleka mumbveke Mbuyeyo.

No. 59
YESU BWENZI MTIMANGA
Martyn
Doh is F

1. Yesu, Bwenzi mtimanga, Ndithawira kwanuko.
   Pakuuka madziwo, Pakuomba mphepoyo.
   Mundibisr Mbuyanga, Likaleka bvutolo,
   Mnditsogoze bwinotu, Mndilandire kwanuko.

2. Pobisala penai, Ndingokangamira 'Nu.
   Ndiri wosauka 'ne, Mbuye, msandisiyedi.
   Wothandiza wanga 'Nu , Ndikukhulupira 'Nu,
   Mu mapiko Anuwo Mundipfunde inedi.

3. Khristu, mukwaniradi, Mndikhutitse mmtimanga;
   Msangalatse ifetu, Obvutika tonsefe.
   Ine ndi woipadi ! Inu wakuyera mbu;
   Ine ndi wonyengadi, Woonadi Inutu.

4. Nsoni zanu ziinga Zakuipa zangazo.
   Mundisunge woti mbe, Ee! Ndi mwazi wanuwo,
   Pa chitsime chanucho Mundimwetse Inudi;
   Mmtima mwanga madziwo. Adzayendayendabe.

No. 60
YESU CHIMWEMWE CHATHU
Lowell Mason
Doh is A

1. Yesu chimwemwe chathucho, Chitsime ndinu cha moyo.
   Ku’nika kwa ‘nthu onsewo, Tibwera kwanu Mbuyathu.

2. Polawa mkate wa moyo Tilakalaka kudyanso.
   Pakumwa madzi a moyo Tikwanitsidwa ndi Inu.

3. Mtima ufuna Inuyo Kumene mtitumizako.
   Tidzakondwera ngatitu Tigwira Inu kolimba.

4. Yesu, mukhale nafetu; Musangalatse ifenso.
   Muchotse mdima wa tchimo, Muwale m’dziko lonseli.

No. 61

# INDE NDIFUNA KUMVATU

Jno. R  Sweney

Doh is A flat

1. Inde ndifuna kumvatu, Za chikondano Chakecho,
   Cha Yesu Mbuye wangayo, Zomwe anamva kalelo.

   CHORUS:
   E! Zina za Yesu, E! zina za Yesu,
   Inde, ndilira mmtimamo, Chipulumutso chakeko.

2. Zina za Yesu ndimvetu Kuti ndichite Zakezo,
   Mzimu Woyera mudzetu, Ndiphunzitseni zonsezo.

3. Yesu ndi mmau mwakemo, Inde ndicheza nayeyo,
   Liu ndimamva mbukhumo, Ndilo la Yesu Mbuyeyo.

4. Zina za Yesu mmwambamo, Ali pa mpando pakepo,
   Udze Ufumu Wakewo, Ndiyetu Mfumu ponsepo.

No. 62

## AMBUYANGA YESU, NDIKONDA INU

A.J  Gordon

Doh is F

1. Ambuyanga Yesu, Ndikonda Inu,
   Ndisiya zoipa chifukwa chanu;
   Ambuye wabwino ndi Mplumutsiyo;
   Ndikonda tsopano koposa kale.

2. Ndikonda chifukwa munakonda’ne
   Mnafera pa mtengo kuombola’ne;
   Mukhulululukira zoipa zonse;
   Ndikonda tsopano koposa kale.

3. Ndidzakukondani kosalekai,
   Ndidzakutamani masiku onse.
   Mpakatu ndidzafa ndidzanenabe,
   Ndikonda tsopano koposa kale.

4. Ku malo owala kumwamba komwe
   Ndidzakuongani, Ambuye Yesu;
   Ntabvala korona ndidzayimbabe.
   Ndikonda tsopano koposa kale.

No. 63

## NDINGAYERE BWANJI ‘NE?

Rev. Robert Lowry

Doh is G

1. Ndingayere bwanji ‘ne? mwazi wa Ambuye Yesu,
   Nch’ani chindichizanso? Mwazi wa Ambuye Yesu.

   CHORUS:
   Mtsinje wa mwaziwo, Undiyeretsanso;
   Sin’dziwa winanso, Mwazi wa Ambuye ndiwo.

2. Pakudetswa ndiona, Mwazi wa Ambuye Yesu.
   Pakuchimwa nditchula, Mwazi wa Ambuye Yesu.

3. Zina sizikwanatu, Mwazi wa Ambuye ndiwo.
   Ntchito zanga zichepa, Mwazi wa Ambuye ndiwo.

4. Ndimakhulupiradi, Mwazi wa Ambuye Yesu.
   Zolungama zangazi, Mwazi wa Ambuye Yesu.

5. Poyamika ndiyimba Mwazi wa Ambuye Yesu,
   Ndithokoza Mbuyanga, Mwazi wa Ambuye Yesu.

No. 64

# KODI WALEMEDWA M’MTIMA MWAKO?

E. S. LORENZ

Doh is B flat

1. Kodi walemedwa m’mtima mwako? Nena kwa Yesu, nena kwa Yesu
   Kodi uli kumva za chisoni? Nena kwa Yesu yekha.

   CHORUS:
   Nena kwa Yesu, nena kwa Yesu, Ndi bwenzi labwinotu.
   Ndiye bwenzi lopambana onse, Nena kwa Yesu yekha.

2. Kodi ukulira mwa chisoni? Nena kwa Yesu, nena kwa Yesu;
   Kodi tchimo lina labisika ? nena kwa Yesu yekha.

3. Kodi umaopa za chisoni? Nena kwa Yesu, nena kwa Yesu;
   Kodi ulikuda nkhawa m’mtima? Nena kwa Yesu yekha.

4. Kodi ukulingalira imfa? Nena kwa Yesu, nena kwa Yesu;
   Kodi ukulira kuti adze? Nena kwa Yesu yekha.

No. 65
N’KWABWINO KUKHULUPIRA
W.J. Kirkpatrick
Doh is A flat

1. N’kwabwino kukhulupira, M’mau Ake a Yesu;
   Kupuma m’malonjezo’ke, Ndimtama nthawi zonse.

   CHORUS:
   Ndikhulupira Yesu, Ndimtama nthawi zonse;
   Yesu ali wa chifundo, Ndimtama nthawi zonse.

2. N’kwabwino kukhulupira, Mwazi Wake wa Yesu;
   Kungomkhulupira Iye Adzatitsuka ife.

3. N’kwabwino kukhulupira, Kuti achotse tchimo;
   Nadzatipatsa’fe moyo, Chimwemwe ndi mtendere.

4. Ndikondwa kumdziwa Iye, Mpulumutsi wangayo;
   N’dziwa adzakhala nane, Mpaka chimariziro.

No. 66

## POYAMBAPO NDAKONDWADI

E. F Rimbault

Doh is G

1. Poyambapo ndakondwadi, Ntapeza Inu Mbuyetu,
   Ndiyimba nyimbo yomweyi, Kukondwa sindikhala du.

   CHORUS:
   Kalelo! Kalelo! Wandisambitsa mmtimamo;
   Wandiweruza lomwelo, Kupempha ndi kukondwako.
   Kalelo! Kalelo! Wandisambitsa mmtimamo.

2. Ndamuza ndimakhalatu Ku nyumba kwake komweko;
   Mnyamata Wake ndinetu, Ndampatsa mtima wonsewo.

3. Omwewo mapanganowo, Sitilekana ifetu.
   Ndamvera ine mauwo, Wandiloleza m’mtimamo.

4. Ndampatsa mtima wonsewo, Kupuma mwa Ambuyeyo;
   Ndikhala, osamlekai, Kuthawa ndi kumsiya ‘Ye.

No. 67
IDZANI NONSENU OKONDA YESU
Robert Lowry
Doh is G

1. Idzani nonsenu, Okonda Yesuyo,
   Tiyimbe nyimbo yabwino, Tiyimbe nyimbo yabwino,
   Ku mpando Wakewo, Ku mpando Wakewo.

   CHORUS:
   Tiyende (tu) pamodzi, Tiri kupita kumwamba;
   Akhristu tiri kupita (pita), Ku Zioni wanwinoyo.

2. Ngakhale enawo Aleke kwimbako,
   Akhristu ‘fe tidzayimba, Akhristu ‘ fe tidzayimba,
   Kumlemekezaye ‘Ye , Kumlemekazayo.

3. Akhristu tonsefe, Tikondwe m’dzikoli,
   Koposa anthu enawo, Koposa anthu enawo,
   Tisanafikeko, Tisanafikeko.

4. Tiyimbe mokondwa, Misonzi iume;
   Poyenda kunka kwathuko, Poyenda kunka kwathuko,
   Kwa Mlungu wathuyo, Kwa Mlungu wathuyo.

No. 68

NDIKONDA KUNENA NDAOMBOLEDWA

W. J. KIRKPATRICK, BY PER

Doh isA

1. Ndikonda kunena chifukwa, Ndaomboledwa ndi mwazi!
   Ndaomboledwa mwa chifundo, Ndine Wake nthawi zonse.

   CHORUS:
   Ndi mwazitu (ndi mwazitu) wa Yesu, ndaomboledwa;
   Ndine Wake (ndineWake) kosatha, ndaomboledwa.

2. Ndinetu wokondwa mwa Yesu, Kukondwa kosaneneka;
   Ndziwa kuti kuwala Kwake Kumakhalabe ndi ine.

3. Ndisinkha za Mombolo wanga, Tsiku lonse ndisinkha “ Ye;
   Ndiyimba wosakhala chete, Ndiyimba chikondi Chake.

4. Ndidziwa kuti ndzamuona, Mfumu amene ndimkonda;
   Yemwe amanditsogolera, Ndi kundisunga usiku.

5. Korona ali kudikira, Mmalo anga owalawo;
   Msanga ndi oyera mtimawo Ndidzakhala ndi Ambuye.

No. 69

TIDZAKHALITSA PA KASUPE

F.E Belden

Doh is E flat

1. Tidzakhalitsa pa kasupe, Wa madzi Akewo.
   Kumene Yesu adikira, Kupatsa moyowo.

   CHORUS:
   Tidzakhalitsa pa kasupe (wathu),
   'Dzakhalitsa pa kasupe (wathu)
   'Dzakhalitsa pa kasupe (wathu),
   Pali madzi a moyo.

2. Tikatopatu ndi ulendo, Tidzapumulatu,
   Pa mtsinje wopambana yonse, Wokondwakondwatu.

3. Idzani nonsenu kwa Khristu, Mudzamwe madziwo,
   Adzatimwetsa kwa ulere, Kasupe Wakeyo.

No. 70

TIDZAIMA BWANJI PA CHIWERUZO?

Jno. R. Sweney

Doh is F

1. Mmene Yesu adzasonkhatu, Mitundu yonse ya dziko,
   Kodi tidzaima bwanji' fe Pa mpando wachiweruzo?

   CHORUS:
   Adzasonkhanitsa tiriguyo, Koma mankhusu adzataya;
   Nanga tidzaima bwanji ko' Pa tsiku la chiweruzo?

2. Kodi tidzamva mau Ake, Wachita bwino iwetu,
   Kapena tidzanjenjemera, Tidzachotsedwa ku mpando?

3. Iye adzakondwera ndithu, Kuona oomboledwa,
   Adzawavekatu zovala, Pa kugwadira Mbuyeyo.

4. Tiyeni tidikire tsono, Ndi nyali zathu zowala,
   Poitana Mkwati ku phwando Tidzakhale okonzeka.

5. Tikakhala okonzekatu, Tikakhala opirira;
   Podzatha ulendo wathuwu, Tidzanka naye kumwamba.

No. 71

## KODI DZINA LANGA LALEMBEDWAMO?

Frank M. Davis

Doh is A flat.

1. Mbuye sindisamala kukhala wachuma;
   Ndifuna kukalowa m'dziko la kumwamba;
   M'bukhu lokometsetsa la ufumu wanu,
   Kodi lalembedwamo Mbuye dzina langa.

   CHORUS:
   Kodi dzina langa, Lalembedwa m'mwamba?
   M'bukhu la ufumuwo, Kodi lalembedwa?

2. Machismo anga alipo ambiri-mbiri,
   Koma mwazi wa Mpulumutsi wandikwana;
   Chifukwa lonjezano lanu liripobe,
   Ngakhale afire, Ndidzawayeretsa.

3. Ku mzinda wokoma wa malo owalawo,
   Ndi anthu obvala za ulemererozo;
   Kumene choipa sichidzaonongako,
   Kodi dzina langali liripo m'bukhumo?

No. 72
TIDZAIMA BWANJI PA CHIWERUZIRO?
F.E Belden
Doh is E flat

1. Chiweruziro ndithu chayambidwa, Mabukhu atsegulidwa;
   Ndipo ntchito iri yonseyo M'lungu adzaweruza.

   CHORUS:
   Kodi ife tidzatani pa tsiku lalikurulo?
   Kodi tidzafika kwa Iye machismo atatsukidwa?

2. Ayamba kuweruza akufa, Msanga aweruza a moyo,
   Mwa zolembedwa m'mabukhu, Adzaweruza onsewo.

3. Kodi tidzatani pa nthawiyo, Pobvumbulutsidwa machismo!
   Podzaweruzidwa mlandu Kodi tidzaloledwatu?

No. 73
POBWERA MFUMU
Rev. E. S. Lorenz
Doh is E flat

1. Taitanidwatu ku phwando, Kukhala nawo anthu Ake;
   Chidzaonekanji kwa ife Pobwera Mfumu?

   CHORUS:
   Pobwera Mfumu, m'bale Pobwera Mfumu!
   Chidzaonekanji kodi, Pobwera Mfumu.

2. Adzabvala korona Iye Amene anafera anthu;
   Tidzamuona bwino-bwino, Pobwera Mfumu.

3. Monga kung'anima kwa mphezi, Zobisika zidzaoneka
   Tidzadziwana wina mnzake, Pobwera Mfumu.

4. Adzaona anthu Akewo Atabvalatu zoyerazo;
   Tikapirira tidzakondwa Pobwera Mfumu.

5. Kulekana kwa nthawi zonse, Kulira kwa anthu ochimwa,
   Kudzakhala koopsya ndithu Pobwera Khristu.

6. Ambuye tilandirenitu, Tikhale pafupi nanutu,
   Kuti tisadzaope konse, Pobwera Inu.

No. 74
M’MAWA TIDZAFESA
George A. Minoc
Doh is C

1. M’mawa tidzafesa mbeu zakukoma,
   Msana ndi usiku tidzafesanso.
   Nyengo ya masika tidatema m’munda,
   Tidzabwera tonse ndi zipatsozo.

   CHORUS:
   Ndi zipatsozo,ndi zipatsozo
   Tidzabwera tonse ndi zipatsozo.

2. Tidzifesa m’dzuwa tidzifesa m’thuzi,
   Sitiopa  ife mtambo ndi mphepo
   Athatu masika ntchitozi zidzatha,
   Tidzabwera tonse ndi zipatsozo.

3. Tingolira kaya koma tidzafes
   Mbeu za Ambuye ntchito ya Yesu.
   Adzachotsa msozi adzatilandira,
   Tidzabwera tonse ndi zipatsozo.

No. 75
A! MBUSA WANGA NDIMVATU
W. A. Ogden
Doh is A flat

1. A! mbusa wanga ndimvatu, Uko ku chipululuko,
   Zilira nkhosa Zaketu, ziri kutari mkholamo.

   CHORUS:
   Bwezatu, bwezatu, Bweza zonse moopsyamo;
   Bwezatu, bwezatu, Bweza Zakezo kwa Yesu.

2. Ndani afuna kunkako, Kukazipeza nkhosazo?
   Ndani adzathandizyo, Kuti zifunde m’kholamo?

3. Etu! Zilira konseko, Ziri ku phiri ko’psyako,
   Imva, anena Mwiniyo, “Kweye, upeze nkhosazo.”

No. 76

## NDIKONDA KUUZABE

W. G. Fischer

Doh is A flat

1. Ndikonda  kuuzabe, nthano ya Yesu, ndi
   Zosaoneka zomwe, za m’mwamba zakezi;
   Ndikonda kuuzabe, za chikondi Chake,
   Kubukitsa mbiriyo ya Mwana wa Mlungu.

   CHORUS:
   Ndikonda kuuzabe, za Yesu mwini wanga,
   Za chifundo Chakecho, Ndiyimbe kumwamba.

2. Ndikonda kuuzabe, nthano yozizwitsa
   Chifukwa ipambana, zonse zina ndamva;
   Ndikonda kuuzabe, zomwe achitira
   Kwa ine ndi kwa onse, a m’mvera ndi mtima.

3. Ndikonda kuuzabe, nthano yokomayo
   Nthawi zonse ndiyimva, ndisekereranso.
   Ndifuna kuuzabe kumvetsa amene
   Sanamve za Mulungu, Wopulumutsayo.

4. Ndikonda kuuzabe, Mpulumutsi wanga
   Natsika kumwambako natifera dala
   Nakweranso kwawoko nadzadzanso Iye,
   Kusonkhanitsa Ake , Naye kukhalabe.

No. 77

KUFUNAFUNA OTAIKAWO

W. A. Ogden

Doh is B flat ( beating 3 to measure)

1. Kufunatu E! ndi mtima wonse,
   Kufuna akusocherawo;
   Lalika kuti Yesu anati,
   Idzani nonse kwa Inetu.

   CHORUS:
   Pitanitu (inde) konse konseko,
   Mukabwere ndi (anthu) osochera;
   M'khola Lake la (Yesu) Mpulumutsi,
   Nafera 'Ye anthu (E) ochimwa.

2. Kufunatu ndi kutsogolera,
   Anthu ofoka'wo kwa Yesu
   Kutsogolera njira yabwino,
   Yonka ku moyotu wosatha.

3. Tidzitero ponka kulalika,
   Kutsata Yesu tsiku n'tsiku;
   Ndi kuthangata ofoka onse,
   Kuwatsogolera kwa Yesu.

No. 78

## PULUMUTSA OMWE ALI KUFA

W. H. Doane

Doh is B flat

1. Pulumutsa omwe ali kufatu,
   Uwachotse m’manda a uchimo;
   Lilira ochimwa, nuwadzutsetu,
   Nuwauze za Yesu Mbuyeyo.

   CHORUS:
   Pulumutsa omwe ali kufatu
   Yesu wachifundo alanditsa.

2. Ngakhale amkana, Iye alinda,
   Afuna kulandira olapa.
   Awapembedzera moona mtima,
   Adzawakhulukira iwo.

3. Mu mtima mwa munthu muli zambiri,
   Koma Yesu azichotsa zonse;
   Atakhudzidwa ndi chikondi Chake,
   Nsinga za Satana zidzaduka.

4. Pulumutsa omwe ali kufatu
   Limbitsa otodwa ndi olema;
   Kwabwezera m’njira yopapatiza,
   Ndi kuwauza za Mpulumutsi.

No. 79

KUFUNA ANTCHITO

J. B. O. Clemm

Doh is A flat

1. Mindatu yayera kale
   Dzinthu zonse zachanso;
   Pafupi ndi kutariko
   M'dziko lonse lapansi.

   CHORUS:
   Mbuye tikupempha Inu,
   Kokosani antchito;
   Atumizeni msangatu,
   Nthawi isanathei.

2. Atumizeni m'mawatu,
   Ndi nthawi ya usana
   Ngakhale dzuwa lilowa,
   Agwirebe ntchitoyo.

3. Ndipo inu otumidwa,
   Gwiranitu ntchito yo;
   Ndipo potsiriza ntchito
   Mudzadza ndi chimwemwe.

No. 80
TINKE IFE KU NTCHITO YA MULUNGU
W. H. Doane
Doh is F

1. Tinke ku ntchito ya Mlungu wathu;
   Tidzitsata mapazi a Mbuye Yesu.
   Mau Ake adzapatsa mphamvu Yake,
   Ndipo ndi mtima wonse tigwire ntchito.

   CHORUS:
   Gwirani ntchitoyo, Gwirani ntchitoyo,
   Mpakatu Yesuyo, Adzabweranso mdzikoli.

2. Tinke ife ku ntchito ya Mlungu wathu,
   Yakudyetsa, kumwetsa osowa onse.
   Ndi mbendela ya mtanda tidzayendatu,
   Pakulalika Chipulumutso Chake.

3. Tinke ife ku ntchito ya Mlungu wathu,
   Ntchito ya kuchenjeza iripo lero;
   Ndi kwa anthu a m’dima a mdziko lino,
   Ndi kukweza Ambuye ndi Mfumu yathu.

4. Tichitebe zintchito za Mlungu wathu,
   Posachedwa Ambuye adzabweranso;
   Ndipo ife tidzanka kumwamba naye,
   Nyimbo zathu zokoma tidzayimbabe.

No. 81

# GWIRA ZINTCHITO ZAKE

Lowell Mason

Doh is F

1. Gwira zintchito Zake, Mdima ukudzatu,
   Yamba mmamawa ndithu, Kuli kuchatu.
   Gwiranso msana monse, Mpaka madzulowo.
   Gwira, usiku udza, Posachedwatu.

2. Gwira zintchito Zake, Mdima ukudzatu,
   Gwira masana onse, Kusanadei
   Udzapumula bwino, Potha zintchitozo,
   Gwira, usiku udza, Posachedwatu.

3. Mkhristu gwiratu ntchito, Mdima ukudzatu,
   Dzuwa lapita kale, Msanga kuda bi!
   Gwira madzulodzulo, Usanagonetu,
   Msanga zintchito zonse Tere zithatu.

No. 82
M’MAWA
Aaron Williams
Doh is F

1. M’dzamva mau anga m’mawa
   Mbuye popemphera;
   Ndidzayang’ana kwa Inu
   M’mene ndipemphera.

2. Mzimu anditsogolere
   M’njira zolungama!
   Andisonyeze njira za
   Ntchito zanga zonse.

3. Anthu okonda dzinalo,
   Adzakwanitsidwa;
   Mulungu adzawaphimba
   Ndi chikopa Chake.

No. 83
ANTHU AMBIRI AYIMBA
R.E Hudson
Doh is A

1. Anthu ambiri ayimba, Lodala dzina la Mbuye!
   Ulemerero kwa Mlungu, Lodala dzina la Mbuye.

   CHORUS:
   Dzina lodala, dzina lodala, dzina la Ambuye Yesu.
   Dzina lodala,dzina lodala, dzina la Ambuye Yesu.

2. Dzinali lichotsa mantha, Lodala dzina la Mbuye!
   Liri nyimbo ya ochimwa, Lodala dzina la Mbuye.

3. Athyola mphamvu ya tchimo, Lodala dzina la Mbuye!
   Mwazi Wake utitsuka, Lodala dzina la Mbuye.

No. 84
YEHOVA TILEMEKEZA
Guillauwe Fraus
Doh is G

1. Yehova tilemekeza, Ndi Mwana ‘ke wokondedwa;
   Titama Mzimu Woyera: Mulungu Wodalitsidwa. Amen.

No. 85

## NDIYIMBA MPHAMVU YA MULUNGU

Arr. F. Root

Doh is E flat

1. Ndiyimba mphamvu ya Mlungu, wolenga mapiri,
   Yemwe anapanga zinyanja ndi mlengalenga;
   Ndiyimba nzeru imene inapanga dzuwa;
   Mwezi uwala usiku, ndi nyenyezi zomwe.

2. Ndiyimba ubwino Wake, Wakupatsa kudya;
   Analenga zonse ndi mau, nayamikira.
   Mbuye munazikhazika mozizwitsa ndithu!
   Zinthu za m’dziko lapansi Ndi zam’mwamba zomwe.

3. Mbeu ndi maluwa omwe, zidziwitsa Inu;
   Mitambo yonse ndi namondwe, zimvera Inu.
   Za moyo zonse zimasamalidwa ndi Inu.
   Tiribe kothawira’ko, koma Kwanu kokha.

No. 86
GWADANI PA MASO PA MFUMU
F.J Haydn
Doh is A.

1. Gwadani pa maso pa Mfumuyo,
   Yimbani chikondi cha Mbuyeyo;
   Iyeyo n'chikopa, mtetezi wathu,
   Amene akhala kumwamba komwe.

2. Yimbani za mphamvu ya Mlunguyo
   Ndi za nsisi Zake kwa ifetu;
   Amakhala m'mphezi ndi m'bingu momwe,
   Ambuye abvala zoyeratu mbu.

3. Chikondi Chake ndi chakuyatu,
   Chimaonekera mu dzuwalo;
   M'mitsinje, m'mapiri, m'madambo momwe,
   Mu mvula, mu mame, ndi m'zina zonse.

4. Ndifetu opanda mphamvu konse,
   Tithemba pa Inu, Mbuyathuyo;
   Mwa nsisi za Inu mtisunge ife;
   Mtetezi ndi Mlengi ndi Bwenzi lathu.

No. 87
TATE TIKUDZA KWA INU
W.J Bostwick
Doh is F

1. Tate tikudzatu, Kwa Inu, Mbuyathu, Ngaka yolimbayo, Tipempha 'fe Dziko ndi la mdima Mmene mulibe 'Nu, Mtisangalatse 'fe, 'Tate wathu.

   CHORUS:
   Tate tibweratu kwa Inuko, 'Mvani popempha 'fe, Tate wathu.

2. Mtipulumutse 'fe Kwa mdani wathuyo, Mutithangate 'fe Mu bvutoli; Ndife ofo'katu, Limbikikitsani 'fe, ndi mphamvu yanuyo, Tate wathu.

3. Tipempha nsisizo Kuti tikhaletu Mu njira Yanuyo, Tate wathu. Mtitsogolere'fe Mpaka mudzabwera, Ndipo tidzapuma kwa Inuko.

No. 88

MSANDIPITIRIRE YESU

W.H. Doane

Doh is A flat

1. msandipitirire Yesu, Ndikupemphani.
   muli kudalitsa ena, Mndidalitse ‘ne.

   CHORUS:
   Yesu, Mbuye, Mundimveretu.
   Mmene muitana ena, Msandilekatu.

2. Ndigwadira Inu, Yesu, Musandikane;
   Ndikalapatu machismo, Ndidzachita mwayi.

3. Nkhope yanu ndifunitsa, Sindiyenera;
   Mtima wanga muchiritsa, Mthenda zangazi.

4. Yesu ndinutu chitsime, Cha chimwemwecho;
   Sindifuna wina konse, Koma Inutu.

No. 89
ZOKOMA NDITHU NTHAWIZI
W. B. BRADBURY
Doh is D

1. Zokoma ndithu nthawizi, Zakupemphera kwanuko,
   Ku mpando wa chifumuwo, Ndiuza zanga zonzezo;
   Pakundibvuta m’mtimanga, Ndimamuuza Yesuyo,
   Pakundiyesa mdaniyo, Ndinena kwa Ambuyeyo.

2. Zokoma ndithu nthawizi, Zopempha kwa Mulunguyo,
   Kwa Yemwe ali wo’natu, Kwa Iye wodalitsa ‘fe.
   Ndilakakalaka Iyeyu, Amene ‘nandiferatu,
   Posautsika m’dzikoli, Ndipempha m’dzina la Yesu.

3. Zokoma etu nthawizi, Za kupemphera Mbuyeyo;
   Zimandisangalatsa ‘ne, M’mabvuto anga onsewo;
   Ndilakalaka mphotho ya Kumwambamwamba komweko,
   Ndigwira mosalekatu Pakupemphera kwanuko.

No. 90
LINDA NDI KUPEMPHERA
R. Lowry
Doh is F.

1. Dikirani lero nthawi iri kutha;
   Mungagwe m’zoipa linda ndi pemphero;
   Thupi ndi lofoka mdaniyo ngwa mphamvu;
   Dikirani nonse mkwati ali kudza.

   CHORUS:
   Linda pempha, linda pempha;
   Usiku ndi usana dikirani ndi kupemphera.

   (Tenor and Bass)

   Linda pempha, linda pempha;
   Linda pempha, linda pempha;
   Usiku ndi usana dikirani ndi kupemphera.

2. Dzukani m’sagone musamakaika;
   Mudzalandiratu mpumulo kumwamba;
   Linda ndi pemphero, Mpulumutsi wanu,
   Anasautsidwa chifukwa cha inu.

3. Khulupira Yesu mdani ali pompo
   Bvala zida zako mpaka Mbuye adze.
   Musachedwe konse lero ndi labwino,
   Dikirani nonse ndi kupempheranso.

No. 91

## NTCHITO YA PA MLUNGU YATHA.

L. MASON

Doh is B flat.

1. Ntchito ya pa mlungu yatha,
   Sabata lina layamba;
   Moyo wangawe pumula,
   Mlungu wadalitsa lero.

2. Idza yamika Ambuye,
   Yemwe apatsa mpumulo;
   Timadalitsidwa lero,
   Koposa masiku ena.

3. Mayamiko athu m’mwamba,
   Akweratu monga nsembe;
   Kuti Khristu atipatse
   Dalitso m’mitima yathu.

4. Mpumulowu uli ngati
   Fanizo la wakumwamba,
   Komwe mpingo udzapuma,
   Zitatha zowawa zonse.

No. 92
SABATA NLA KUPUMA
German
Doh is F

1. Sabata nla kupuma, Ndi la chimwemwecho,
   Ndi tsiku lotonthoza, Lokometsetsatu;
   Akuru ndi ang'ono, Tigwade tonsefe,
   Tiyimbe kwa Woyera Wa nthawi zonsezo.

2. Sabata liri ngati Chochinjiriza 'fe,
   Ndi monga ngati munda Wotupa mdambomo;
   Litsitsimutsa m'yoyo Ya akutopawo,
   Popuma pa Sabata Tiona mmwambamo.

3. Ndi tsiku lakusinkha, Ndi la chikondicho,
   Lakuyanjana nazo Za mmwambamwambamo;
   Tipeze zakukoma Zoposa zinazo,
   Tifuna kupuma Kosatha mmwambamo.

No. 93
MSAIWALE TSIKU LA MBUYE
Wm. B. Bradbury
Doh is C

1. Msaiwale tsiku la Mbuye wathuyo.
   Ndi tsiku lopambana masiku enawo;
   Ndi tsiku lakupuma ndi la chimwemwecho,
   Kuwala kwake kuli kuchoka mmwambamo.

   CHORUS:
   Tikondwera kudza kwa Sabata Lakelo.
   Tikondwera kudza kwa Sabata Lakelo.

2. Sunga tsiku Lake lopatulikalo,
   Pembedza mwini njira yakunka mmwambamo;
   Tikamtsatira Iye pa dziko linotu,
   Adzatipatsa madzi a moyo Wakewo.

3. Timyimbira Yesu pa tsiku lonseli,
   Ambuye ali Bwenzi la ana onsewo.
   Wokoma mtima ndinu, Mukhale nafetu,
   Munalonjeza kuti mudzadza mmtimamu.

No. 94
SKULU YA SABATA
W.H Doane
DOH IS A flat

1. Skulu ya Sabata ndithu, Yokondedwa ndine;
   Mtima wanga uikonda, Skulu ya Sabata.

   CHORUS:
   Skulu ya (bwino), Sabata (bwino),
   Skulu ya (bwino) Sabata (bwino).
   Mtima wanga uikonda, Skulu ya Sabata.

2. Ndi mmenemo mtima wanga, Uyamba kudziwa;
   Ndinayamba kuikonda, Skulu ya Sabata.

3. Yesu ndi mau okonda, Andiitanatu;
   Ndipo ndisankha yekhayo, M’skulu ya Sabata.

No. 95
MLUNGUWATISUNGA ‘FE
L mason
Doh is G.

1. Mlungu watisunga ‘fe Mpaka mlungu winawu;
   Tiyeni timpembedze ‘ Ye Tsiku lopumulali;
   Tiganize zinthu za Mau a Mulunguyo.
   Tiganize zinthu za Mau a Mulunguyo.

2. Pakufuna nsisizo, Zakudzera m’dzinalo,
   Mudze, Mbuye wathu ‘ Nu, Mukhulululukire ‘fe;
   Pakupuma mwanumo, Tikumbuka Inuyo.
   Pakupuma mwanumo, Tikumbuka Inuyo.

3. Pakulemekeza ‘Nu, Tikuyandikira ‘Nu;
   Tikuona mphamvuyo, Ndi ulemererowo.
   Mtithangate Mbuyathu Kudya phwando m’mwambamo.
   Mtithangate Mbuyathu Kudya phwando m’mwambamo.

4. Mbuye mugonjetsetu Tchimo la mu mtimanga,
   Kuti ndikagwiretu Ntchito zokondwetsa ‘Nu.
   Masabata onsewo Alingane momwemo,
   Masabata onsewo Alingane momwemo.

No. 96

IDZA TSIKU LOPUMA

Ignace Pleyel

Doh is G

1. Idza tsiku lopuma, Lopatsidwa ku dziko.
   Idza mmtima mwangamu, Monga nyali ya mmwamba.

2. Tsiku lokondweretsa, Likupita msangatu;
   Litisangalatsanso Mpaka ncthito idzatha.

3. Tsiku loyeretsetsa, Tsiku lakupemphera;
   Tsiku lakulandira madalitso anuwo.

4. Idza tsiku lopuma Ndi zimphamvu za mmwamba,
   Ndi kuyera kwanuko kudzw m’mtima mwangamu.

No. 97
TAMVA MAU OMWEWO
W.M J. Kirkpatrick
Doh is G

1. Tamva mau omwewo, Atitu Yesuyo;
   Mpulumutsi ndiyedi, Yesuyo, Yesuyo;
   Pita m’midzi monsemo, Dziko lonse limvetu,
   Pita iwe konseko, Mveratu Mbuyeyo.

2. Lalikani nanunso, Yesuyo, Yesuyo;
   Kwa ochimwa onsewo, Amve za Mbuyeyo.
   Lalikani m’zisimo, Ndi m’mapiri monsemo,
   Kuti onse amvetu, Yesuyo, Yesuyo.

3. Yimbadi za Iyeyo, Amvetu anthuwo;
   Kuti Yesu wafadi, Kalelo,kalelo.
   Atikonda ifetu, Natifera indedi.
   Kuchotsera tchimoli, Yesuyo, Yesuyo.

4. Bukutsani maunso, Konseko, konseko.
   Aitana anthuwo, Ponsepo, ponsepo.
   Kodi wina samvatu? Pitako, pitako’ we,
   Angofuna onsewo, Yesuyo, Yesuyo.

No. 98
MOMBOLO AKHALE NANE
R. SWENEY
Doh is E.

1. Mombolo akhale nane, Kwenda ndekha sinditha
   Akhale pafupi nane, An’gwire m’dzanja lake.

   CHORUS:
   Sindidzaopa nthenda (E! nthenda), Akanditsogolera (tsogoza);
   N’dzapita wosang’ung’udza, Kutsata mapazi’ke.

2. Chikhulupiro changachi, Chiri chofoka ndithu;
   Andilimbikitsa Iye, Ndi mau Ake okha.

3. Mombolo akhale nane, Nd’yende m’njira ya moyo;
   Kupyola mayeso onse, Ndikumenyana nkhondo.

4. Mombolo akhale nane, Kuti anditsogoze;
   Kufikira nditafika, Ku tsidya lina lija.

No. 99
POKUMBUKIRA MTANDAWO
E. S. Widdemen
Doh is F

1. Pokumbukira mtandawo Umene Mbuye nafapo,
   Zokoma za pa dzikoli Sizinga kanthu konse bi.

2. Onani mutu, manjanso, Mapazi ndi mu nthitimo.
   E! panalibe winayo Wondibvalira mingayo.

3. Chinkana ndinachimwatu, Anakhulukira 'ne.
   Ndisadzitame ndekhai, Nditame mtanda Wakewo.

4. Chinkana ndipereketu, Ee! Chuma chonse m'dzikomo,
   Sizingakwane konseyi, Ndingopereka mtimanga.

No. 100

BWENZI LATHU NDIYE YESU

C. C. Converse

Doh is F

1. Bwenzi lathu ndiye Yesu, Atikonda ifetu,
   Zifunsiro zathu zonse, Tipemphere Mbuyathu;
   Mtima phe tisowa tonse, Zitivuta chabeko,
   Kaamba sitimanka konse, Kumpemphera Mlunguyo.

2. Tiri nazo zotiyesa, Zitidetsa nkhawamu,
   Tisadandaule chabe, Timpemphere Mbuyathu;
   Kodi tikaona wina, Timkhulupiriramo?
   Yesu atidziwa bwino, Timpemphere yekhayo.

3. Kodi tikulema nazo, Zotiwawa m'mtimamo,
   Atipulumutsa Yesu, Timpemphere Iyeyu.
   Kodi akuthawa 'bale, Pempheratu bwenzilo
   Akusunga mkono mwake, Udzapumuliramo

No. 101
YESU ALIKUITANA
Geo. C. Stebbins
Doh is C

1. Yesu alikuitana iwe, Lero lomwe, lero lomwe;
   Bwanji unasochorera iwe, Kutari kutariko?

   CHORUS:
   Aitana lero lomwe; Yesu alikuitana iwe tsopano.

   Tenor and Bass:
   Aitana lero lomwe; Aitana lero lomwe;
   Yesu alikuitana lero, ‘itana iwe tsopano.

2. Yesu aitana wotopa ‘we, Lero lomwe, lero lomwe;
   Tula katundu wako pa Iye; Ndipo sadzakukana.

3. Yesu alikulindira iwe, Lero lomwe, lero lomwe;
   Idza ndi machismo ako onse; Idzatu usachedwe.

4. Yesu ali kudandaulira, Lero lomwe, lero lomwe;
   Okhulupira adzakondwera; Podzakomana naye.

No. 102
MLENDO ALI PA KHOMO
E. O. Excell
Doh is D flat

1. Mlendo ali pa khomo, Mlowetse ( Mlowetsenitu, Mlowetsenitu),
   Wadza kale kalelo, Mlowetse ( Mlowetsenitu, Mlowetsenitu).
   Mtsegulire msangatu, Wakuyerayerayo,
   Mwana wa Mulunguyo, Mlowetse ( Mlowetsenitu, Mlowetsenitu).

2. Utsegule mtimawo, Mlowetse (Mlowetsenitu, Mlowetsenitu).
   Ukachedwa ‘chokatu, Mlowetse (Mlowetsenitu, Mlowetsenitu).
   Ndiye bwenzi lakolo, ‘Dzakupulumutsa we;
   ‘Dzakusamaliranso, Mlowetse (Mlowetsenitu, Mlowetsenitu).

3. Imva mau Akewo, Mlowetse (Mlowetsenitu, Mlowetsenitu),
   Sankha Iye leroli, Mlowetse (Mlowetsenitu, Mlowetsenitu).
   Wangoima khomopo, ‘Dzakusangalatsa ‘we,
   Udzamlemekezatu, Mlowetse (Mlowetsenitu, Mlowetsenitu).

4. Mlendo wa kumwambayo, Mlowetse (Mlowetsenitu, Mlowetsenitu).
   ‘Dzakupatsa zonsezo, Mlowetse (Mlowetsenitu, Mlowetsenitu).
   ‘Dzakhulululukira ‘we, Ndipo potsirizapo
   ‘Dzakutenga mmwambamo, Mlowetse (Mlowetsenitu,
   Mlowetsenitu).

No. 103

ANADZA KWA YESU MKURU WINA

Geo. C. Stebbins

Doh is E Flat

1. Anadza kwa Yesu mkuru wina, Kufunsa za njira ya chip’lumutso;
   Nayankha momveka Ambuyathuyo, Mukabadwensotu.

   CHORUS:
   Mukabadwensotu, mukabadwensotu;
   Indetu ndinenadi kwa inuyo, Mukabadwensotu.

2. Nonsenu mverani mau ake Amene Ambuye nenena Kwa ‘ye,
   Msanyozetu mau a uthengawu, Mukabadwensotu.

3. Mufuna kulowa mmwamba kodi? Kuyimba pamodzi ndi odalawo?
   Mukafuna moyo wa nthawi zonse, Mukabadwensotu.

No. 104
MUNDIMVE, YESU
W.H DOANE
Doh is C.

1. Mundimve, Yesu, ndikuliratu, ‘Dzani kwa inetu.
   Mu mtimanga ndilakalaka ‘Nu, Yesu, idzanitu.

   CHORUS:
   Ndinasocheratu kutariko, Kutari ndi Atateyo.
   Tsopano, koma mndilandirenso, Yesu, idzanitu.

2. Ndiribe malo mokhaliramo, ‘dzani kwa inetu.
   Khalani nane m’mtima mwangamo, Yesu, idzanitu.

3. Njobvuta njira ndimayendamo. ‘Dzani kwa inetu.
   Ndione nkhope yanu, Mbuyanga, Yesu, idzanitu.

4. Wolapa mtima simunyozadi, ‘Dzani kwa inetu.
   Pemphero langa mumve lonseli, Yesu,idzanitu.

No. 105
YESU AP’LUMUTSA
Emma L. Morton
Doh is F.

1. Yesu aombola! nena konseko;
   Yesu aombola yemwe amvatu;
   Yesu aombola m’ng’anjo ya moto;
   Yesu aombola yemwe adzatu.

2. Yesu aombola ndi zoona ko?
   Kodi kuli mphamvu yop’lumutsa ‘ne?
   Tandiuzanitu, kodi Khristuyo
   Nkutha kumasula nsinga zangazo?

3. Yesu aombola! limba mtima ‘we,
   Gwira ntchito Yake, aombola ‘we;
   Usaope mdani, gwira Yesuyo,
   Usakaiketu, ima ndithu nji.

No. 106

## Tidzamangatu Pa Thanthwe

F.E Belden

Doh is A flat

1. Tidzamangatu pa thanthwelo, Pa thanthwe losatha Yesu;
   Tidzaima nji osagwanso, Pa nthawi ya namondwe.

   Chorus:

   Tidzamangatu (tidzamangatu),
   Mwa Mbuyathuyo (mwa Mbuyathuyo);
   Timanga pa thanthwe lolimbalo, Pa Yesu Khristiyo.

2. Alipo amanga pa mchenga, Pa chuma cha dziko lino;
   Ndi ena amanga mtchimolo, Zokoma za pa dziko.

3. Mangani pa thanthwe Khristiyo, maziko olimbalimba;
   Ndichotu chiyembekezero Cha chip'lumutso chathu.

No. 107

Nthano Ya Yesu Uzeni

Jno. R. Sweney

Doh is E flat.

1. Nthano ya Yesu Uzeni, Lemba mu mtimangamu;
   Nthano yodala uzeni, Nthano yoposa zonse.
   Nyimbo ya ‘ngelo uzeni, Nthawi yobadwa Yesu,
   Ulemerero kwa Mlungu, Ndipo mtendere pano.

   CHORUS:

   Nthano ya Yesu uzeni, Lemba mu mtimangamu,
   Nthano yodala uzeni, Nthano yoposa zonse.

2. Nena masiku ajawo, Mbuye nasala kudya,
   Anayesedwa koopsya, koma analakika.
   Za ntchito Yake uzeni, Ndi za zisoni Zake,
   Anazunzidwa kolimba, Mphawi wopanda kwao.

3. Za mtanda Wake uzeni; Ndi za zowawa Zake;
   Za manda Ake uzeni, Ndi za kuuka kwake.
   M’nthano ndiona chikondi, Cha Yesu, Mbuye wanga,
   Mmene ndiimva ndilira, Anaombola ine.

No.108.
Mbusa Wabwino Yesu
W.A Ogden
Doh is F

1. M’busa wabwino, Yesu, Ati idzanitu
   M’khola mulowe zonse, Malo alipodi.
   ‘Dzani akuru inu, Ndi anyamatanso,
   ‘Dzani, mulowe m’khola, M’njira ya choonadi.

   CHORUS:

   Akuitana mwa nsinsi Zake, Wakusochera ‘we, idza kwa ‘Ne;
   M’busa wabwino aima mwa phee! Kukulindiratu ‘we.

2. M’busa wabwino, Yesu, anakufera ‘we;
   Aitanabe lero, akusochera ‘nu.
   Kuli zoopsya kunja, Idza, atero ‘ye;
   ‘Dzani, mulowe m’khola, Malo opuma du.

3. Inu msachedwe konse, Kuli mimbuluyo,
   Iri kufuna nkhosa kuti iziphetu.
   M’busa wabwino, Yesu, Akuitanabe,
   ‘Dzani, mulowe m’khola, malo alipomu.

No. 109

Mmene Mbuye Adzayeza

F.E Belden

Doh is F.

1. Mmene Mbuye adzayeza, Zinthu za mu mtimamo;
   Koditu tidzapambana, Pena ‘dzalepheranso?

   CHORUS:

   Mbuye wayeza iwetu, Nuperewera;
   Ndi malamulo Akewo, Nuperewera.

2. Kodi ‘dzamva mau Ake Wachitadi bwino ‘we?
   Pena kumva akunena, Choka iwe wochimwa?

3. Kodi dzamva Mzimu Wake Nthawi isanathei?
   Pena tizengerezabe, Ndi kuonongekadi?

No. 110.
Odala Ali Akuchita
P.P Brass
Doh is A

1. Imva mau a Mpulumutsi, Mau owona a moyo;
   Wosasamalawe kumbukiratu, Odala ali akuchita.

   CHORUS:

   Odala ochita malamulo, Ndi malonjezano Ake;
   Kumvako sikungatipulumutse, Odala ndi akuchita.

2. Ngakhale timve malamulo, Ndi malonjezano Ake;
   Kumvako sikungatipulumutse, Odala ali kuchita.

3. Adzalowa mu mzinda uja, Opanda tchimo ndi imfa;
   Atayeretsedwa kwa nthawi zonse, Adzadya za mtengo wa moyo.

No. 111.

## Bwenzi Palibe Lofana Naye

Geo. C. Hugg

Doh is F

1. Bwenzi palibe loposa Yesu, palibe,palibe
   Wina palibe wochiza, nthenda, palibe, palibe.

   CHORUS:

   Yesu ‘dziwa zobvuta zathu, Atitsogoza konseko;
   Bwenzi palibe lofana Naye; palibe, palibe.

2. Bwenzi palibe, lofana naye, palibe, palibe
   Iye ngofatsa koposa onse, palibe, palibe.

3. Nthawi palibe amatisiya, palibe, palibe
   Akondweretsa mu mdima monse, palibe, palibe.

4. Iye samasiya munthu Wake, palibe, palibe
   Pena kukana wolapa konse, palibe, palibe.

5. Mphatso palibe yofana Yesu, palibe, palibe
   Iye satimana malo mmwamba? Palibe, palibe.

No. 112

Yang'ana Pa Mtanda Kwa Yesuyo

F.E Belden

Doh is E flat

1. Yang'ana pa mtanda kwa Yesuyo, Kuti upeze moyowop;
   Chuma cha m'dziko nchakuthatu, Chosatha tipeza pa mtandapo.

   CHORUS:

   Poyang'ana Yesuyo, Pakuona mtandawo,
   Tingapeze moyowo, Poyang'ana Yesuyo (E, Yesuyo).

2. Ambuye anandikondweratu, Mmene ndinayang'ana 'Ye;
   Pondifikira mayesowo, Pa mtandapo ndipeza mphamvuzo.

3. Ndidzayang'anabe pa mtandapo, Pokhulupira Yesuyo;
   Yemwe amakhulupira 'Ye Sadzagwa m'mayeso a m'dzikoli.

No. 113
YESU MOFATSA AITANA TONSE
W.L. Thompson
Doh is A flat

1. Yesu, mofatsa, aitana tonse, M'vanitu mau Ake,
Akugogoda pa khomo pa mtima, Alikulindira 'fe.

CHORUS
Idzani kwanu! Inu, otopa, idzani.
Yesu mokonda aitana nonse. Iwe, wochimwa, idza.

2. Yesu apempha kwa 'Tate kumwamba, Ka'mba ka iwe ndine.
Bwanji tikana zifundo Zakezo, kodi tichedweranji?

3. Nthawi ya nsinsi ipitatu msanga, Kwa iwe ndi inenso;
Mdima wa imfa ukudza msanganso, Kwa iwe ndi inenso.

4. Yesu napatsa chikondi chakecho Kwa iwe ndi inenso.
Nkana tachimwa akhulukira, Tchimo la iwe ndine.

No. 114
CHIPATA CHOCHINJIKACHO
S.J Vall
Doh is C

1. Chipata chochinjikacho Chionetsera cheza;
   Kuchokatu ku mtandawo, chikondi chioneka.

   CHORUS:

   Mwachinjikira ine ko, Chipata cha kumwambako?
   Ine, ine, Mwachinjikira ‘ne:

2. Chipata n’chauleretu kwa onse akufuna;
   Achuma, osaukanso, A mtundu uliwonse.

3. Pitanitu mtsogolomo, Chipata n’chosatseka;
   Landira mtanda wakewo, Mbonitu ya chikondi.

4. Pa tsidya tidzatulapo, mtandawo wa manyazi;
   ‘Dzavalatu koronayo, ‘Dzamkonda ‘Ye koposa

No. 115
SING’ANGA MKURU NDIYE YESU
Arr. J.H Stockten
Doh is E flat.

1. Sing’anga mkuru ndiye Yesu, Mwana wa Mulungu,
   Asangalatsa a chisoni, Ali wa chifundo.

   CHORUS:
   Dzina la Yesu ndi lokoma, Dzina la Yesu lipambana,
   Dzina Lake la Kukonda, Yesu, inde, Yesu.

2. Zoipa zakhululukidwa, Yesu amatero,
   Tiyende bwino m’njira Yake, Tilowemo lero.

3. Nditama nsembe ya Mulungu, Ndilandira Yesu;
   Ndikonda dzinalo labwino, Dzina lanu, Yesu.

4. Akuru inu mbwere nonse, Ana inu nomwe;
   Ambuye akuitana, Bvomerani nonse.

No. 116
MTIMA WALEMEDWA KO?
W. J Kirkpatrick, by per
Doh is D

1. Mtima walemedwa ko, Yesu alibe malo?
   Muli tchimo lokha ko, Yesu alibe malo?
   Iye wangoimatu, Agogoda mtimamo,
   Adandaulira ‘we, Kodi alibe malo?

2. Nthawiyo wataya ko, Sugwira ntchito Yake?
   Mphamvuzo watayanso, Sugwira ntchito Yake?
   Sunaleke tchimolo, Sunakope munthuyo?
   Sunabweze mlendoyo, Sugwira ntchito Yake?

3. Wangofuna dzikoli, Nthawi ya Yesu ‘libe?
   Ntchito Yake waleka, Nthawi ya Yesu ‘libe?
   Ungotsata dzikoli, Chuma ndi zoipazi,
   Kudzikondweretsa ‘we, Nthawi ya Yesu ‘libe?

4. Ee, masamba okhawo, Wamana Yesu mphatso?
   Mmanja mwako muli mbe, Wamana Yesu mphatso?
   Sunasunge kanthui, Sunagwire ntchitoyo?
   Sudzakondwa tsikulo, Pakuonatu Yesu

No. 117
NDINAMVA MAUWO
REV. L. Hartsough
Doh is E flat.

1. Ndinamva mauwo, Anditiitana ‘ne;
   Ndisambe m’mwazi wanuwo, Wodzera mtandamo.

   CHORUS:
   Ndiri kudzatu; Ndidza kwanuko!
   Munditsuke mtimamo, Ndi mwazi wanuwo.

2. Ndiribe mphamvuzo, Mundilimbitsa ‘ne;
   Mundiyeretsa konseko, Ndiyerayera mbu.

3. Atero ndaniyo? Ndi Yesu wabwino,
   Apatsa mvanu mtendere; Ndi mphamvu mtimamo.

4. Nditama mwaziwo! Nditama nsisizo,
   Nditama Yesu Mbuyeyo, Chiyero chathucho.

No. 118
ATI YESU MBUYEYO
John T. Grape, by per
Doh is E flat.

1. Ati yesu mbuyeyo Ofo’ka ndinutu,
   Mudikire, mpemphedi, Ndidzapatsa mphamvutu

   CHORUS
   Yesu wathadi za mangawatu,
   Inde ndinaipa bii, Watsuka ine mbu.

2. Mbuye ndimva leroli za mphavu zanuzi,
   Zokha zisandutsadi mtima wanga woti bii.

3. Ine kanthu ndiribe, kogula moyowu,
   Ndingotsuka mtimamo M’wazi wa Ambuye yesu ‘Nu.

4. Mmene ndizaimatu pa chiweruzopo,
   Podzapulumukatu, Ndidzamtama yesuyo.

No. 119
NDIONA MWAZI WAKEWO
Mrs. Jos F. Knapp, by per
Doh is E flat

1. Ndiona mwazi wakewo, kasupe wodzaza;
   Ambuye yesu. Mp'lumutsi, Aloza balalo.

   CHORUS:
   Ndiona mwazi wakewo, Unditsuka 'ne mtimamo!
   Nditama mbuye yesuyo, Ndiyere mtima mwangamo.

2. Ndibadwa mwa tsopano. Za kale zafanso;
   Ndikhala moyo mwa yesu, Ndisamba m'mwazi 'ke

3. Ndiyenda m'nyali ya m'mwamba, kupewa tchimolo;
   Ambuye yesu alowa. Mumtima mwangamo.

4. Chisomo chozizwitsatu kusamba mwaziwo;
   Ambuye wopachikwayo, Ndimdziwa yekhayo.

No. 120
ATATE, NDZIPEREKATU
Arranged
Doh is C

1. Atate, ndziperekatu, Palibe winanso.
   Popanda Inu, Mbuyanga, Ndidzanka kutiko?

   CHORUS:
   Ee! Ndikhulupirira ‘Ye, Wondifera ine.
   Anapereka mwazi ‘ke Kupulumutsa ‘ne.

2. Ndikhulupira Mwanayo, Ndifuna mphamvu ‘ke;
   Zoipa zanga zonsezo, Mzichotse Inutu.

3. Kwa Inu, Mbuye, mwini wa Chikhulupirocho,
   Mndipatse mphatso Yanuyo, Ndingafe m’mtimanga.

No. 121
NDIYIMBATU ZA YESU
F. E. Belden
Doh is B flat.

1. Ndi’ mbatu za Yesuyo, Yemwe anaconda ‘ne;
   Anachoka m’mwambamo, Anafa mtandapo.

   CHORUS:
   Ndi’mbatu za Yesuyo, Kuyamika kosatha;
   Nadza kundifera ‘ne, Ndi’mbabe chikondicho.

2. Yesu analira ‘ne Mu Getsemane kale;
   Napemphera inedi, Ndisanamdziwetu.

3. Anthu ndi angelowo Sangazindikiretu,
   M’mene tchimo langali Liyeretsedwadi.

4. Sinachite kanthu bi kulipira chikondi;
   Ndingopatsa mtimanga, Ndimkonda konseko.

No. 122
NDIDZE PAFUPI NDI INU
Mrs. C.H. Morris
Doh is D flat

1. Ndidze pafupi ndi Inutu, Yesu, Mombolo wopambana 'Nu;
   Inu mndisunge mmanja mwanu, Inu mndibise mu ngaka Yanu,
   Inu mndibise mu ngaka Yanu.

2. Ndidza pafupi ndekha ndekha, Kanthu ndiribe kopatsa Yesu;
   Mtima woipa ndipatsa 'Nu, Munditsuketu ndi mwazi wanu,
   Munditsuketu ndi mwazi wanu.

3. Ndidza pafupi, ndine wanu, Ine ndisiya zoipa zonse;
   Zonse zonyada za dzikoli, Koma mndipatse Ambuye Yesu,
   Koma mndipatse Ambuye Yesu.

4. Ndidza pafupi ndinu, Mbuye, Mpaka kumwamba ndidzalowatu;
   Nthawi zosatha n'dzakhalabe, Pafupifupi ndi Mp'lumutsiyo,
   Pafupifupi ndi Mp'lumutsiyo.

No. 123
DZINA LOPAMBANA MMWAMBA
W. A Ogden
Doh is F

1. Dzina lopambana m'mwamba, Ndi pa dziko lonselo,
   Lomwe Tate anamutcha Mwana Wake mmodziyo.

   CHORUS:
   Dzina loyeratu (loyera), Dzina lofatsanso (lofatsa),
   Lomwe nalinena angelowo,
   Pa usiku uja (dzinalo), Dzina lokomatu (dzinalo),
   Ndilo la Ambuye Yesu.

2. Dzinalo lipatse dalo, Ndi chimwemwe mtimanga,
   Ndidzauza anthu ena Za chokoma Chakecho.

3. Moyo wanga udzayimba Za chikondi Chakecho;
   Ndidzatamandabe dzina , Lopambana onsewo.

No. 124
NDIKWEZE YESU YEKHA
Fannie. E. Bolton
Doh is E flat.

1. Ndikweze Yesu yekha m’zinthu zonse;
   Amveke, aoneke yekhayo;
   Mu ntchito, m’maganizo ndipo m’mau,
   Ambuye aoneke yekhayo.

2. Ndi Yesu atonthoza akulira,
   Yekhayo angachotse msoziwo;
   Yekhayo angatule akatundu,
   Yekhayo angachotse manthawo.

3. Ndileke mau onse ena chabe,
   Ndileke zakupusa zangazo;
   Ndikweze Yesu, ndisanyade konse,
   Ndisadzitame, koma Iyeyo.

4. Ndi Khristu amapatsa ‘ne zosowa,
   Ndi yekha amapaysa mphamvunso.
   Yekhayo m’thupi, m’moyo, ndi mu mzimu;
   Ndi Khristu yekha nthawi zonsezo.

No. 125
MULI DZUWA M'PHIRI MUJA
Melody by M.T Haughey, arr.
Doh is A.

1. Muli dzuwa m'phiri muja, Muli dzuwa m'nyanjamo;
   K'wala kwake kumagwera Pa maudzu ponsepo;
   Koma dzuwa lopambana Liri m'mtima mwangamu;
   Ka'mba komwe mukhalitsa, Kuli dzuwa lowala.

   CHORUS:
   Muli dzuwa lakuwalitsa! Muli dzuwa m'mtimanga.
   Yesu adzachotsa mdima, Muli dzuwa m'mtimanga.

2. Ndisiya 'ne nsoni zanga Ndi zobvala za nsanza;
   Mundibvekatu zoyera, Ndiyamika m'mtimamo;
   Kuli malo a ulemu Munandikonzera 'ne;
   Mtima wanga ufunako, Ndidzatsata Inutu.

3. Inu, Yesu, mwandigula, Ndine wanu konseko,
   Munayatsa nyali yanga, Iwalire Inuyo;
   Kuli malo a ulemu Munandikonzera 'ne;
   Mtima wanga ufunako, Ndidzatsata Inuyo

No. 126
IRIPO NYIMBO NDIKONDA
E.O. Excell
Doh is G

1. Iripo nyimbo ndikonda Kuyimba ineyo,
   Ya Yesu Mbuye wangayo, Ch'omboledwere 'ne.

   CHORUS:
   Ntaomboledwa 'ne, Ndzalemekezatu dzina la Ambuyeyo.
   Ntaomboledwa 'ne, Ndidzalemekeza dzinalo.

2. Wakukwanitsa mtimanga Ndi yesu Khristuyo;
   Ndichita chifuniro 'ke, Ch'omboledwere 'ne.

3. Iripo mboni yangayo, Chomboledwere 'ne,
   Yochotsa nkhawa, manthanso, Ch'omboledwere 'ne.

4. Alipo malo angawo, Wandikonzera 'Ye.
   Kumene ndidzakhalako, Ntaomboledwa 'ne.

No. 127
MULUNGU ASAMALABE
S. W STRAUB
Doh is F

1. Mulungu asamalane Mbalame zonsezo;
   Ngatitu azikondadi, Akonda inenso.

   CHORUS:
   Andikonda, andikonda, Akonda inenso;
   Akonda zinthu zonsezo, Akonda inenso.

2. Maluwa mthengo monsemo Napanga Mbuyeyo;
   Ngatitu awakondadi, Akonda inenso.

3. Mulungu, mlengi wathuyo Apanga zonsezo;
   Samaiwala ana ‘ke, Akonda onsewo.

No. 128

# NTHAWI YA PEMPHERO

W.H Doane.

Doh is E flat

1. Nthawi ya pempheroyo, powerama ife,
   Tisonkhana kwa Yesu, Ambuyathuyo;
   Tikakhulupiratu adzatibisanso,
   Tidzapeza mpumulo tikapempheratu.

   CHORUS:
   Ndi yokomadi, nthawi ya pempho.
   Tidzapeza mpumulo tikapempheratu.

2. Nthawi ya pempheroyo, Yesu ali mfupi
   Ndi chifundo Chakecho atimvera ‘fe.
   Atiuza nkhawazo, tizitaye kwa ‘Ye,
   Tidzapeza mpumulo, tikapempheratu.

3. Nthawi ya pempheroyo, akuyesedwawo
   Amatula kwa Yesu zisoni zawo;
   Yesu wachofundoyo amazichotsatu,
   Tidzapeza mpumulo tikapempheratu.

4. Nthawi ya pempheroyo tikhulupiranso
   Kuti zomwe tisowa tilandiradi;
   Tikakhulupiradi nkhawa zichokanso;
   Tidzapeza mpumulo tikapempheratu.

No. 129
YESU MNALONJEZA
Dr. W.O. Perkins
Doh is A flat

1. Yesu mnalonjeza, Kuti komwetu
   Asonkhana ‘tatu, Muli komweko;
   Tikukhulupira, Tigwadira ‘Nu;
   Yesu, mtidalitse, Mkhale nafetu.

   CHORUS:
   Yesu, mtidalitse Popemphera ‘fe;
   Yesu, mtidalitse, Mkhale mfupimo.

2. Mnasonkhana nafe, Nthawi zonsezo,
   Tikusowaninso Mpaka mapeto;
   ‘Dzani, Mpulumutsi, Mtidalitsenso;
   Mutimvere ife, Tikupempha ‘Nu.

3. Yesu, mtithangate Poyimbira ‘Nu,
   Pempho liri lonse Mlilandiretu;
   Chikh’lupiro chathu Mchikulitsenso;
   Mdzaze ‘fe chikondi, Ndi ku’nikanso.

No. 130
NDINE WANUYO
W.H Doane
Doh is A flat

1. Ndine wanuyo, ndamva mauwo, A chikondi chanucho;
   Mundikoketu mfupi ndinuyo, Mwa chikhulupirocho.

   CHORUS:
   Mndisendeze (mfupi), mfupi Mbuyanga, Ndi pa mtanda Wanuwo;
   Mndisendeze mfupi, Mbuye wanga ‘Nu, Ndi pa mwazi Wanuwo.

2. M’nchito yanu mndipatulire ‘ne, Mwa chisomo Chanucho;
   Moyo wangawo uyang’ane ‘Nu, Ndichitetu zanuzo.

3. Ndikondwera ‘ne  pakupitatu, kugwadira Mbuyeyo;
   Pakunenatu naye mtserimo, Monga bwenzi langalo.

4. Sindidziwatu za chikondicho, Mpaka n’dzanke tsidyalo;
   Sindifikira za chimwemwecho, Mpaka n’dzake kwanuko.

No. 131
INETU NDIFUNADI
W.H DOANE
Doh is F

1. Inetu ndifunadi Kufanana ndi Yesu,
   Andidzaze mtimamo Ndi kufatsa Kwakeko;
   Ndidziyenda monga ‘Ye Mdziko la zoipali;
   Ndine wosaukadi, Yesu mkhale mtimanga.

2. Ngati amva khwangala, Nayang’ana mphetazo,
   Nasamala zonsezo, Ndithu andimveranso,
   Adzandiphunzitsa ‘ne, Nakhululukira ‘ne;
   Ndikhaletu wangwiro, Yesu mkhale mtimanga.

3. Popemphera ndikhale MOnga Yesu Mbuyeyo;
   Ndipumule mwa Iye, Andimwetse madziwo.
   Mwa chisomo ndabadwa, Ndafa mwa zoipazo,
   Ndikhulupiriretu, Yesu mkhale m’mtimanga.

No.132
YESU, MUNDISUNGETU
W.H. Doane
Doh is F

1. Yesu, mundisungetu, Mfupi mtanda wanu;
   Ndipezepo kasupe Wondichiza mtima.

   CHORUS:
   Mtandawo, mtandawo, Nditamanda mtanda,
   Mpaka moyo wangawo Udzapume mmwamba.

2. Nsisi zandipezanso, Pomwe pali mtanda.
   Ee! Pa mtanda nthandayo Indiunikira.

3. Pa mtandapo ndiona Mwana wa Mulungu,
   Mndithandize, Mbuyanga, Kuyendabe nanu.

4. Pa mtandapo ndzalinda, Ndikuyembekeza,
   Mpaka ndidzafika ku Dziko la kumwamba.

No. 133
NDIYENDE NANU MULUNGU
Edwin Barnes
Doh is A flat.

1. Ndiyende nanu Mlungu ‘Nu , Mongatu Enoke kalelo;
   Mndigwire dzanja langalo, Mulankhule ndi inenso;
   Ngakhale sindionatu, Ndiyende ndinu,Mbuyanga.

2. Sin’funa kwenda ndekhatu, Namondwe amaombabe;
   Misampha inditchera ‘ne, Adani andizinganso;
   Mutontholetse nyanjayo, Ndiyende ndinu, Mbuyanga.

3. Mukandigwira dzanjali, Nditayatu za dzikoli;
   Ndzayenda molimbikatu, Ndzasenza mtanda wangawo;
   Mpakatu ndzake m’mwambamo, Ndiyende ndinu, Mbuyanga.

No. 134
NDI MTIMA WANGA WONSE
E.S LORENZ
Doh is C.

1. Ndi mtima wanga wonsewo, Ndikweza mau kwnuko,
   Ndiyimbe bwanji chikondi Chozizwitsa cha Yesu Mbuye?

   CHORUS:
   Chikonditu chozizwacho, Chikondi cha Yesuyo;
   Chikonditu chozizwacho, Chikondi cha Yesuyo;

2. Chipatsa ‘ne mtenderewo, Chiunikira m’njirayo,
   Chichotsa bvuto chikondi Chozizwitsa cha Yesu Mbuye.

3. Chiyembekezo changacho Chonditurutsa m’machimo;
   Pakufa ndi’mba chikondi Chozizwitsa cha Yesu Mbuye.

No. 135
NDIKONDA INU, MBUYANGA
R. E. HUDSON
Doh is C

1. Ndikonda Inu, Mbuyanga, Koposa zonsezo;
   Chifukwa mwandipatsatu Mtendere wanuwo.

   CHORUS:
   Sanazinene zonsezo (zonsezo), Za nsisi Zakezo;
   Sanazinene zonsezo (zonsezo) Watsuka inenso.

2. Mukhala mfupi ndineyo, Koposa onsewo;
   Ndikonda kuganiza 'Nu Koposa zinazo.

3. Mwandikondwetsa, Mbuyanga, Ndisangalaladi;
   Popanda nsisi zanuzo Sindingakondwei.

4. Ambuye wanga, Yesuyo, Mkayenda nanedi,
   Masiku onse pansipo Ndidzakondweradi.

No. 136
AKAN’TSOGOZA NDINKAKO
J.M Black
Doh is E flat

1. Akan’tsogoza ndinkako, Ndikhulupira Mbuyeyo;
   Ndikumbukira kutitu Anandifera pa mtanda.

   CHORUS:
   Yesu anditsogozatu Ulendo wanga wonsewo.
   Bwenzi loona ndiyeyo, Ndikumbukira mtandawo.

2. Ndikonda mau Akewo, Anditsogoza Mbuyeyo;
   Kufuna Kwake,ndichite, Anandifera pa mtanda.

3. Ndzapita osaopai, Akhala nene Yesuyo,
   Pa tsiku lina n’dzaona Yesu tsamwali wa mtanda.

No. 137

## DZIKO AI, KOMA YESU

Jno. R. Sweney

Doh is F

1. Dziko ai, Koma Yesu, Dziko ndi la chabetu;
   Nsisi zake zikhalitsa Nthawi zonse yemweyo.

   CHORUS:
   Nsisi Zake n'zazikuru, Ndi chikondi Chakenso;
   Chiombolo chozizwitsa, Moyotu wosathawo!

2. Dziko ai, koma Yesu, Wondisangalatsa 'ne;
   Iye andiyang'anira, Nkana m'vuto ndi mbabe.

3. Dziko ai, koma Yesu, Ndiyang'ane Iyeyo;
   Pa ulendo wanga wonse, Andiunikira 'ne.

4. Dziko ai, koma Yesu, Mtandawo ndigwiradi;
   Mpakatu maso ndi maso, Ndidzamone Mbuyeyo.

No. 138
NDIPEREKA MOYOWU
W.J Kirkpatrick
Doh is D

1. Ndipereka moyowu Kwa Ambuye wanga ‘Nu;
   Manjawa achitetu Chifuniro chanucho.

   CHORUS:
   Munditsuke ine mtima mbu (E, ine mbu),
   M’mwazi wa Ambuye Yesuyo (E, Yesuyo).
   Kwanu Mbuyanga ndidziperekadi,
   Kwanu nthawi zonsezo.

2. Ndipereka myendoyi, Ikhaletu yanuyo;
   Mau ayimbirenso Inu Mfumu yangayo.

3. Ndipereka milomo, Inenetu mauwo;
   Ndipereka chumacho, Sindimana kanthui.

4. Ndipereka nsikuzo, Kuti ndiyamike ‘Nu;
   Ndipereka nzeruzo Kuchitatu ntchitoyo.

5. Chifuniro changacho Chikhaletu chanunso;
   Ndipereka mtimanga, Ukhaletu wanunso.

6. Ndipereka chikondi pa mapazi anuwo;
   Munditenge ndensene, Ndikhaltu wanuyo.

No. 139

TSAMWALI NDAMKUMANAYO

Geo. C . Stebbins

Doh is A

1. Tsamwali ndamkumanayo, Anandikonda kale;
   Kukonda kwandigwirako, M’kukondamo nditsale,
   Ku Mtima kundimangako, Kosamasuka konse,
   Ambuye ndine wanuyo, Ku nthawi nthawi zonse.

2. Tsamwali ndamkumanayo, Anandifera yekha;
   Anandipatsa moyowo, Ndatenga ine ndekha;
   Zimene ndiri nazozi, Za yesu, mwini ine ndekha;
   Ndi moyo wanga wonse ndi Wakenso nthawi zonse.

3. Tsamwali ndamkumanayo, Ndapeza mphamvu zanga,
   Pakundisunga inemo, Ndiyende m’njira mwanga;
   Zolemerera zoti mbe Zindilimbitsa monse,
   Ndalema kuno komweko, Nkupuma nthawi zonse.

4. Tsamwali ndamkumanayo, Wokoma mtima Wake,
   Wotsogolera nzeruzo, zisunga m’njira Mwake;
   Kwa Iye wondikondako, Sandichotsamo konse,
   Pa moyo, imfa, nayeyo, Ndiripo nthawi zonse.

No. 140
MAU A YESU
Louis Spohr
Doh is D

1. Ndinamva Yesu akuti, Idza udzapume;
   Wolema'we ndi zoipa, Tsamira pa Ine.
   Ndinadza kwa Yesu momwe Ndinali-wolema;
   Mwa Iye ndinapumula, Nandikondweretsa.

2. Ndinamva Yesu akuti, Ndipatsa kolere
   Madzi a moyo wosatha, Idza udzamwetu
   Ndinadza kwa Yesu ndi 'mwa Mu mtsinje wamoyo;
   Ndipo ndinatsitsimuka, ndikhala mwa Iye.

3. Ndinamva Yesu akuti, Ndine kuunika;
   Yang'anitsitsa kwa Ine, Ndipo udzakondwa.
   Ndinayang'ana kwa Yesu, Mwa Iye ndiwala;
   Ndidzayendabe m'ku'nika, Mpaka kumwambako.

No 141

NDIKHALETU WANU

F.E Belden

Doh is A flat

1. Ndikhaletu wanu Mbuyanga; Konseko konseko;
   E, kufuna kwanu ndichite, Mndithandizetu.

   CHORUS
   Wanutu (Mbuye), Wanutu (Mbuye), Ndine wanu Mbuyanga;
   Wanutu (Mbuye), Wanutu (Mbuye) Ndine wanu Ieroli.

2. Chuma ninji ko popandatu Inuyo, Mbuyanga,
   Ndidzasiya zinthu zonsezo, Ndidzatsata ‘Nu.

3. Pofulatira ‘ne dzikoli, Mkhaletu nanenso;
   Inu ndinu Cuma changaco; Mnditonthozetu.

No. 142
TSIKU LOKOMA LEROLI
Kingsley
Doh is E flat

1. Tsiku lokoma leroli, Loposa enawo;
   La kuganiza zinthu za Mulungu wathuyo.

2. Inde, kukoma kumvatu Za mau acewo,
   Otembenuza mtimawo Kuloza mmwambamo.

3. Ngati sititha chimolo, Kusiya tokha ‘fe
   Ambuye wathu, Yesuyo, Adzalicotsatu.

No. 143
MBUYE MTIPITITSE
Sicilian
Doh is E

1. Mbuye, mtipititse tonse, Ndi dalitso lanulo;
   Mwa cikondi canu, Mbuye, Mutipatse nsisizo.
   Mutitsitsimutse ife Pakuyenda m'dzikoli.

2. Tiyamika Inu, Mbuye, Kamba ka uthengawu;
   Mphatso za cipulumutso Zidzazetu mtimamu,
   Kuti ife tikhalebe Okhulupirikawo.

3. Nsiku zathu zonse, Mbuye, Tipereka kwathuko;
   Mutilimbikitse, Mbuye, Kuti tisaopei,
   Mpaka tidzaone tonse, Ulemerero wanu.

No. 144
NDIPITABE MTSOGOLOMO
Chas. H. Gabriel
Doh is A flat.

1. Ndipitabe mtsogolomo, Ndikwera nthawi zonsezo;
   Ndipempha Inu, Mbuyanga, Mndikweze ’ne pamwambapo.

   CHORUS:
   Mndikwezetu, ndiime ’ne, Pamwamba nsiku zonsezo;
   Pamene sin’nafikepo, Mndikweze ’ne pamwambapo.

2. Sin’funatu kukhalabe Kumene kuli nkhawazo;
   Ngakhale ena ’khalelo, Mndikweze ’ne pamwambapo.

3. Ndikhalebe pmwambapo, Ngakhale ndiyesweda ’ne;
   Ndikhulupira kutitu, Mndikweze ’ne pamwambapo.

No. 145
MSAKANE NTCHITO YA MULUNGU
F.E Belden
Doh is E

1. Msakane nchito ya Mulungu wanuyo, Mupite komweko Afuna Iyeyo.
   Anaitana ’nu, Amaitanabe, Mudzakondweradi Pogwira nchitoyo.

   CHORUS:
   Bwerani, Msakane nchitoyo, Bwerani, Kwa Mlungu wanuyo.
   Msakane nchito ya Mulungu wanuyo, Mupite komwe Afuna Iyeyo.

2. Msakane nchitoyo, Imvani leroli; Mwakana kalelo, Musakanenso bi!
   Zotuta nzambiri, Acepa ’nchitowo, Mukondekondetu Kukopa anthuwo.

3. Msakane nchitoyo, msacedwecedwenso; pakukanidwabe Cikondi cicoka.
   Pamene Mzimuyo Aloza njirayo, Popempha Yesuyo, Idzani leroli.

No. 146
MUKHALE M'MTIMA MWANGA
Samuel Wesley
Doh is E flat

1. Mukhale m'mtima mwanga Ee, Yesu, Mfumuyo.
   Mundiyankhire ine Mafunso angawo.
   Mukhale m'mtima mwanga, Mnditsogoleretu,
   Kuti ndionetsere Ukuru wanuwo.

2. Kacisi wa mtimanga Wayeretsedwatu,
   Ulemerero wanu Uwale mkatimo;
   Ndi thupi langa lonse Likhale lanulo,
   Licite nthawi zonse Kufuna kwanuko.

3. Ziwalo zanga zonse, Mzilamuliretu,
   Mucite nazo zonse Kufuna kwanuko;
   Ndidzipereke ndense, Osang'ung'udzanso,
   Polamulidwa nanu Mu nchito zangazo.

4. Ndidzapumula ndithu Mu mtima mwangamo,
   Ndidzalindira Inu, Mukandifunatu;
   Mukhale m'mtima mwanga, Ee, Yesu, Mfumuyo,
   Mundiyankhire ine, Mafunso ngawo.

No. 147

TATE MUNDISENDEZE MFUPI

J.H Tenney

Doh is A

1. Tate mudisendeze mfupi, Ndifuna Inuyo;
   Mundiyangate mmanja mwanu, Ndipume mwanumo.

   CHORUS:
   Zingwe za cikondicho, Mfupi, zikokere ‘ne.
   Mfupi, mfupi, Ndinu m’mwambamo.

2. Yesu mundisendeze mfupi, Ndisasiye Inu;
   Dzanja lanu linditsogoze, Ndisasocerei.

3. Mzimu mundisendeze mfupi, Ndifane ndinuyo;
   Mtima mwangamo munditsuke, Ndiyere ine mbu!

No. 148
PONSE PONSE NAYE YESU
D.B Towner,by per
Doh is D

1. Ponse ponse naye Yesu ndzapita, Ponse ponse anditsogolera ‘ne.
   Pakapanda Iye sindikondwai, Ponse ponsse naye sindiopatu.

   CHORUS:
   Ponsepo, ponsepo, sindiopai, Ponse ponse naye ndidzapitapo

2. Ponse ponse Yesu ali ndi ine, Nkana ena andisiye m’dzikoli.
   Nkana njira yanga iri yoopsya, Ponse ponse ndimyamika Yesuyo.

3. Ponsepo ndi Yesu ndidzagonatu, Mmene mdima undiphimba ineyo.
   Ndziwa kuti ndidzauka tsikulo. Ponsepo ndi Yesu ndiko kwathuko.

No. 149

YENDA  MKUUNIKA

Geo. C. Hugg

Doh is D

1. Yenda mkuunika kwakeco, Atsogolere ‘we;
   Ndi Mzimu wa kumwambayo ‘Dzainga mdimawo.

   CHORUS:
   Yendanibe, Mkuunikatu;
   Yendanibe, Mkun’ikatu kwa Mlunguyo.

   Bass and Tenor:
   Yendanibe mku’nikatu kwa Mlunguyo,
   Yendanibe mku’nikatu kwa Mlunguyo,
   Yendanibe mku’nikatu kwa Mlunguyo;
   Mku’nikatu kwa Mlunguyo.

2. Yenda mku’nika Yesuyo, Wowala m’mauyo,
   Atsogolera onsewo, Okhulupirawo.

3. Nkana mithunzi igwetu, kudetsa njirayo,
   Mdimawo udzathawatu, Ku’nika kwaceko.

4. Yenda mku’nika kwaceko, Udziwe nsisizo,
   Cikondi cidzaposadi, Pofika mmwambamo.

No. 150
OKUNKHAWO ALI KUTI?
Geo. F. Root
Doh is G

1. Okunkhawo alitu kutiko? Amene akunkhatu zabwino?
   Kocoka mu dziko loipali, Pocita ndi mau a Mlunguyo?

   CHORUS:
   Ndanitu adze kudzakunkha, Kusonkhanitsira anthu m'mwambamo?
   Ndi yani atithandizeko, Pofunafuna zobalazo?

2. Pitani mu mphambano monsemo, Funani mepezemo abwino;
   Pitani kwa anthu ponse ponse, Musonkhanitsire kumwambako.

3. Zobala zakhwima ponse ponse, Za m'dzikomu zilindira ife.
   Okunkha achepa ku ntchitoyi, Zambiri zidzaonengekatu.

4. Anthuni idzani ndi zidazo, Kudzasonkhanitsa zam'mundamo;
   Gwiranibeni mpaka Mbuyeyo, Adzabwera ali kukondwatu.

No. 151
NDIGANIZA ZA DZIKO LOKOMETSA
Jno. R Sweney
Doh is A

1. Ndiganiza za dziko lokometsalo, Komwe n'dzafikako tsikulo;
   Podzaima pa mbali pa M'lumutsiyo, Ndidzabvala nyenyezizo ko?

   CHORUS:
   Ndidzabvala nyenyezizo ko,  Mbuyanga, Mmene dzuwa lidzalowadi(lowadi)?
   Mmene n'dzauka mmalo a mpumulowo, Ndidzabvala nyenyezizo ko(tsikulo)?

2. Mphamvu yakeyo ndigwiretu nchitoyo, Kuti ndikopetu anthuwo;
   Kuti n'dzapate nyenyezi pa tsikulo, Mmnene Mbuye 'dzayamike 'fe.

3. Ndidzakondwera poona Mbuyangayo, ndikupereka mituloyo;
   Ndidzakondwera m'mzinda wa golidiyo, Ndikadzabvala nyenyezizo.

No. 152
YESU MUNDILANKHULE
Adapted by L.L. Pickett
Doh is E flat

1. Yesu, mundilankhule, Mau ofatsawo;
   Mndinong'oneze kuti, Sulitu wekhawe.
   Mtima munditsegule, Kuti ndimvere 'Nu;
   Mdzaze mu mtima mwanga, Kuti ndikondwedi.

   CHORUS:
   Mundinong'onezetu, mwa nsisi zanuzo,
   Udzangonjetsa ndithu, Udzamasukadi.
   Mundilankhule, Mbuye, tsiku ndi tsikunso,
   Ndimvetu mau anu, Sulitu wekhawe.

2. Yesu, munene mau, Ndi ana anuwo,
   Kuyang'anira Inu, Muwaphunzitsetu;
   Kuti apereketu Moyo kwa Inuyo,
   Udze ufumu wanu, Kuti 'dzaone 'Nu.

3. Kale munaonetsa Kufuna kwanuko,
   Yanga ndidziwe nchito, Ndichite zanuzo;
   Ndilemekeze Inu, Kwa anthu onsewo,
   Ncite kufuna kwanu, Masiku onsewo.

No. 153
SINDIPEMPHERA, MBUYANGA
F.E Belden
Doh is G

1. Sindipemphera, Mbuyanga, Za mwazo;
   Mndipulumutse m'chimolo Lero lokha;
   Mau ndisalankhulenso Oipawo;
   Msungetu mlomo wangawu, Lero lino.

2. Ndzagwira nchito yanuyo, Ndzapemphanso;
   Ndikhala wacifundoyo, Lero lokha;
   Mundithandize, Mbuyanga, Kumvera 'Nu;
   Kuti ndidzipereketu Pa leroli.

3. Ngatitu moyo wangawo Utha ndithu;
   M'malonjezano anuwo Ndikhalebe;
   Sindipemphera, Mbuyanga, Za mawazo;
   M'ndisunge m'manja mwanumo Pa leroli.

No. 154
MLONDA TANDIUZA INE
W.B Bradbury
Doh is G

1. Mlonda, tandiuza ine, Kunja kuli kucako?
   Zosonyeza kudza kwace, Kodi zionekadi?
   Inde, mlendo, taonani, Kuca kwayandikiratu,
   Bvala za kukoma zako, Kuli kuca, dzuka ’we.

2. Mlonda, nyali iunika Mommo m’njira mwakomo;
   Zozizwitsa m’dziko monse, Zisonyeza tsikulo.
   Podzaomba pa lipenga, Pakudzuka a ku manda,
   Omwalira mwa Ambuye, Adzabvala cosafa.

3. Mlonda, pfu’la liri kudza Tsiku lalikurulo.
   Onse alalike kuti, Mfumu yayandikatu.
   Inde, mlendo ’we, ndiona, Dziko lopambana lija.
   Mzinda wopambana yonse, Uoneka tsidyalo.

4. Mlonda, undiuze inea mu mzinda momwemo,
   Mmene Mfumu ikukhala, Pa cimpando caceco.
   Dziko lija likuwala Ndi ulemerero wace;
   Kuli duwa ndi mitengo, Ndi mitsinje yoposa.

5. Dzuwa lituruka ndithu, La usana womwewo.
   Onse alalike kuti, Tsiku lyandikatu.
   A ulendo aonenso, Kuli phiri la Mulungu;
   Tidzafika konko msanga, Tidzakondwererako.

No. 155
KAPENATU SI KU PHIRIKO
Carrie E. Rounsefell
Doh is F

1. Kapenatu si ku pjiriko, Kapena ku nyanjako,
   Kapena ku nkhondo komwetu, Mufuna ndipite ’ne
   Komatu mwa mphamvu ya Mbuyeyo, Ndzapita mufunako.

   CHORUS:
   Ndzapita kumene mufunako, M’phiri, m’dambo, ndi m’nyanjamo,
   Ndzanena zimene mufunazo, Ndzatsata mpulumutsiyo.

2. Alipo mau Ambuyeyo Afuna ndinenedi;
   Kapena kuli wocimwayo Wosowa thandizoli;
   Ambuye, mkanditsogoza ‘ne, Ingabvute njirayo,
   Ndzauza uthenga wabwinowo, Ndzanena mufunazo.

3. Alipo malo a inenso Ku munda wa Mbuyeyo,
   Ndzagwira nchito yotutayo ya Yesu wopacikwa.
   Pokhulupirira mwanumo, Podziwa mndikonda ‘ne,
   Ndzacita kufunatu kwanuko, Ndzakhala mufunazo.

No. 156
MAU AKUKWIYA LEKA
H.R. Palmer
Doh is E flat

1. Mau akukwiya leka, Muasenene konsetu;
   Muwameze mau onse Asanadetse m’lomowo.

   CHORUS:
   Kondananitu, Ati Ambuye, Ana mverani malamulowo;
   Kondananitu, Ati Ambuye, Ana, mverani lamulo.

2. Cikonditu ndi coyera, Ndi cibwenzi comwenso,
   Musaciononge konse Ndi mau akukwiyawo.

3. Maubwenzi amasweka, Ndi mabanja omwenso,
   Ka’mba mau a kukwiya Olankhulidwa mwa nsontho.

No. 157
WAKUFESA NDI KULIRA
C.S Cable
Doh is E flat

1. Wakufesa ndi kulira, Mbeu za cikondico,
   Wosatopa, wosagona, Yesu amdalitsa ‘ye.

   CHORUS:
   Ona! Mmera wakukondwa, Dzinthu dzonse dzacanso.
   Ona! M’minda mwayeratu, layandika khunkhalo.

2. Mvula idzatsiririrapo, Dzuwa ‘dzawaliranso,
   Ndi zipatso zidzabala, M’mphamvu ya Mulunguyo.

3. Fesa mbeu, usatope, Usaope konsetu.
   Nkana utapeza bvuto, Udzatuta mokondwa.

No. 158
MASIKA A DZIKO AYANDIKA
F.E Belden
Doh is E flat

1. Masika a dziko ayandikatu, Aitana Mbuye okololawo;
   Ndi minda yayera pa dziko lonse, Ndi mwini zotuta wayandikanso.

   CHORUS:
   'Dzanitu msanga, Tengatu zotuta; Mdzititenge 'fe, Kwathuko.

   Alto, Tenor, ndi Bass:
   Idzanitu angelo, msangatu; Tengerani zotuta mmwambamo.
   Mudzatengetu ife, kunkatu, Kwathu mmwambamo.

2. E, tsiku lopanda misonzi konse, Layandika kudza mothamangatu;
   Akubalalika ndi ucimowo, mwasonkhetu nthawi isanathei.

3. Ikomatu nchito ya cikondico, Kasupe wosaphwa wa kumwambako;
   Cikonditu ndico ciitana 'fe, cigwiritsa nchito, cibalitsatu.

No. 159

MBUYANGA, NDISOWA INU

F.E Belden

Doh is G

1. Mbuyanga, ndisowa Inu! Ndine wosaukadi;
   Mundigwire dzanja, Mbuye, Mundilimbikitsetu.

   CHORUS:
   Nthawitu zonsezo, Ndimasowa Inu, Mbuye!
   Nthawitu zonsezo, Yesu mundisunge' ne.

2. Mundibveke zakuyera, Zanga ziri nsanzatu;
   Mndiphunzitse kupemphera, Mundipatse mphamvuzo.

3. Munditsogolere, Mbuye, Ndekha ndilepheradi;
   Myende nane pa myalapo, Ndinu nyali yangayo.

4. Ndingapezetu mabvuto, Oliritsa mtimanga;
   Ndidzaumirira Inu Mdzandisangalatsadi.

No. 160
YESU ANDISUNGETU!
I Allan Sankey
Doh is D

1. Yesu andisungetu! Ndi mphamvu yaceyo;
   Dziko lisandidetse; Kuti nditsate ‘Ye.

   CHORUS:
   Yesu andisungetu! Mbuye ndipempha ’Nu;
   Inetu ndine cabe, cabe, Inu ndi zonsezo.

2. Yesu andisungetu! Nditumikire ‘Ye;
   Ndicitetu kufuna, Kwa Yesu, Mbuyeyo.

3. Yesu andisungetu! Dziko ndilisiya;
   Ndikhaletu wofatsa, Woyera mtimamo.

4. Yesu andisungetu! N’khaletu waceyo;
   N’khaletu wace yekha, Ku nthawi zonsezo.

No. 161
TSAMWALI NDIRI NAYE
Hubert P. Main
Doh is F

1. Tsamwali ndiri naye Wokondakondadi;
   Akonda ‘ne kopostu, Akonda konseko;
   Ndikhale ndi tsamwaliyo, Ndimkonda bwinotu;
   Pamodzi ndi Ambuye Ndikhalabe.

2. Ndifo’ka ndithu mwina, Adziwa mbuyeyo,
   Auza ’ne ndimtsamire, Andithangatatu;
   Anditsogoza inetu, Mwa kuunikako,
   Pamodzi ndi Ambuye Ndiyendabe.

3. Zokondwa, za cisoni, Ndiuza Mbuyeyo;
   Ndiuza Mbuye zonsetu Za mtima mwangamo;
   Auza ‘ne cocitatu, Anena, Yesanso;
   Pamodzi ndi Ambuye ndinenabe.

4. Adziwa ndikufuna, Kukopa winayo,
   Auza ‘ne kupitatu Kunena nayenso;
   Cikondi ca Mulunguyo, Ndi imfa ya Yesu;
   Pamodzi ndi Ambuye Ndicitabe.

No. 162
YESU ANDITSOGOZATU
Rev. R. Lowry
Doh is A flat

1. Yesu nditsogozatu; Nanganso ndifunanji?
   Kodi ndimkaika Iye, Wonditsogolerayo?
   Mtenderewo andipatsa, Mwa cikhulupiroco!
   Nkana lindigwere bvuto, Yesu athangata 'ne;
   Nkana lindigwere bvuto, Yesu athangata 'ne.

2. Yesu anditsogolera, Andisangalatsanso;
   Athandiza 'ne m'mayeso, Andidyetsa mkatewo;
   Nkana ndiri wakutopa, Ludzu landigwiranso,
   Mu Thanthwelo Yesu Kristu, Ndionamo madziwo;
   Mu Thanthwelo Yesu Kristu, Ndionamo madziwo.

3. Yesu anditsogolera, Mwa cikondi caceco!
   Alonjeza 'ne mpumulo, Mnyumba ya Atateyo;
   Nkadzauka tsiku lija, Ndidzapita mmwambamo,
   Ndidzayimba kosaleka, Yesu natsogoza 'ne;
   Ndidzayimba kosaleka, Yesu natsogoza 'ne.

No. 163
‘MVANI YESU AITANA
F.E Belden
Doh is D

1. ‘Mvani Yesu aitana, Ndani angagwiretu?
   Mindayo yayera kale, Ndani akakunkhemo?
   Momvekadi aitana, Mphotho ’dzalandira ’we.
   Ndani angayankhe msanga, Ndine Mbuye, tumeni.

2. Nkana sungapite mtari Ku maiko enawo,
   Ungapeze anthu ena Apafupi ndi iwe.
   Ngati sungalalikire Monga ngati Paulo,
   Unganene za cikondi Ca Ambuye wakoyo.

3. Ngati sungakhale mlonda Wocenjeza anthuwo;
   Kuwauza anthu njira Yonka nayo mmwambamo;
   Pakumpherera ena, Ungagwire nchitoyo,
   Ungachite ngati Huri pothangata Moseyo.

4. Mmene anthu alikufa, Mbuye aitanabe;
   Wina asamamve muti, Singacite kanthui.
   Gwira nchito wakupatsa, Nuigwire msangatu;
   Ndi kuyankha poitana, Ndine Mbuye, tumeni.

No. 164
PA MAPAZI ACE YESU
Arranged
Doh is F

1. Pa mapazi ace Yesu, Ndimva mau acewo!
   Ee, pafupi ndi Ambuye, N'khale nthawi zonsezo;
   Pa mapazi ace Yesu, Ndiyang'ana m'mbuyomo,
   Ee, cikondi cace conse, cakopadi mtimanga.

2. Pa mapazi ace Yesu, Malo opambanawo;
   Ndisiyepo chimo langa, Ndi kupeza mpumulo;
   Pa mapazi ace Yesu, Ndimalira mtimanga,
   Pomwe ndimapeza nsisi, Tsiku liri lonselo.

3. Inu Yesu mndidalitse, Ndigwadira Inuyo;
   Muyang'anetu pa ine, Nane ndikuoneni;
   Ndikhaletu nawo mtima, Monga Yesu Mbuyeyo,
   Ndionetseretu Yesu, Cilungamo cangaco.

No. 165
NDIKONDA, NDIKONDA AMBUYANGA
Jer. Ingalla
Doh is E flat

1. Ndikonda, ndikonda Ambuyanga ‘Nu;
Ndikonda Yesuyo, Mpulumutsitu.
Ndikonda Inuyo muzidziwadi;
Zinchito zinena kukonda kwanga.

2. Ndikondwa, ndikondwa kopambanadi!
Ndaima pa phiri ndiyang’anitsa
Ku mzinda woyera ndikakhaleko,
Ndi Yesu, angelo, ndi anzangawo.

3. Yesu ‘Nu, Mp’lumutsi, mndidalitsetu,
Ndinutu cimwemwe mpumulo wanga.
Ndiyimba cikondi ca Mbuyangayo;
Cisomo canuco cindidzaza ‘ne.

4. Ndaniyo aposa Mpulumutsiyo?
Akonda inenso nan’thangata ‘ne.
Ndiyamika Mbuye, ndiyimbira ‘Ye,
Ndikondw koposa mu mtimangamo.

No. 166
THANTHWE LONG'AMBIKA
Thomas Hastings
Doh is C

1. Thanthwe long'ambikatu, Ndibisale momwemu!
   Madzi ndipo mwaziwo Zoturuka m'nthitimo,
   Zinditsuke m'mtima mbu! Zindilimbikitse.

2. Nchito zanga zonsezo, Sizikondweretsa 'Nu;
   Ndikazigwiritsadi, Ndikalira nsonizi,
   Zonse sizikwanazi, Koma Yesu yekhayo.

3. M'manja mwanga cabe bi, Mtanda ndingogwiradi;
   Marisece mbveke 'ne, Ndiri ndekha, msunge 'ne,
   Ndithawire mtsinjewo, Munditsuke m'mtimamo.

4. M'moyo uno kunsiku, Pena ndimwalira,
   Mmene ndidzaukanso Tionane masowo;
   Thanthwe long'ambikatu, Ndibisale momwemu.

No. 167
MAZIKO OLIMBA
J. Reading
Doh is G

1. Maziko olimba Ambuyathu, Waikira inutu m'mau mwace.
   Anene ciani koposa ico? Wathawira ndani kwa Mp'lumutsiyo;
   Wathawira ndani kwa Mp'lumutsiyo.

2. Ndikati uyende pa mistinjeyo, Madziwo sadzakukokolola 'we,
   Pakuti ndzakhala pamodzi nawe, Ndzadalitsa iwe, ndzapatula 'we;
   Ndzadalitsa iwe, ndzapatula 'we.

3. Poyenda 'we m'moto wa mayesowo, Cisomo cangaco cikwaniradi;
   Sudzapsa konsei ndangofunatu Kucotsa zoipa kuyeretsa 'we,
   Kucotsa zoipa kuyeretsa 'we.

4. Wakudza kwa Yesu kubisalako, Sindimtaya kunjatu kwa mdaniyo;
   Ngakhale adani amgwedezetu, Sindimsiya konse, sindimsiyatu;
   Sindimsiya konse, sindimsiyatu.

No. 168
YEHOVA NDI MBUSA WANGA
German
Doh is G

1. Yehova ndi Mbusa, Sin'dzasowa, Ndigona ku busa La msipu wace. Anditsogolera Ku madzi ace, Anditsitsimutsa Ndi mphamvu yace.

2. Anditsogolera M'mabande mwace, Cifukwa ca dzina Lokondedwalo. Ngakhale ndiyenda Pafupi imfa, Ha! Sinsidzaopa Zoipa zonse.

3. Cibonga ndi ndodo Za Mbusa wanga Zindisangalatsa Masiku onse. Mundiyalikira Pa maso panga, Mkuona kwa mdani Cakudya canga.

4. Mudzoza mafuta Pa mutu panga, Mwadzaza cifundo Mu cikho canga Udzanditsatira Ukoma wanu, Ndidzakhala nanu Masiku onse.

No. 169

# UGONERANJITU MWANA WA MFUMU?

L. Mason

Doh is B flat

1. Ugoneranjitu mwana wa mfumu,
   Kwinanso wayandikira mmwamba?
   Dzuka, nyamuk, ubvale za nkhondo;
   Bweratu nthawi isanathei.

2. Anthu a mdziko adzanjenjemera,
   Adzaopsedwa ndi kudza kwace;
   Mvetsa migugu abwera Ambuye,
   Mwana wa mfumu usacedwatu.

3. Usacedwenso ndi zinthu za mdziko
   Ulemerero udzathadi phe!
   Dula zinsinga zolimba za mdani,
   Mwana wa mfumu kondwera ndithu.

4. Usayang'anetu kwina iyai,
   Yembekezera ufumu wace;
   Ona kuwala m'mapiri monsemo,
   Mwana wa mfumu zileke.

No. 170
MULUNGU, MFUMU
Uknown
Doh is D

1. Mulungu, Mfumu ‘Nu, Ndiribe mphamvutu,
   Munandilenga, mundisunga Nthawi zonsezi.
   Munandilenga, mundisunga Nthawi zonsezi.

2. Ndiribe winnso, Ndimatsamira ‘Nu;
   Zabwino zanu zipambana, Ndicitenji ko?
   Zabwino zanu zipambana, Ndicitenjiko?

3. Ndipatse ciani ko? Poona zonsezi
   Zakhala zanu kale ndithu. Ndidzatani ko?
   Zakhala zanu kale ndithu. Ndidzatani ko?

4. Mufuna mtimangu, Ndipatsa msangatu.
   Ndikhale wanu nthawi zonse, Mndilandire ‘ne.
   Ndikhale wanu nthawi zonse, Mndilandire ‘ne.

No. 171
KUNJA KULI KUCA KODI
T. Hastings
Doh is D

1. Kunja kuli kuca kodi? Mlonda, tandiuza ‘ne.
   Kodi nthanda yaturuka? Kodi kunja kwacatu?
   Ukuona kodi kuti kwacadi?
   Ukuona kodi kuti kwacadi?

2. Tifunsitse za ulendo, Kodi ulikuthadi?
   Tayandikatu ku doko, Kodi tingaoneko?
   Tingaone dziko la kumwambako?
   Tingaone dziko la kumwambako?

3. Tipfuuletu kolimba, Kunja kuli kucatu;
   Nthanda iri kuturuka, Ioneka mwambamo.
   Kondwerani, tayandika kwathuko;
   Kondwerani, tayandika kwathuko.

4. Tiri nao mau, otitsogolera ’fe.
   Tithamangetu dzolimba, Kuti tikafikeko.
   Pfuulani mokondwera m’mtimamo.
   Pfuulani mokondwera m’mtimamo.

No. 172
AMBUYE WATHU YESU, MUBWERA LITI?
Webb
Doh is B flat

1. Ambuye wathu Yesu, Mubwera liti ko?
   Mitima yatopadi, Mucedweranji ko?
   Lidzadza liti tsiku Lonyezimiralo,
   Limene anthu anu Adzakondweranso?

2. Musiya mpaka liti, Ee, nyumba yanuyo?
   Mwacedwacedwa, Mbuye, Ambiri agwatu;
   Agwidwa ndi za dziko, Antchito anuwo;
   Atsalatu pang'ono Oyang'anira 'Nu.

3. Dzutsani anthu anu, Tumani mauwo;
   Anene anthu onse, Akudza Mbuyeyo!
   Ziyake nyali zathu, Tibvale bwinotu.
   Tikonze mtima wathu, Kuona Mbuyeyo.

No. 173
NDIKADAKHALA NACO CIKHULUPIRO
J. Ingalia
Doh is B flat

1. Ndikadakhala nacotu Cikhulupiroco,
   Sindinganjenjemeretu M'mabvuto monsemo.

2. Coti ndikalangidwa 'ne, Ndisang'ung'udzatu,
   Popwetekedwa ineyo Ndikhulupira 'Ye.

3. Comwe ciwala m'mtimanga, Pokhala m'mdimamo,
   Cimene siciopatu, Sicikaikanso.

4. Cosasunthika konsetu, Pokwiya dzikoli,
   Macimo sangakope 'ne Akandidzera 'ne.

5. Mbuye, patseni mphamvuyo, Cikhulupiroco.
   Cinkana pansi panotu Ndidzakondwerabe.

No. 174
AKRISTU ALI NACO CIYEMBEKEZO
S.Hibbate
Doh is E

1. Akristu ali nacotu Coyembekezoco.
   Cimatikondweretsatu M’mabvuto monsemo.
   Cimatikondweretsa M’mabvuto monsemo.

2. Cinena za mpumulowo Pokhala ndi Kristu.
   Pamodzi ndi anzangawo Tidzakhalitsako.
   Pamodzi ndi anzangawo Tidzakhalitsako.

3. Mayeso ndi macimowo Kulibe mdzikolo.
   Misonzi ndipo imfanso Kulibe komweko.
   Misonzi ndipo imfanso Kulibe komweko.

4. Masiku athe msangatu, Ambuye adzetu.
   Tilakalaka kuona Dzikolo ndi Inu.
   Tilakalaka kuona dzikolo ndi Inu.

No. 175
MPULUMUTSI, MBUSA WATHU
Wm. B. Bradbury
Doh is E flat

1. Mpulumutsi, Mbusa wathu, Mutitsogolere ’fe;
   Mutiwete, mutisunge, M’khola mwanu tinkemo;
   Yesu wathu, Yesu wathu, Mnatigula ana ‘nu,
   Yesu wathu, Yesu wathu, Mnatigula ana ‘nu.

2. Ndife anu, mutikonda, Mutiperekeze ‘fe,
   Mcotse nsoni ndi zoipa, Mbweze osocerawo;
   Yesu wathu, Yesu wathu, Mumve mapempherowo,
   Yesu wathu, Yesu wathu, Mumve mapempherowo.

3. Munanena mulandira Osauka omwewo;
   Inu ndinu wa cifundo, Ndi wopulumutsayo;
   Yesu wathu, Yesu wathu, Tidzatu tiana ‘fe,
   Yesu wathu, Yesu wathu, Tidzatu tiana ‘fe.

4. Tifunitsa Inu tere, Cifuniro canuco;
   Mbuye wathu, Mpulumutsi, Mutikonze mkatimo.
   Yesu wathu, Yesu wathu, Mtikondebe ana ‘fe,
   Yesu wathu, Yesu wathu, Mtikondebe ana ‘fe.

No. 176
CIYEMBEKEZO CODALA
J.G Negeli
Doh is F

1. Ciyembekezo Codalitsikaco,
   Coposa zinthu zonsezo Za dziko lathuli.

2. Iripo nyalitu Yowala m'mdimamo,
   Yomwetu isonyeza 'fe, Za manda onsewo.

3. Alipo mauwo Osangalatsatu,
   Acotsa makaikowo A nsisi zacezo.

4. Ee, mau acewo Atimasula 'fe.
   Ndiwotu nyali yathuyo, Ciyembekezero.

No. 177
MDZIKO LA KUWALALO
H.P Danks
Doh is E flat

1. M'dziko la kuunika, Kuli mzinda uko;
   Iwo sudzacotsedwa, Kulibe usiku.

   CHORUS:
   Misonzi icotsa, Imfa, nthenda ndi mantha.
   Sawerenganso, Zaka kulibe usiku.

2. Zipata nza ngaletu, za ku mzinda uko;
   Miseu nja golidi, Kulibe usiku.

3. Zipata nzosatseka, za ku mzinda uko;
   Komwe kuli mtsinjewo, kulibe usiku.

4. Samasowa dzuwanso, a ku mzinda uko;
   Yesu aunikako, kulibe usiku.

No. 178
MMAMAWA KAPENA POTURUKA DZUWA
James McGranahan
Doh is D

1. Mmamawa kapena poturuka dzuwa, Ambuye Yesuyo ’dzafika ndi mphamvu,
   Ndi ulemerero wokuru kutenga Anthu ace mu dzikoli.

   CHORUS:
   Yesu, Mbuye wathu, ’Dzayimba mokondwa liti?
   Kristu adza, Kristu adza, Aleluya amen. Aleluya amen.

2. Kapena usana kapena madzulo, Kapena usiku pamene Ambuye
   ’Dzafika mu ulemerero kutenga Anthu ace mu dzikoli.

3. Tidzakondwa ngati tidzanka osafa, Opanda kudwala, cisoni, maliro;
   Kungokhwathulidwa podzadza kutenga Anthu ace mu dzikoli.

No. 179
WAKONZEKA PAKUBWERA MKWATI?
R. E Hudson
Doh is A

1. Wakonzeka pakubwera Mkwatiyo, Mkwatiyo?
   Wakonzeka pakubwera Mkwatiyo, Mkwatiyo?
   Onani adza; onani adza; Konzeka akubwera Mkwatiyo.

   CHORUS:
   Onani Mkwati, Yesu abweratu! Onani Mkwati, Yesu abweratu!
   Yang'ana adza, yang'ana adza! Konzeka akubwera Mkwatiyo.

2. Konzetsani nyali zanu, adzatu, adzatu!
   Konzetsani nyali zanu, adzatu, adzatu!
   Akudza msanga; akudza msanga; Konzeka moyo wanga wonse 'we.

3. Tidzakomana naye, Mkwatiyo, Mkwatiyo!
   Tidzakomana naye, Mkwatiyo, Mkwatiyo!
   Adzadi Yesu; adzadi Yesu; Tidzakomana naye Mkwatiyo.

4. Tidzayimba mokondwera, Aleluya, kwa 'Ye;
   Tidzayimba mokondwera, Aleluya, kwa 'Ye.
   Yang'ana adza;yang'ana adza;  Yimbani, Aleluya adzatu.

No. 180
SITIDZIWA NTHAWI YA KUDZA
F.E Belden
Doh is C

1. Sitidziwa nthawi yakudza kwa Mbuye, Koma zooneka pa dziko zinena
   Adzabwera msanga, tikondwa, komatu Sitidziwa nthawi.

   CHORUS:
   Adzatu! Tikonzeke, lilinde! Adzatu! Aleluya! Aleluya!
   Adza ndi mphamvu za 'Tate wace, komatu Sitidziwa nthawi.

2. Ku'nika kulipo kwa anthu a nzeru, Co'nadi ciripo mu mau a Mlungu,
   Alembi anena momveka, komatu Sitidziwa nthawi.

3. Tilinde, tipemphe ndi nyali zowala, tigwirenso nchito mpakatu abwera.
   Poona zozizwa tiyimbe, komatu Sitidziwa nthawi.

No. 181
SITIDZIWA KUDZA KWA MBUYE
Will H. Pontius
Doh is E flat

1. Sitidziwa kudza kwa Mbuye, Madzulo kapena mmawa;
   Kapena nthawi ya usiku, Kapena m’mabinga kuca;
   Atiuzatu tikonzeke, Tisazime nyali zathu;
   Pobwera adzatipezetu, Tiri kumdikira Iye.

   CHORUS:
   Kudikiratu, Ndi kupemphera; Kucezeratu, Ndi kuyang’anira Inu.

   Alto, Tenor, ndi Bass:
   Kudikiratu ndi kupemphera, kudikiratu ndi kupemphera;
   Kucezeratu ndi kupemphera, Ndi kuyang’anira Inu.

2. Cikondi cace ncodabwitsa, Kutiombola ifetu;
   Anasiya malo oposa, Nadza kudzatiferatu;
   Nthawi zonse amakondwera, Mmene oomboledwawo;
   Akondwera m’ciyembekezo, Podikira Mbuye wao.

3. Inu Yesu, Mombolo wanga, Mudziwa ndikukondani,
   Ndiyembekeza kuniona, Ndidzamva mau anuwo;
   Mmene mudzadza kuweruza, Ena adzakuthawani,
   Koma ine ndidzakondwera, Ndiri kudikira Inu.

No. 182

MASOMPHENYA A TSIKULO

J. Graham, by per

Doh is G

1. Tsiku lowala liri pafupi; Yesu adzatu
   Kudzatenga ana Ace Kunka nao kwawoko.

   CHORUS:
   Tione masomphenya a tsikulo
   Limene liri kudza!
   Ndi uleme'ro wa tsikulo manda
   Adzatseguka.

2. Uthenga upite konse msanga, Kwa anthu onse;
   Pompo Mkwati adza posacedwa, Liu limveka.

3. Adzabwera ndi angelo onse, Mulemerero
   Woweruza natengera Ace, Komwe sadzafa.

4. Tidzakomana ndi okondedwa, Omwe adafa;
   Misonzi ya iwo akulira, Adzapukuta.

No. 183
ANALONJEZA AMBUYE WATHU
F.E Belden
Doh is G

1. Analonjeza Ambuye wathu, Ndibweranso msanga kulandira ‘nu.
   Gwiritsanitu coonadico, msagonenso tulo, dikiranitu.

   CHORUS:
   Gwiritsanitu coonadico, Apatsa inu ufumu wace.
   Lowani nonse m’cimwemwe canga; Korona alinda, gwiritsanibe.

2. Tidikiratu ndi nyali zathu, Adzadzanso monga usiku mbala.
   Timadziwanso wayandikadi, Komatu za tsiku sitidziwai.

3. Ciyembekezo ca mau ace, Kubwera kwa Yesu, Ambuye wathu.
   Ndi lonjezano lopambanadi, Abweradi msanga, gwiritsanibe.

No. 184
A M'DZIKO AKONDWERETU
George F. Handel
Doh is D

1. A m'dziko akondweretu, Ambuye adzanso.
   Mlandire Mfumu yathuyo Poyimba mokondwa,
   Poyimba mokondwa, Poyimbayimba mokondwa.

2. A m'dziko akondweretu, Adzalamula 'Ye.
   Ndi anthuwo ayimbetu Kutama Mbuyeyo,
   Kutama Mbuyeyo, Kutama Mbuye wathuyo.

3. Adzalamula mwa nsisi Mitundu yonseyo;
   Nawasonyeza onsewo Cikondi caceco
   Cikondi caceco, Cikondi cace Mbuyeyo.

No. 185
TINENA ZA DZIKO LIJA
Lewis Edson
Doh is G

1. Tinena za dziko lija, Lokoma ndi lowalalo;
Tinena ubwino wace, Tidzazizwa pofikako.
Tinena miseu yace, Makomanso a ngalewo;
Zokoma zosaneneka, Tidzazizwa pofikako.

2. Tinena zomasukatu  M'ucimo ndi m'mayesewo;
Kusiya mabvuto onse, Tidzazizwa pofikako.
Tinena cikondi cawo, Zobvala za oyerawo,
Za mpingo w onka mmwamba, Tidzazizwa pofikako.

3. Mukonze mu mtima mwanga, Ngakhale ndiyesedwatu,
Nanenso ndidziwe ndithu Khalidwe la kumwambako.
Pomwepo mu dziko lija, Lokoma ndi lowalalo,
'Dzayenda ndi angelowo, Ndi Yesu adzakhalako.

No. 186
TABWERA M’NMYUMBAYI
J.G Naegeli
Doh is F

1. Tabwera  m’nyumbayi, Pa maso panupo;
   Idzani, Mbuye, mkhaletu Pamodzi nafenso.

2. Mitima ythuyo Isowa Inudi;
   Tilakalaka Yesuyo Akhale m’moyomu.

3. Ndi Mzimu wanuyo Atithangatebe
   Kumvera mau anuwo, Tikhale anudi.

4. Muticotseretu Zoipa zathozo;
   Mukadzafika tsikulo, Mtitenge kwanuko.

No. 187
TIRI KUYIMBA NYIMBO YOMWEYI
E.J Hopkins
Doh is A flat

1. Tiri kuyimba nyimbo yomweyi, Yakuyamika Mbuye wathuyo,
   Mtendere wace titofunadi, Titapemphera tinke kwathuko.

2. Titanka kwathu, mkhale nafeko, Tikufunani, Yesu, Mbuyathu,
   Mutisungire nthawi zonsezo, Mutiyeretse m’mtima mwathu mbu!

3. Usiku uno mutisungedi, Khalani mfupi mnyumba mwathumo.
   Mamawanso mudzatidzutse nji! Kuti tigwire nchito zathuzo.

4. Mtitsogolere nthawi zonsezo, Kuyenda tokha sitikhozai.
   Ngati mukhala, Mbuye, mfupimo, Sitidzaopa kanthu kena bi.

No. 188
NKANA NDINACIMWADI
Spanish
Doh is A flat

1. Nkana ndinacimwadi, Yesu anafera ’ne.
   Anafera kutitu Ndikhale mmwambamo;
   Monga nthambi m’mpesamo Ndikhalatu mwacemo.

2. Ee, cikondi caceco, Ncacikurudi,
   Ciya ngati nyanjayo, Ndicotu cosathanso;
   Nandifunafuna ‘ne, Ndikali wocimwabe.

3. Nkana ndinacimwadi, Kristu akwaniratu;
   Ndi zosowa zangazo Azidziwa zonsezo;
   Andipulumutsa ‘ne, Andilimbikitsanso.

No. 189
TIRIBE MZINDA M'DZIKOLI
Unknown
Doh is G

1. Tiribe mzinda m'dzikoli Wolimba, wokhalitsanso;
   Komatu tikondwera 'fe, Tifuna mzinda udzawo,
   Tifuna mzinda udzawo.

2. Tiribe mzinda m'dzikoli, Wolimba, wokhalitsanso;
   Tifuna wina mmwambamo, Wowala ndi wosathanso,
   Wowala ndi wosathanso.

3. Ee, malo a mtenderewo Otopawo apumako!
   Ndikhala ndi mapikowo, Ndikadaulukirako,
   Ndikadaulukirako.

4. Tonthola moyo wanga 'we, Adziwa nthawi Mlunguyo;
   Ndicite nchito yaceyo, Apatsa 'ne mpumulowo,
   Apatsa 'ne mpumulowo.

No. 190
KONDA DZINA LA YESU
W.H Doane
Doh is A flat

1. Konda dzinalo la Yesu, Mwana wosauka ‘we,
   Ndilo lothandiza anthu, Khala nalo ponse phee.

   CHORUS:
   Dzina la Yesuyo, Lokondwetsa onsewo.
   Mwambamo, ponsepo, Litonthoza m’mtimamo.

2. Konda dzinalo la Yesu, M’moyo mwanu monsemo;
   Mmene mulikuyesedwa, Chula dzina lacelo.

3. Dzina ili ndi lokoma, La Mombolo wathuyo,
   Polandira ife mmwamba Tidzakondwererako.

4. Mbuye Yesu timtamanda. Ndi zinyimbo zathuzo;
   Mfumu ya mafumu onse, Yesu timayesadi.

No. 191
NDIDZIWITSITSA YESU NGWANGA
Mrs. Jos. F. Knapp, by per
Doh is D

1. Ndidziwitsitsa Yesu ngwanga; Tsiku ndi tsiku ndimakondwera.
   Anandigula ndi mwazi 'ce, Anandipatsa mzimu wace.

   CHORUS:
   Mau omwewo, nyimbo yomwe, Yesu ndimtama tsiku lonse.
   Mau omwewo, nyimbo yomwe, Yesu ndimtama tsiku lonse.

2. Nkamvera Yesu ndikondwatu, Ndiyang'anitsa Ambuyangayo
   Ndipo angelo atengera Ine cisomo ndi cumanso.

3. Ndine kapolo wa Mbuyanga, Andigwiritsa zinchito zace.
   Ndimyembekeza 'dzabweranso, Adzanditenga kwawo mmwamba.

No. 192
PA MTANDA POMWE NAFERAPO
Rev. J.H Stockton
Doh is A flat

1. Pa mtanda pomwe naferapo, Pomwe ndalira ndi chimolo,
   Anandipaka ndi mwaziwo, Tama dzinalo.

   CHORUS:
   Tama dzinalo, Tama dzinalo,
   Anandipaka ndi mwaziwo, Tama dzinalo.

2. Nandiombola mzoipazo, Yesu akhala mu mtimanga,
   Nandilandira pa mtandapo, Tama dzinalo.

3. Ndiye kasupe woyerayo! Ndikondwa kuti ndasambamo,
   Yesu watsukadi inenso, Tama dzinalo.

4. Idza kwa Yesu kasupeyo, Igwa pa mapazi acewo,
   Sambamo lero uyeretu. Tama dzinalo.

No. 193
KODI UNGAKHALE MOYO WONGA WACEWO?
Rev. Cyrus S. Nusbum
Doh is C

1. Kodi ungakhale moyo wonga wacewo? Kumayenda naye m'njira monsemo?
   Ungamlole Iye kunyamula nkhawazo? Mlole atsogole 'Ye.

   CHORUS:
   Mwa mphamvu yace udzakhala, Wakumasuka, inde, m'mwazi 'ce.
   Cikondi 'ce cidzaze mtimako. Poyenda nawe zidamkonda 'Ye.

2. Ungamlole kuti Iye amasule 'we? Kuti umutsate poitana 'Ye?
   Ungamlole kukucinjiriza Mbuyeyo? Mlole atsogole 'Ye.

3. Monga ukapeza malo mu ufumuwo? Ungamyese akusamalire 'we?
   Ungagwire nchito yace kopambanadi? Mlole atsogole 'Ye.

No. 194
PAKAKHALA CIKONDI
Arr. From  J.H McNaughton
Doh is A flat

1. Pakakhala cikondi, Banja likondwa; Pakakhala cimwemwe, Banja likondwa.
   Mtendere ukhalitse, Masiku awo onse; Akhala mu mtendere, Akakondana.

   CHORUS:
   Cikondi mbanjamo; Akhala mu mtendere, Akakondana.

2. M'nyumba muli cimwemwe, Akakondana; Mulibenso madano, Akakondana.
   Ana onse akondwa, Namveranso makolo; Moyo wao ukondwa, Akakondana.

3. Mulungu akondwera, Akakondana; Dziko lonse likoma, Akakondana.
   Zonse zowazingazo, Zimawakondweretsa; Mulungu akondwera, Akakondana.

4. Yesu mndilandire 'ne, Ndidzakondadi; Munandifera ine, Ndidzakondadi.
   Ndidzapumula ndithu, Wopanda nkhawa konse; Mwa cifundo canuco, Ndidzakondwadi.

No. 195
TIFUNA MZIMU WANUYO
German
Doh is B flat

1. Tifuna mzimu wanuyo, Yemwe nawala kalelo;
   Nawatenthetsa m'mtimamo, Nawalimbitsa mzo'psamo.

2. Mzimuyo ali kuti ko, Nadzazayo Abramuyo?
   Namsintha mtima Paulo, Yemwe nampatsa canguco?

3. Yemwenso kalekalelo Nanena za cikondico,
   Nawala pa Yesayayo, Nampatsa Daniel nzeruzo.

4. Kodi mulibe mphamvuzo Monga Eliya nazimva?
   Mose nawala nkhopeyo, Yobu anapiriranso?

5. Mcitetu monga kalelo, Dzutsani nchito yanuyo.
   Mmene tipempha kwanuko, Mtitsanulire Mzimuyo.

No. 196
UFUNA KUOMBOLEDWA KODI?
L.E Jones
Doh is B flat

1. Ufuna kuomboledwa kodi? Iripo mphamvu m’mwazi wace;
   Ufuna kugonjetsa zoipa? Muli mphamvu m’mwazi wace.

   CHORUS:
   Muli mphamvu (m’mwazi) yozizwitsatu, M’mwazi wa Yesuyo;
   Muli mphamvu (m’mwazi) yozizwitsatu, M’mwazi wa mwana wa nkhosa.

2. Ufuna kuleka kunyadako? Iripo mphamvu m’mwazi wace;
   Idzatu pa mtanda nutsikidwe, Muli mphamvu m’mwazi wace.

3. Ufuna kuyera kopambana? Iripo mphmvu m’mwazi wace;
   Zoipa zonse adzayeretsa, Muli mphamvu m’mwazi wace.

4. Ufuna kugwira nchito yace? Iripo mphamvu m’mwazi wace;
   Ufuna kumuyimbira Iye? Muli mphamvu m’mwazi wace.

No. 197
MDIMAWO KULIBE
Ira D Sankey
Doh is F

1. Mdimawo kulibe akadza ‘Ye, Mdimawo kulibe akadza ‘Ye,
   Mdimawo kulibe akadza ‘Ye, Kutenga ‘nthu acewo.

   CHORUS:
   Kutenga ‘nthu cewo (ace), Kutenga ‘nthu acewo(ace);
   Mdimawo kulibe akadza ‘Ye, Kutenga ‘nthu acewo.

2. Imfayo kulibe akadza ‘Ye, Imfayo kulibe akadza ‘Ye;
   Tidzakondweratu akadza ‘Y, Kutenga ‘nthu acewo.

3. Msoziwo kulibe akadza ‘Ye, Msoziwo kulibe akadza ‘Ye;
   Adzasonkha onse akadza ‘Ye, Kutenga ‘nthu acewo.

4. Tidzayimba nyimbo akadza ‘Ye, Tidzayimba nyimbo akadza ‘Ye;
   Onse ‘dzasonkhana akadza ‘Ye, Kutenga ‘nthu acewo.

No. 198
BWENZI LABWINO NDILO YESU
P.P Bithorn
Doh is G

1. Bwenzi labwino ndilo Yesu, Mmene mubvitidwa m'dzikoli;
   Alimbitsa mtimamo, Atipatsa mphamvunso,
   Bwenzi labwino ndilo Yesu.

   CHORUS:
   Kulibe woposa Yesu (Yesuyo), Kulibe woposa Yesu (Yesuyo);
   Pogwa athangatadi, Poitana 'dzamvatu;
   Bwenzi labwino ndilo Yesu.

2. Ndinapezatu bwenzi Yesu, Atonthoza moyo wangawu,
   Mmene ndimtsamira 'Ye, Sin'dzaopa mdaniyo,
   Bwenzi labwino ndilo Yesu.

3. Pakuyenda usiku wo'psa Wa cisoni ndi wa imfayo,
   Sindiopa konse bi, Yesu ap'lumutsadi,
   Bwenzi labwino ndilo Yesu.

4. Podzafika kumwamba konko, Tonse okhulupirika 'fe,
   Inde,tidziyimbadi kumtamanda Iyeyo,
   Bwenzi labwino ndilo Yesu.

No. 199
ULEMU KWA MULUNGU
W.H Doane
Doh is A flat

1. Ulemu kwa Mlungu, Ambuye wathu, Akonda, napatsa ’fe Mwana wace;
   Napatsatu moyo kuombola ’fe, Pa khomo la moyo natsegulatu.

   CHORUS:
   Tamani Mbuyeyo, Dziko limvere ’Ye; Tamani Mbuyeyo, Anthu akondwetu;
   Idzani kwa ’Tate mwa Mwana wace, Mpatseni ulemu anakonda ’fe.

2. Anapulumutsa ndi mwazi wace Amene akhulupirira mwa ’Ye.
   Ngakhale wocimwa koposa ndithu, Adzakhulukidwa mwa Yesuyo.

3. Anatiphunzitsa zopambanazo, Tikondwa mwa Yesu, Ambuye wathu;
   Komabe ’dzazizwa kopambanadi, Pamene atenga ’fe kumwambako.

No. 200

NDINU WAKUYERA!

John B. Dykes

Doh is E

1. Ndinu wakuyera! Wa mphamvu zonse,
   Nthawi ya mmamawa tiyimba nyimboyi;
   Mlengi wacifundo tikuyamikani,
   Ee, Mlungu mmodzi mwa Atatuwo.

2. Ndinu wakuyera! Onse pa dziko
   Akuyimbirani nakupempherani;
   Akumwamba omwe nagwadira Inu,
   Wa cikhalire ndi wosafai.

3. Ndinu wakuyera! Ife ocimwa,
   Ulemero wanu sitimaona bi!
   Mwayeradi nokha, wina saoneka;
   Wangwiro m’mphamvu ndi m’kuyeramo.

No. 201
ANANDIBVUULA
H.L Gilmour
Doh is E flat

1. Mtima wanga unaopa Yehova,
   Ntakanikizidwa pansi ndi cimo;
   Ndamulirira Ambuye m'thopemo,
   Anandibvuulamo mwa cifundo.

   CHORUS:
   Anandibvuula m'matope,
   Nandikhazikitsa pa thanthwe
   Moyo wanga lero uyimba,
   Matamando Haleluya.

2. Wandikhazika pa thanthwe lolimba,
   Ndakhazikitsidwa sindicokapo;
   Pano palibe coopsya ndakhala,
   Cisomo cidzandibveka korona.

3. Wandipatsa nyimbo ya mayamiko,
   Msana ndi usiku ndidzayimba;
   Mtimawu useka ndi ufulu,
   Ndikutamandani Mombolo wanga.

4. Ndidzayimba nsisi mwandichitira,
   Ndzalimbika mpaka onse amdziwe;
   Cipulumutso ndzayimba konseko,
   Kuti ambiri amvere Mulungu.

No. 202
YESU TSOGOLERENI
John E. Gould
Doh is B flat

1. Yesu tsogolereni, Pa ulendo woopsya;
   Zobvuto zosatheka; Ziri m’tsogolo mwanga,
   Inu zonse mudziwa, Yesu tsogolereni.

2. Monga mai acita Naye mwana polira,
   Muletse zobvutazo; Nditonthozedwe ine,
   Ndinu Mfumu ya luntha; Yesu tsogolereni.

3. Pakutha pa dzikoli, Zoopsya zidzakula;
   Pokhapokha pa Inu, Ndidzapeza mpumulo,
   Ndidzamva mau aja ”Msaope nditsogola.”

No. 203
NKHOSWE YADZA
William J. Kirkpatrick
Doh is C

1. Lalikira mau Konse kuli anthu,
   A mtima wosowa A m’dziko latsoka,
   Mkristu ali yense Anene mokondwa:
   Nkhoswe yafikadi!

   CHORUS:
   Nkhoswe yafikadi, Nkhoswe yafikadi!
   Mzimu wa Mulungu Pangano la Mbuye;
   Lalikira mau Konse kuli anthu,
   Nkhoswe yafikadi!

2. Usiku wapita, Kunja nako kwaca;
   Kulira kwaleka, Ndi mkwiyo naonse,
   Pamapiri napo Dzuwa lioneka;
   Nkhoswe yafikadi!

3. Mfumu ya mafumu Ibwera ndi mwayi,
   Kwa ocimwa onse Kudzapulumutsa;
   M’malomo mwa cete Mumvekera nyimbo
   Nkhoswe yafikadi!

4. Cikondi cakuya! Ndicinene bwanji,
   Kwa anthu ocimwa Apeze cisomo,
   Wocimwa ngati’ne Ndingawale bwanji;
   Nkhoswe yafikadi!

5. Kuyimba kumveke Mlengalenga monse,
   Oyera a m’mwamba Ndi a pansi pano
   Abvomerezane Nyimbo yacikondi,
   Nkhoswe yafikadi!

No. 204
BWERA WOSOCERA! BWERA!
Ira D Sankey
Doh is F

1. M’dziko la alendo, Komwe ukhala,
   Imva kuitana, ”Mwana wanga!”

   CHORUS:
   ”Bwera wosocera! Bwerera kwanu!
   Wasocera kutari; Bwera kwanu!”

2. Ku dziko la njala, Wokomokawe,
   Idza ukondedwe, ”Mwana wanga!”

3. Siya zandeuzo Coka m’matsoka,
   Watopa mumtima, ”Mwana wanga!”

4. Khomo ndotsehuka! Ndiwe wangabe;
   Ndikuyang’anabe, ”Mwana wanga!”.

5. Wasocereratu; Subwera kodi?
   Wakhululukidwa, ”Mwana wanga!”

6. Gome lilindira, Suiwalika!
   Udzadye upume, ”Mwana wanga!”

7. Wopanda kwanu’we, Wopereweza,
   Ndikukonda iwe, ”Mwana wanga!”

No. 205
YESU PONONG'ONEZA
Horatio R. Palmer
Doh is F.

1. Yesu ponong'oneza, idzanitu, Mupempherera ife, idzanitu;
   Njabwino nthawi ino, idzanitu, Yomdziwa Mpulumutsi, idzanitu.

2. Tulani zoipazo, idzanitu; Yesu adzatha zonse, idzanitu;
   Olema ndi ocimwa, idzanitu, Sakumbukira izo, idzanitu.

3. Imvani mau ace, idzanitu; Mudzalandira dalo, idzanitu;
   Naco cisomo cace, idzanitu, Yesu alinda inu, idzanitu.

4. Mverani Iye ati, idzanitu; Tiyeni mudzamona, idzanitu.
   Ee! Akuitanabe, idzanitu, Ife tibvomereza, tibweratu.

No. 206
NDINAKUFERATU, WACITANJI ‘WE?
J.E White
Doh is B flat

1. Ndinakufera ‘we, ndakhetsa mwaziwo,
   Kupulumutsa ‘we kucoka mwimfayo.
   Ndapatsa moyo wangawo, wapatsa Inenji?
   Ndapatsa moyo wangawo, wapatsa Inenji?

2. Ndasiya mwambamo, ulemererowo,
   Ndinadza m’dzikomu mwa mdima wokhawo.
   Ndasiya zonse zabwino, wasiya c’ani ‘we?
   Ndasiya zonse zabwino, wasiya c’ani ‘we?

3. Ndinazunzidwa ‘ne, kosanenekatu,
   Ndasautsidwa ‘ne, populumutsa ‘we.
   Ndinapirira zonsezi, wapiriranji ‘we?
   Ndinapirira zonsezi, wapiriranji ‘we?

No. 207
CIKHULULUKIRO COONA
Arr. By Henry W. Greatorex
Doh is G

1. Ndinaona pamtandapo,
   Wothatha ndi mwazi,
   Ali kundiyang'anitsa,
   Pafupi ndi mtanda.

2. Sinditha kuiwalira
   Zomwe ndinaona;
   Ngati ndine ndinamupha,
   Zidziwika zokha.

3. Anandiyang'anitsanso,
   Ngati kundiuza
   Imfa yino, mwazi uno,
   Zikupulumutsa.

4. Chimo langa linamupha,
   Loda ngati mdima,
   Cinsisi ca cisomoco,
   Cakhululukira.

No. 208
USAMANONG’ONA
W.H Doane
Doh is B flat

1. Usamanang’ona M’kacisi muno!
   Udzikhala cete, Kumvetseratu.

   CHORUS:
   Nyang’ama (tu), Nyang’ama (tu),
   Poyenda muno
   Popeza (tu), m’nyumba (tu)
   Ya Mlungu wathu.

2. Udzikhala cete malo ano
   Cifukwa Ambuye aona iwe.

3. Udzidzicepetsa popempherapo;
   Cifukwa Ambuye amvera iwe.

4. Ganiza zabwino za Mlungu wathu,
   Dikira, numvere uthenga wace.

No. 209
NTAYENDA NANU
Henry W. Greatorex's "collection"
Doh is G

1. Ntayenda nanu Mulungu!
   Ngati a Kumwamba,
   Ntaunikidwa panjira,
   Yofitsa kwa Yesu.

2. Mzimu Woyera bwerani,
   Mthenga wa mpumulo;
   Ndidana nazo zoipa,
   Zotilekanitsa.

3. Ndinakondwa nthawi ija!
   Sindingaiwaile,
   Ndatsala m'zobvuta zokha,
   Dziko ndi lacabe.

4. Fano ndinalikondalo,
   Kaya ndi lotani,
   Thangateni kulicotsa,
   Nditsale ndi Inu.

No. 210
MOMBOLO WOZIZWITSA
Elisha A. Hoffman
Doh is D

1. Kristu nsembe ya ocimwa, Mombolo wozizwitsa!
   Taomboledwa ndi mwazi, Mombolo wozizwitsa!

   CHORUS:
   Mombolo wozizwitsa Ndiye Yesu wanga!
   Mombolo wozizwitsa Ndi Yesu Mbuye.

2. Nditama mwazi wacewo, Mombolo wozizwitsa!
   Wandifitsa kwa Mulungu, Mombolo wozizwitsa!

3. Wanditsuka chimo lonse, Mombolo wozizwitsa!
   Mfumu ndiye m’kati mwanga, Mombolo wozizwitsa!

4. Ndiri naye m’njira monse, Mombolo wozizwitsa!
   An’sunga tsiku ndi tsiku, Mombolo wozizwitsa!

5. Andipatsa cigonjetso, Mombolo wozizwitsa!
   Ndi m’mayeso cipambano, Mombolo wozizwitsa!

6. Ndampatsa mtima wonsewu, Mombolo wozizwitsa!
   Dziko silingathandize; Mombolo wozizwitsa!

No. 211
MADALITSO NGATI MVULA
James McGranahan
Doh is B flat

1. “ Madalitso ngati mbvumbi;” Pangano la cikondi;
   Nyengo yakupata mphamvu, Yocokera kumwamba.

   CHORUS:
   Tipempha Inu Mvula ya madalitso;
   Nsisi zitigwere ife, Tipempha madalitso.

   Alto, Tenor and Bass:
   Mvula tipempha Inu, Mvula ya madalitso,
   Nsisi zitigwere ife, Tipempha madalitso.

2. “Madalitso ngati mbvumbi: “Titsitsimutseninso;
   M’mapiri ndi m’madombonso, Mvula ya citsitsimutso.

3. “Madalito ngati Mbvumbi:” Tipatsenitu Mbuye;
   Mtitsitsimutse tsopano, Tiope Mau anu.

4. ”Madalitso ngati mbvumbi:” Mbvumbiwo ugwe lero,
   Tilandirenso Mbuye, Yesu musatitaye!

No. 212
NDIYIMBA MU MTIMA MOKONDWA
P.P Bilhorn
Doh is A

1. Ndiyimba mu mtima mokondwa! Ndi nyimbo yokoma, yoyera;
   Ndiyimba za Yesu Mbuyanga, Anditonthozane phe!

   CHORUS:
   Cete! Cete! M'mtima mtenderemu phe;
   Udzera kwa Yesu wokonda, Mtendere mu mtimamu.

2. Pa mtanda Mbuyanga nafera, Adandicotsera zocimwa;
   Anandigulira mtendere, Anditonthozane phe!

3. Pomsankha Yesuyo Mbuyanga, Mtendere walowa mu mtima;
   Ndapeza dalitso loposa, Anditonthozane phe!

4. Pokonda Yesuyo, mtendere, Ku nthawi zosatha mtendere;
   Potsata Mbuyanga apatsa, Mtendere mu mtimamu.

No. 213
NYIMBO YANGA
D.S Hakes
Doh is G

1. Yesu Mombolo wanga, Ndinu nyimbo yanga,
   Mpulumutsi wabwino, Ndikamabvutika.

   CHORUS:
   Yesu Mombolo wanga, Mdiyimbira Inu;
   Palibe bwenzi lina, Ndikondana nalo.

2. Ndiyembekezera'nu, Mwa zaka zonsezi,
   Ndikapanikizidwa, Polira misonzi.

3. Inu nokha Mbuyanga, Bwenzi ndi mtsogozi,
   Ndikondetsa Inutu, Kuposa za dziko.

4. Msangalatsi ndi Inu, M'dziko la ucimo,
   Ndikuganizani'nu M'zipata za m'Mwamba.

No. 214

KODI YESU ASAMALA?

J.Lincoln Hall

Doh is D flat

1. Kodi Yesu asamalira
   Nkasowa cimwemwe;
   Ndikapsinjika ndi kuda nkhawa,
   M'njira yonse yaitari?

   CHORUS:
   Ndidziwa amasamala, Inde ndikabvutika;
   Ndithu masana ndi usiku Amandisamalirane.

2. Kodi Yesu asamalitsa
   Mu'siku woopsa,
   Pamene kwada zoopsa zadza,
   Andisamalabe kodi?

3. Kodi Yesu asamalitsa
   Ndikagwa m'mayeso?
   Mwa za cisoni zosapumitsa,
   Misonzi usiku wonse?

4. Kodi Yesu asamalitsa
   Poleka za dziko,
   Ndiri kuthatha pafupi kufa,
   Kodi akundionadi?

No. 215
LINDA USADANDAULE
William J. Kirkpatrick
Doh is C

1. Kwathu kosasinthikako, Ndi masautso kulibe;
   Inde kwathu kowalako, Kodi sudzapumulako?

   CHORUS:
   Linda, usadandauletu, Linda usadandauletu;
   Linda, Linda! Usadandauletu.

2. Walemedwa ndi katundu, Wa zinthu za dziko lino,
   Tsiku lopuma lidzadza (fatsa usadandaule).

3. M’njira muli minga kodi, Iye anabvala minga;
   Wapeza cisoni kodi, Iye cinamgwera kale.

4. Gwira nchito upirire, Ngakhale umanyozeka;
   Tsiku lopuma lifika, Linda usadandaule.

No. 216
SINDIRI NDEKHA
J.C.H and V.A White
Doh is C

1. Ndekha? Bi, sindiri ndekha Yesu ngwanga;
   Amandisangalatsa; Ali pafupipa,
   Ulibe bwenzi ko, Ndiri naye Yesu;
   Ndimasinthasinthadi, Iye sasinthatu.

   CHORUS:
   Sindiri ndekha, sindiri ndekha;
   Anapangana nane kuti sadzandisiya ndekha.

2. Kutopa? Nditoperenji, Yesu ngwanga;
   Ndatsamira pa Iye, Ndiri kupumula,
   Wosowae; inde ndatsamira zedi,
   Pa dzanja lace Yesu phe Andisamalira.

3. Kulindira? Inde, ndiri kulindira;
   Kaya acedweranji Ambuye kubwera,
   Ndiye ukukondwa? Inde, kukondwadi;
   Ndikondwa ndi maziko ndiye Ambuyanga.

No. 217
CINTHU CINA KWA YESU
Robert Lowry
Doh is G

1. Mbuye! Cikondico ’natifera,
   Cosandiyenera, ndidza kwanu;
   Ndidziperekatu mphatso zanga zonse,
   Sindidzamanatu ciri conse.

2. Wondipembedzera ndinu nokha,
   Ndiyembekezera pa Inutu;
   Senzeni mtandawo ndiuze cikondi
   Kuti ndingacite cinthu cina.

3. Zonse ndiri nazo nzolandira
   Monga masikuwa’ kupita,
   Nchito yacikondi yayambidwa kale,
   Otaika ena tikabweze.

4. Zonse ndiri nazo mwandipatsa,
   Ndipatsa kwa Inu Ambuyanga
   Nditafika m’mwamba moyo wanga ngwanu,
   Cinthu cina ncanu nthawi zonse.

No. 218
MAZIKO AMODZI
Samuel S. Wesley
Doh is E flat

1. Maziko a mpingo amodzi ndi Kristu;
   Colenga catsopano, mwa madzi ndi mau;
   Anatsika kumwamba nalenga mpingowo:
   Naugul ndi mwazi naufera mpingo.

2. Wokwanira mitundu yonse ya pa dziko;
   Koma cipulumutso mwa njira imodzi,
   Dzinali loyeretsa lapanga mpingowu,
   Cogawira cimodzi cisomo coyera.

3. Ponyoza mpingo wace anthu adzaona,
   Adani apasula Thanthwe sadzalitha;
   Oyerawo osunga cikhulupiriro:
   Cisoni cikadzatha, tidzakondwerera.

4. M’kati mwa masauko a mpingo woyera;
   Mpingo ulindirira cipulumutsoco;
   Maso otopa nako kulira kukwera;
   Mpingo waukuruwo udzagonjetsadi.

No. 219
MUNDITSOGOLERE YEHOVA
Thomas Hastings
Doh is A

1. Mbuye nditsogolereni,
   Ndine mlendo m'dzikoli;
   Ndalefuka nditengeni
   Mundisunge m'manjamo.
   Mundidyetse, mundudyetse,
   Mundidyetse, Kufikira ndikhute.

2. Mundimwetse madzi anu Andicize nthendazi,
   Utsogole mtambo wanu, Ndikafike komweko,
   Wamphamvun'u wamphamvunu,
   Wamphamvun'u, Khalani mphamvu yanga.

3. Ntaponda gombe la Yordan, Mantha mundicotsere;
   Ndioloke tsidya ilo, Komwe kuli cimwemwe.
   Nkayimbira, nkayimbira,
   Nkayimbira, Nkatamande kosatha.

No. 220
KWATHU
George C. Stebbins
Doh is F

1. Ndilakalaka kwathu! Dziko laufulu!
   Kwathu kopanda mdima, Kulibe usiku;
   Ndiri kulira kwathu, Mtima suli bwino;
   Kulibe zowawa kwathu, Ndayandikirako;
   Kulibe zowawa kwathu, Ndayandikirako.

2. Mbuyanga ali kwathu, Angelo abwino;
   Kulibe chimo kwathu, Mayeso kulibe;
   Nyimbozo za kwathuko Ndiri kuzimvatu
   Ndikaganiza za kwathu Ndilira misonzi.
   Ndikaganiza za kwathu Ndilira misonzi.

3. Anthu okhala kwathu Andikodolane,
   Kopanda zacisoni Kwa okhala mommo;
   Kokomadi kwathuko! Kwa mtendere uko!
   Kristu atifitsa kwathu Mwini wotikonda;
   Kristu atifitsa kwathu Mwini wotikonda.

No. 221
ZOKUMBUTSA GALILEYA
Dr. H.R. Palmer
Doh is B flat

1. Ndamva nkhunda….Ndi nthambinso….,
   Zimamveka….pa madzulo…,
   Zindiuza…umulungu,
   Zinkumbutsa…Galileya…

   CHORUS:
   Galileya Wokoma'we
   Komwe Yesu 'nakhalitsa,
   Galileya Wakuyawe,
   Idza udzandiyimbire.

2. Mwa madambo… Muli ndere…
   Mbalamenso… Ziyimbira…
   M'mawamaw… Ziyamika…
   Mokwanira… M'galileya…

3. Nkawerenga… Zozizwazo…
   Za woyenda… Pa nyanjayo…
   Ndifunadi… Kopambana,
   Kumtsata'Ye… M'galileya…

No. 222
M’MANJA A YESU WANGA
W.H Doane
Doh is G

1. M’manja a Yesu wanga ndiri kugonamo,
   Mommo aphimba ine naco cikondico.
   Mvera! Mudzera mmwamba mau a Yesu wanga,
   “Mwana ndikusungira pano pa mtima panga.”

   CHORUS:
   M’manja a Yesu wanga ndiri kugonamo,
   Mommo aphimba ine naco cikondico.

2. M’manja a Yesu wanga nkhawa zonsezo zi!
   Momwe zoipa zanga sizindibvuta bi.
   Mommo mulibe nsoni, mommo mokoma monse,
   Sindiliramo msozi, nkondwa ndi mtima wonse.

3. Mtima umabisala m’manja mwa Yesumo,
   Mbuye musunge ine, ndikhulupira ‘Nu.
   Mommo wa cete ine mpaka wacoka mdima,
   Tsono ndiona komwe Yesu wokoma mtima.

No. 223
NDIDZATSATA KONSEKO
Arr.by Ira Orwig Hoffman
Doh is G

1. Ndimva Mpulumutsi wanga, Mwa cifundo andi'tana;
   Ndimva mau ace ati, "Unditsate-tsate konseko.

   CHORUS:
   Ndidzasenza mtand wanga,
   Kutsatira Mpulumutsi;
   Komwe anditsogolera,
   Ndinke naye, naye, konseko.

2. Njira ide mdima bwanji, Mapazi atope bwanji;
   Mtimawu 'dzalimbikira, Pakumtsata-tsata konseko.

3. Yesu atsogolerabe, Wondiunikira m'Mwamba,
   Nkafoka andilimbitsa, Pakumtsata-tsata konseko.

4. Mobvuta antsogolera, Ndidya mana a Kumwamba;
   Ambuye ndikusowani, Pakumtsata-tsata konseko.

5. Mwandilera ndi cikondi, Mundifungate dzolimba,
   M'cisomo canu mndisunge, Pakumtsata-tsata konseko.

No. 224
NYALI YANU IWALIRE
P.P Bliss
Doh is B flat

1. ’Tate wathu wa Kumwamba, ’natipatsa nyali’Ce,
   Koma atiuza ife, Tiwalire enawo.

   CHORUS:
   Nyali yanu iwalire, Kusonyeza njirayo,
   Kwa ocimwa ndi ofo’ka, Njira yonka m’Mwambamo.

2. Kuli mdima m’dziko lino, Ndi namondwe wa bvuto,
   Obvutika alindira Nyali yotsogozayo.

3. Konza nyali yako msang, Pena wobvutikayo
   Atayidwatu mu mdima, Akapanda nyaliyo.

No. 225
UYANG’ANE MDANIYO
W.B. Bradbury and Philip Philipps
Doh is A flat

1. Mkristuwe dzuka! Alamula Mbuye;
   Tenga cikopa, Ndi lupanga m’dzanja,
   Ukomane naye, usamuope
   Ulimbe mtima, Myang’ane mdaniyo.

   CHORUS:
   Limba mtima, Limba mtima,
   Limba mtima Pom’yang’ana mdani.

2. Zoopsa ziripo, ucenjeretu,
   Usafulatire, ungapwetekwe;
   Unyinji wa ‘dani, udzagonjetsa,
   Ulimbe mtima, M’yang’ane mdaniyo.

3. Nchito ya Mbuyako uiteteze;
   Dzukatu mwa cangu nkhondoyo ithe;
   Akakulamula, pita mwa cangu,
   Ulimbe mtima M’yang’ane mdaniyo.

4. Pita limbikira, suli wekhai,
   Mwayi apatsa, cisangalatsonso;
   Mwayi apatsa, cisangalatsonso;
   Cikondi cace ngati mtsinje m’thengo;
   Ulimbe mtima M’yang’ane mdaniyo.

No. 226
PAFUPI KUKOPEKA
P.P. Bliss
Doh is G

1. Pang'onong'ono kukopedwa;
   Pang'onong'ono kumlandira,
   Wina akutero, " Pita, Mzimu, pita,
   Ndikaona nthawi n'kuitana."

2. Pang'onong'ono, lero idza;
   Pang'onog'ono usalubze,
   Yesu akwitana, angelo mpafupi,
   Anthu akupempha, Bweranitu..

3. Pang'onong'ono mwayi watha;
   Pang'onong'ono tsoka ladza!
   Kucedwa simwayi, ndi tsoka loops,
   Ha, adzaliradi, "Ndacedwatu!"

No. 227
PA MTANDA
R.E Hudson
Doh is E

1. Ambuye mwazi nakhetsa, Mfumu yanga nifa,
   Naperekera mutuwo Mbozi ngati ine!

   CHORUS:
   Pa mtanda, pa mtanda ndaona kuwala,
   Colemetsa mtimanga cacoka;
   Mwa cikhulupiriro ndiona,
   Ndikondwerera kosaleka.

2. Anabuula pa mtengo, Ndi zoipa zanga;
   Kuya cisomo citere, Cikondi cakuya!

3. Nzosatheka kubwezera Cikondi cotere;
   Ndingodzipereka Mbuye, Zokhazo ndicita.

No. 228
MUYAMIKENI YESU
Chester G. Allen
Doh is A flat

1. Myamikeni! Yesu wodala Mombolo!
   Yimba cikondi cozizwitsaci!
   Mkondwereni mkuru wa angelo m'Mwamba,
   Dzina lace lilemekezedwe!
   Monga mbusa yesu asunga ana,
   M'mikono mwace awanyamula.

   CHORUS:
   Myamikeni! Ali wamkuru koposa;
   Myamikeni m'nyimbo zokondwera.

2. Myamikeni! Yesu wodala Mombolo!
   Zathu zocimwa nathira mwazi;
   Ndiye Thanthwe lathu la cipulumutso,
   Myamikeni Yesu wopacikwa;
   Mbukitseni! Yesu wotithangata,
   Cikondi cosamariza ncace.

3. Myamikeni! Yesu wodala Mombolo!
   Khomo m'mwamba mumveka hosana!
   Yesu Mbuye alera nthawi zosatha;
   Mbveke krona Wansembe ndi Mfumu!
   Kristu adza wogonjetsa dzikoli,
   Mphamvu ndi ulemu ndi za Yesu.

No. 229
WA YESUYO NDANI?
F.E Belden
Doh is G

1. Wa yesuyo ndani? Ngoona;
   Mbali ndi ziwiri; Usankhe.

CHORUS:
Sankha, sankha, (Wa Yesuyo ndani? Wa Yesuyo ndani?)
Yabwino, yoip? Uankhe,
Sankha, sankha,
Yabwino, yoipa? Usankhe.

2. Ambiri asankha Yoipa;
   Yosalimba ndi ya mabodza.

3. Gwirizana naye Anbuye,
   Ndiyo mbali yokha Yolimba.

No. 230
NDINE NJIRA
James McGranahan
Doh is E flat

1. Monga nkhosa zotayika, Zomwazika konse;
   Zasiya moyo, mtendere, Njira yandisowa?

   CHORUS:

Sop. & alto: ndine njira, co'nadi, moyo,
Sungafike Atate koma mwa Ine,
Ndine njira, co'nadi, moyo,
Sungafike Atate koma mwa Ine.

Bass & Ten: ndine njira, ndine njira, ndine njira co'nadi, moyo
Sungafike Atate koma mwa Ine,
Ndine njira, ndine njira, ndine njira co'nadi, moyo
Sungafike Atate koma mwa Ine.

2. Nkhawa zandisokoneza, Mulungu ndifuna;
   Manena-nena ngambiri, Ndingagwire ziti?

3. Kwa Kristu, njira, co'nadi Ndi moyo ndibweranso;
   Adzandifitsa kwa 'Tate, Kumalo kosatha.

No. 231
LOWETSA YESU MU MTIMA
Mrs. C.H Morris
Doh is A flat

1. Kodi watopa nazo zoipa, Lowetsa Yesu mu mtima;
   Ngati ufuna kutembenuka, Lowetsa Yesu mu mtima.

   CHORUS:
   Leka kukayikaku; usamkanenso lero,
   Tsegula mtima wako; Lowetsa Yesu mu mtim.

2. Ukafuna kukhala woyer, Lowetsa Yesu mumtima;
   Madzi osamba ali pafupi, Lowetsa Yesu mu mtima.

3. Ngati muli bvuto mu mtimamo, Lowetsa Yesu mu mtima;
   Ngati wapereweza za m'dziko, Lowetsa Yesu mu mtima.

4. Abwenzi akakusndukira, Lowetsa Yesu mu mtima;
   Ndiye bwenzi losatekeseka, lowetsa Yesu mu mtima.

5. Ngati uyimba nao odala, Lowetsa Yesu mu mtima;
   Udzalowe m'nyumba za mpumulo, Lowetsa Yesu mu mtima.

   CHORUS (wotsiriza):
   Leka kukayikaku; Usamkanenso lero,
   Ndatsegula citseko, Kuti Yesu alowemo.

No. 232
SINDIDZAKUSIYA
Unknown
Doh is E flat

1. Sindidzakusiya konse, Sindidzakukananso;
   Ndzatsogola ndzakusunga, Mogwa mwa dzina langa;
   Musaope coipaco, Pomvera malangizo.

2. Mphepo zikaomba mkuntho, Upemphere kwa Ine;
   Ndidzakufungata iwe, Kukusamala bwino;
   Poyesedwa konyazitsa, Ndidzakuyendetsa bwino.

3. Mlengalenga pong'azima Pakakoma ponsepo,
   Madyerero osasowa, Zokondweretsa zokha;
   Ndidzakhala nawe ndithu, Ndi kuti usacimwe.

4. Ngati ndadodometsedwa, Ndi nkhawa ndi cisoni,
   Ngakhaletu kuli nkhungu, Ndidzakuunikira,
   Mbendera yokwezekayi, Ya cikondi canga njo.

No. 233
UZENI NTHANDO YAKALE
William H. Doane
Doh is C

1. Uze nthando yakale, Ya za kumwambako,
   Za Yesu wacifundo, Za Yesu wokonda;
   Pang'ono pang'onotu, Monga kwa kamwana,
   Poti ndiri wotopa, Wopanda thandizo.

   CHORUS:
   Nthano yakale uze, Nthano yakale uze,
   Nthano yakale uze, Ya Yesu Wokonda.

2. Pang'ono ndi pang'ono, Motsimikizadi;
   Pakuti ndaipadi, Yesu nandifera;
   Nthano yonseyo uze, Musacite mphwayi,
   M'nthawi yonse ya bvuto, Andisangalatsa.

3. Nenatu yomwe ija, Ukhala ndi mantha,
   Kuti dziko loipa, Ndilikondetsetsa;
   Ulemu wa dzikowu Uyamba m'moyomu,
   Uze nthano yakale; Yesu akuciza.

No. 234

# YESU NYALI YA DZIKO

Geo. D. Elderkkin, arr

Doh is F

1. Ha! Nayimba angelo, Yesu nyali ya dziko;
   Mwana wabadwa Mfumu, Yesu nyali ya dziko.

   CHORUS:
   Yenda m'kunika kwabwinoko,
   Idza kumene kuli cifundo,
   Kuwala kwa msana ndi usiku:
   Yesu, nyali ya dziko.

2. Mapfukonu kondwani, Yesu nyali ya dziko;
   Kondwani ndi a m'mwamba, Yesu nyali ya dziko.

3. M'mwamba amlemekeza, Yesu nyali ya dziko;
   Yesu Mbuye wosatha, Yesu nyali ya dziko.

4. Mfumu ya mtenderedi, Yesu nyali ya dziko;
   Dzuwa la cilungamo, Yesu nyali ya dziko.

No. 235
LADZANSO TSIKU LAKUPUMULA
Unknown
Doh is E flat

1. Ladzanso tsiku lakupumula,
   Lodalitsidwa ndi Mulunguyo;
   Iye napuma nchito zacezo,
   Ndipo afuna tipumulenso.

2. Tiyeni tonse pa Sabatali,
   Timveretu kufuna kwaceko;
   Tsono poyimba ndi kupemphera,
   Iye adzakondwera nafetu.

3. Mbuye, muchere khutu lanulo,
   Mumve pemphero la tiana ’fe;
   Kumbukirani lonjezanolo,
   Mupulumutse otaikawo.

4. Inu, Atat wakumwambako,
   Ndinu wakuticinjiriza ’fe.
   Ndinu wakutitsogoleranso,
   Tikuongani nthawi zonsezo.

No. 236
CIFUNDO CACE
Joshua Leavitt's " Christian Lyre"
Doh is G

1. Dzuka moyo wanga kondwa, Yimbira cipulumutso;
   Ndimyimbire nyimbo; Cifundo cace; Ncoposa!

   CHORUS:
   Wacifundo, wacifundo, Cifundo cace, ncoposa!

2. 'Nandiona wotayika, Anandikondabe ndithu;
   'Nandibweza potayikane: Cifundo cace, Ncoposa!

3. Acurukadi adani, Ngakhale acite zao,
   Moyo wanga asungabe; Cifundo cace, Ncamphamvu!

4. Bvuto loda ngati mtambo, Lasonkhana ligundira,
   Aima pafupi nane; Cifundo cace, Ncokom!

5. Mwini Mfumu akadzadza, Kudzatenga anthu ace,
   Ndikayimba pa tsikulo Cifundo cace, Kosatha!

No. 237
AKRISTU LIMBIKANI
Geo. J. Webb
Doh is G

1. Akristu limbikani, imani mtima nji!
   Mbendela nyamulani, musanthenthemerebi.
   Wotsogolera wathu ndi mwana wa Mulungu;
   Adzangonjetsa onse, adani anthuwo.

2. Tigwire nkhondo yomwe ya Mbuye wathuyo;
   Ticotse zakuipa zokhala mtimamo.
   Sitikwanira tokha kuleka zathu zomwe;
   Koma Mbuyathu Yesu atithangatatu.

3. Tsopano timenyana ndi zakuipazo,
   Pamene nkhondo yatha tidzanka kwathuko;
   Yesu adzalandira ankhondo ace onse,
   Adzakhalitsa naye Kumwamba komweko.

4. Limbikani anzathu! Msanga nkhondo itha;
   Lero kuli cinkhondo,mawa tigonjetsa.
   Kwa iye wolakika, adzakhala moyo.
   Pamodzi ndi Mfumuyo ‘dzakhala kosatha.

No. 238
AKULOWA M’ZIPATA
T.C O’Kane
Doh is E

1. Awa ndani pa tsidya la nyanja, Omwe apyola manda acete,
   Akondwera mwa Yesu? Asamba m’mwazi Wace.

   CHORUS:
   Akulowa mzinda wa Yerusalemu,
   Asamba m’mwazi (wace) wa nkhosa;
   Alowa m’zipata za Yerusalemu,
   Asamba m’mwazi Wace.

2. Awa ndiwo anapeza Yesu, Pamene anali anyamata,
   Nalandira cisomo, Asamba m’mwazi Wace.

3. Awa ndiwo munsautso yao, Anapeza kupuma mwa Yesu,
   Mtendere mu mtimamo, Asamba m’mwazi Wace.

4. Iwo adapirira mabvuto, Anapyola pakati pa moto;
   Yesu ati idzani, Asamba m’mwazi Wace.

No. 239
KODI ULI KULEMEDWA?
Henry W. Baker
Doh is G

1. Kodi uli kulemedwa ndi zoipazo?
   Idza kuno ati Yesu, Pumako.

2. Ndikamzindikira n'inji Mbuye wangayo?
   Ali ndi mabala m'manja mwacemo.

3. Kodi ali ndi cilema m'mphumi mwacemo?
   E! cilembaco ca minga cirimo.

4. Ndikampeza ndikamtsata ninji pansi?
   Masauko ndi misozi ziripo.

5. Ndikamfunafuna Iye ndipezenjiko?
   Kumariza kwa cisoni conse.

6. Ndikampempha anditenge ati bwanji ko?
   Ati Yesu " idza msanga, idzatu."

7. Kukamtsata, kukampeza ndisaukanji?
   Oyera, atumwi, ati idzani. Amen.

No. 240
PAKHOMO
Lowell Mason
Doh is E

1. Mpulumutsi Pakhomopo! Agogoda mofatsa tu,
   Walindila, alindabe, Musamcitire cipongwe.

2. Akulangiza ugule Golide yo ndi Chobvala;
   Dzoze maso, muonetu, Uchotse zonyansa zako.

3. Mvera mau a umboni Ati usanke wachedwa,
   Uli wonyoza, wofunda! Khala changu usanduke.

4. Ntchito yayandika kutha, Kudandaulira kutha;
   Wonyansa anyansebetu. Woyera akhalebe choncho.

5. Lonyowa tsitsi ndi mame, Chifukwa akukondadi,
   Dzuka! Tsegula chitseko; Muuze asachedwenso.

6. Alowe wokondedwayo; Upume pamaso pake,
   Mwa chiyanjano chokoma Ndzadye naye Iye nane.

No. 241
DZIKO LABWINO
John R. Sweney
Doh is G

1. Ndapeza dziko lokoma, Ndi zinthu zonse ndi zanga;
   Zokometsetsa konseko, Usiku wndichokera.

   CHORUS:
   O,dzikolo,lokomalo, Pa phiri lokometsalo,
   Ndipenyetsetsa ku nyanja, Manyumba andikonzera,
   Ndiyang'anitsa dzikolo, Komwe ndidzakhalitsako.

2. Ndiyenda ndi Mpulumutsi, Andikondwera m'njiramo;
   Anditsogolera bwino, Kumwamba ndikafikeko.

3. Mphepo zinunkhira bwino, Za mitengo ya dzikolo,
   Maluwa nao safota, Mitsinje simaumako.

4. Mphepo za kumadzulozo, Ndi nyimbo za kumwambako,
   Angelo onyezimira Ayimba za mphamvu Zake.

No. 242
CHODALA CHIKONDI
Johan G. Naegeli, arr. By. Lowell Mason
Doh is F.

1. Chodala chikondi Chotiyanjanitsa!
   Chiyanjano cha Akhristu, Chifana cha m’mwamba.

2. Pa mpando, wa Mlungu, Wathu tipemphera;
   Tisowa chinthu chimodzi, Chotisangalatsa.

3. Timathandizana, Akatundu athu;
   Timalirirana tonse, M’zobvuta zathuzo.

4. Tikalekanatu, Timamva chisoni;
   Tiyembekezerabetu, Kudzakomananso.

No. 243
DZUKA MOYOWE
Lewis Edson
Doh is B flat

1. Dzuka moyo wanga, Chotsa mantha ako;
   Nsembe ya mwaziwo, Chifukwa cha Ine;
   Indiimira ku mpando, Indiimira ku mpando;
   Dzina langa lalembedwa.

2. Kumwamba alipo, Kundipembedzera,
   Chikondi Chakecho, Chinakhetsa mwazi;
   Anatifera tonsefe, Anatifera tonsefe,
   Awaza mpando wansisi.

3. Mabala asanu, Anampwetekapo;
   Ndiwo mapemphero Ondinenerako
   Atitu “khululukani” Atitu “khululukani”,
   Msalole wolapa afe!

4. Tate amamumva, Wodzozedwa Wake;
   Sangachotse mwana, Wofika kwa Iye,
   Mzimu ubvomera mwazi, Mzimu ubvomera mwazi,
   Ndabadwira mwa Mulungu.

No. 244
IDZA KWA YESU
Unknown
Doh is F

1. ‘Dza kwa Yesu, ‘dza kwa Yesu,
   ‘Dza kwa Yesu lero, lero ‘dza kwa Yesu,
   ‘Dza kwa Yesu lero.

2. Pulumuka, pulumuka,
   Pulumuka lero, lero pulumuka,
   Pulumuka lero.

3. Akhozadi, akhozadi,
   Akhozadi lero, lero akhozadi,
   Akhozadi lero.

4. Muitane,muitane,
   Muitane lero, lero muitane,
   Muitane lero.

5. Alindira, alindira,
   Alindira lero, lero alindira,
   Alindira lero.

6. Mkhulupire, mkhulupire,
   Mkhulupire lero, lero mkhulupire,
   Mkhulupire lero.

7. Adalitsa, adalitsa,
   Adalitsa iwe, iwe adalitsa,
   Adalitsa iwe.

No. 245
PALIBE DZINA LINA
P.E Belden
Doh is G

1. Dzina lokhalo la Yesu, Ndilo dzina lokoma;
   Likondwetsa ‘ngelo m’mwamba, Ndi Akhristu tonsefe.

   CHORUS:
   Dzina, dzina, Palibe longa la Yesu,
   Dzina, dzina, Palibe longa la Yesu.

2. Dzina lokha ndi la Yesu, Pamene ndibvutika;
   Dzina lokha ndi la Yesu Pamene ndikondwera.

3. Ndikufuna kudzamwona, Podza mu’lemerero,
   Ndidzamve Wachita bwino, Ndidzakondwererako.

4. Ngat’afuna n’gwire ntchito, M’munda Wake wa mpesa.
   Kuli bwino Yesu yekha, ’Dalitse ntchito zanga.

5. Ngat’afuna kuti ndife, Akhudze thupi langa,
   Kukhale bwino ndi Yesu, Ndikhulupira mwa ‘Ye.

No. 246
MNENERE YESU LIU
W.H. Doane
Doh is D

1. Mnenere Yesu liu; Bwenzi la pamtima,
   Utiuzetu zomwe; Anakuchitira.

   CHORUS:
   Pomunenera Yesu Zidzatithandiza;
   Mau pang'ono pokha, Nena, yimba, pempha.

2. Mnenere Yesu liu; Wakhulukukidwa,
   Ndi kuyesayesako, Ufike kumwamba.

3. Mnenere Yesu liu, Kukana sinditha;
   Ndikonda Mpulumutsi, Wondiombolayo.

4. Mnenere Yesu liu, Usataye nthawi;
   Wozemba ntchito Yake, Apeza chisoni.

5. Mnenere Yesu liu, Pochepa nkhongono;
   Dzuka ukafooka, mlekere zinazo.

No. 247

# ANGELO AYIMBA KUMWAMBA

Geo. F. Root

Doh is B flat

1. Mabelo kumwamba! Kuli chimwemwe,
   Akatembenuka wochimwa;
   Tate amuchingamira kunjira,
   Mwana wotopa wosochera.

   CHORUS:
   Angelo ayimba kumwamba;
   Ulemu, ulemu m'mingoli,
   Opulumukawo abvekedwa mbu,
   Ayimbira molemekeza.

2. Mabelo kumwamba! Kuli chimwemwe,
   Wotayika wabvomeredwa;
   Wochimwayo wabwezedwa ku tchimo,
   Wabadwanso ngati walero.

3. Mabelo kumwamba! Phwando leroli,
   Angelo ayimba kolimba;
   Mwazani chimwemwe konse achimve!
   Munthu mmodzi wabadwa lero.

No. 249
YESU MNAZARETE APITA
Theo. E. Perkins
Doh is G

1. Chikhamuchi chifunanji Choyenda motanganidwa,
   Chosonkhana tsiku ntsiku? Ndiuzeni achitanji?
   Khala chete ndikuuze; “Yesu Mnazerete apita,”
   Khala chete ndikuuze; “Yesu Mnazerete apita.”

2. Yesuyo ndani? Wakuti agwedeza mudzi chonchi?
   Mlendo chabe ndi Waluntha Kugwedeza anthu chonchi?
   Modzidzimutsa nayankha: “Yesu Mnazerete apita,”
   Modzidzimutsa nayankha: “Yesu Mnazerete apita.”

3. Yesu! Pansi natsikira Ngati munthu nayendapo;
   Opsyinjika nawapeza, Odwala opundukawo,
   Akhungu nakondwa kumva; “Yesu Mnazarete apita,”
   Akhungu nakondwa kumva; “Yesu Mnazerete apita.”

4. Lero ayenda ponsepo Tiona mapazi Ake;
   Ayenda m’ntchito zathuzo, Adza kwathu kudzakhala:
   Mokondwa tipfuulitse: ”Yesu Mnazarete apita,”
   Mokondwa tipfuulitse: “Yesu Mnazarete apita.”

5. Idzani olemedwanu! Mupume mpeze mudziwo
   Otaika a Atate, Bwerani mulandire;
   Oyesedwanu thawani: “Yesu Mnazarete apita,”
   Oyesedwanu thawani: “Yesu Mnazarete apita.”

6. Ukanabe naitana, Nunyoza chikondi Chake,
   Chisoni adzakusiya Maomboledwe Akewo;
   Udzati mayo ndachedwa “ Mnazarete wandisiyadi,”
   Udzati mayo ndachedwa “ Mnazarete wandisiyadi.”

No. 249
NKHOSA ZAMBIRI M'KHOLAMO
Ira D. Sankey
Doh is A flat

1. Nkhosa Zake zambiri m'kholamo
   Anasunga m'busayo.
   Imodzi Inasocherera,
   Yotaika kuthengo.
   Kutari ku phiri loopsya,
   Kutari ndi m'busa Wakeyo,
   Kutari ndi m'busa Wakeyo.

2. Mbuye muli zambiri m'kholamu
   Kodi sizikwanira?
   Nayankha m'busa, ndi yangayo,
   Imene yatalika.
   Ngakhale njoopsya njirayo
   Ndilinga ku phiri kupeza.
   Ndilinga ku phiri kupeza.

3. Koma opulumuka sadziwa
   M'khawa m'busa napyola,
   Ndi mdima wo'psya usikuwo,
   Polanda nkhosayo.
   Anamva kulira kutali,
   Napeza yofo'ka ikufa,
   Napeza yofo'ka ikufa.

4. Mbusa, Ndiona mwazi m'njirayi;
   Ndi chifukwa chiyani ko?
   Ndinaukhetsa potsata 'we,
   Kubweza ku kholako.
   Ndi m'manja mwalaswa bwanjimo?
   Ndalaswa pofunafuna 'we,
   Ndalaswa pofunafuna 'we.

5. Ndipo ponse pa phiri ndi m'dambo,
   Ndi m'makhwawa ponsepo,
   Namveka liu lopfuula,
   Kondwani ndapezayo.
   Angelo a Mlungu nayankha,
   Ambuye napeza nkhosayo,
   Ambuye napeza nkhosayo.

No. 250
TCHIMO MUSALOLE
Horatio R. Palmer
Doh is B flat.

1. Tchimo musalole, Limachimwitsa,
   Gonjetso limodzi Libweza wina;
   Pitabe m’tsogolo, Zoipa leka,
   Yang’ana kwa Yesu, Adzakusunga.

   CHORUS:
   Funsa Mbuye thandizo,
   Adzakusunga iwe;
   Ali wolola Iye,
   Adzasunga iwe.

2. Thawani oipa, Ndi otukwana,
   Lemekeza Mlungu, Osamamnyoza;
   Khala waulemu, Ndi wachifundo,
   Yang’ana kwa Yesu, Adzakusunga.

3. Kwa wolakikayo, Korona ‘patsa,
   Mwa chigonjetsocho, Kwa opirira;
   Mpulumutsi wathu, Adzalimbitsa,
   Yang’ana kwa Yesu, Adzakusunga.

No.251
KULIRA SIKANTHU
Rev. Robert Lowry
Doh is E flat

1. Kulira sikanthu-Ngakhale nkhope igwe,
   Singaletse matsoka, Singatsuke machimo-
   Kuli sikanthu.

   CHORUS:
   Yesu nafa pa mtanda, Yesu nandiferatu,
   Yesu andilindira Kundipulumutsa.

2. Ntchitonso sikanthu-Ngakhale ikometse,
   Maganizo oyera, Sangandikonzetsenso-
   Ntchito sikanthu.

3. Kudika sikanthu-ndigona wotayika,
   Ndimva kuitanatu; Kudika ndifa chabe-
   Kudika sikanthu.

4. Yesu Mpulumutsi Amene nandifera,
   Ndikhulupira Inu, Mundipulumutsenso-
   Mundipulumutsa.

No. 252
WOCHIMWA IWE, BWERA
J.H STOCKTON
Doh is G.

1. Wochimwa iwe, bweratu, Kwa Yesu, Mbuyeyo;
   Atero Iye, pumatu, Umvere mauwo.

   CHORUS:
   Khulupira mau onse a Mbuyathuyo,
   Uli nawo pakumvera, Inde, moowo.

2. Ambuye Yesu anatsira Mwazi Wake psyu,
   Timira m’mwzi womwewo, Tiyeayera mbu.

3. Wa moyo ndiye Yesudi, Zoona Zakezo,
   Akhala Iye njiratu Yofika mmwambamo.

4. Tiyeni tonse, tinkeko, Ulendo wathuwo,
   Ku dziko Lake mmwambamo, ’Dzakhale nayeko.

No. 253
MBUSA WA ISRAYELI
W.H. Havergar
Doh is A flat

1. M'busa wa a Israyeli, Wochititsa chidwi;
   Imva aitana nkhosa Adzatifukate!

2. Akaitana zimadza, Satonza maina;
   Amazidalitsa zonse, Mwini wa angelo.

3. Tibwera nazo kwa Inu, Tikupatsirani,
   Ife tiri anu omwe, Ana'thu ndi anu.

No. 254
DZINA LA YEHOVA
Attributed to Henry Carey
Doh is F

1. Dzina la Yehova, Liyamikidwetu, tiliopa;
   Kumwamba-mwambako, Chikondi choposa,
   Konseko kumveka Mphamvu Yake.

2. Lipenga limveke Lachigonjetsocho, konse konse;
   Mngoli ukhalepo; Alimba abwino;
   Amveke ponsepo, Omtamanda.

3. Poyimba mokweza, Kungani zingwezo, zotengana!
   Atipatsa mpweya, Mpweya wodzazatu,
   Ufulu Wakewo, Tiyamike.

No. 255
NDIKUSOWANI YESU
Arr. By Edward F. Rimbault
Doh is F

1. Ndikusowani Yesu, Ndiri waumphawi;
   Mlendo wopanda malo, Za dziko ndiribe.
   A Yesu mundikonde, Mundichingamire,
   Ndi kunditsogolera, Mphamvu yanga ndinu.

2. Ndisowa mtima wanu, Kudziwa nkhawazo,
   Ndi mayesero anga, Ndi zachisonizo.
   Nsowa Mzimu Woyera,Womandiphunzitsa,
   Kundiuzane Yesu, Ndi Mwana wa nkhosa.

3. Ndikusowani Yesu, Ndionane Nanu,
   Mu uta-wa-lezamo, Pa chimpando Chanu
   Ndi ogulidwa m’mwazi, Ndikakondwerere
   Nyimbo zosadukiza, Ndikumpenyetsetsa.

No. 256
MULUNGU MUNATHANGATA
William Croft
Doh is C

1. Mulungu munathangata, Mudzathangatabe;
   Wotitchinjiriza m’zoopsya, Kwanu mutifitse!

2. Mwa mthunzi wa mpando wanu, Ndimo tibisala;
   Dzanja lanu liposadi, Tiri mosungika.

3. Dziko linakhazikidwa Mapiri naima,
   Mulungu wosamariza, Zaka zosathera.

4. Zaka zambiri, kwa Inu, Ziri ngati dzulo,
   Ufupi ngati usiku, M’mawa kusanache.

No. 257

OLIMBA NGATI THANTHWE

Scottish Psalter

Doh is E flat

1. Mapiri sagwedezeka, Ifenso chomwecho;
   Olimba gwa ngati thanthwe; Ake a Yehova.

2. Phiri ndi khoma kulibe, Lofanana Naye;
   Mikono yokonda myaya Isunga oyera.

3. Achitireni zabwino, Akumvera Inu,
   Otsamira choonadi, Cha malamulowa.

No. 258
CHIKHULUPIRIRO CHIMODZI CHA MOYO
Music C.H.683 Louis Bourgeois
Doh is G

1. Lamulo la Mulunguli, Sichinthu chopanda pake;
   Ndi lokhalitsa myayadi, Simau chabe, ndi moyo.

2. Lamulo lanu loyera Mutikhulululukirefe,
   Langwiro mwa ilo lokha, Akunja sangalione.

3. Khululukira anu, Kwa zolakwa zao zonse,
   Mutithandize kusunga Malamulowo angwiro.

No. 259
TIDZAKOMANA KODI?
Elibu. S. Rice
Doh is A

1. Tidzakomana patsidya, Mafunde akazatha?
   Kowala kosalekeza, Kulibe chisoninso?

   CHORUS:
   Tidzakomanako? Tikakomna patsidya?
   Tikakomane patsidya, mabvuto akadzatha?

2. Tikakomana padoko. Akadzatha mavuto?
   Tidzaiponya nangula Pagombe lokomalo?

3. Tikakomana m’mudzimo; Nyumba zonyezimira,
   Makomanso nga yasipi, Omangidwa ndi Mbuye?

4. Tikakomana ndi Yesu Potenga anthu Ake;
   Ubwino tidzaudziwa Ntakhala mu mpando’ke.

No. 260
DAMBO LA BYULA
Joseph Garrison
Doh is C

1. Ndipitir kunsi kwa dambo la chipululu,
   Liri dambo lokongola lotchedwa la Byula
   Koma ndapezanso monse momera maluwa,
   Mpulumutsi Mwini Wake ayenda ndi Ine.

   CHORUS:
   Dambo Byula, dambo Byula, likomera Ine
   Dziko la pangano ndilionera patari.

2. Palibe mthuzi wotsitira panjira panga,
   Kuunika kwa ulemerero kuwalitsa:
   Am'mwamba andiyimbira nyimbo zokongola.
   Apokolezana bwino kundichingamira.

3. Ndiri kunka ndi nsangala ku mzinda wowala,
   Nsangalazo ziwalitsa njira tsiku ntsiku;
   Ndasendez zipata za mzinda wakuwala
   Khwalalalo lindifitsa mzinda wa chikondi.

No.261
DAMBO LOKONGOLA LA EDENE
William F. Shervin
Doh is E flat

1. Dambo labwino Edene, Muli bata msana;
   Mitima ya otopabe Ipuma nichira.

   CHORUS:
   Dambo labwino Edene, Kwao  kwa odala,
   Ndazunzikadi ndi mabvuto, Ndidzatu ndidzapume.

2. Mtima wosowa wolira, Ndzapeza mwayi,
   Nuimba nyimbo nda'ngelo, Akutaritari.

3. Ali kwao Mpulumutsi; Ndi oomboledwa,
   Dziko la ulemerero, Imvani nyimboyo.

No. 262
KHRISTU KAPENA BARABA
F.E Belden
Doh is C

1. Nditani naye Yesu? Waima panoyu,
   Wavala chinyong'onyo, Ndi minga pamutu.

   CHORUS:
   Tsopano ndifunse, Muyankha chotani?
   Ndimpachike Mfumu Yesu, Atsale Baraba?

2. Ndimasule mbalayi, Chimunthu cha dama?
   Wochimwa, ngosachimwa?Mukanapo yani?

3. Funsotu loopysali! Litengeni bwino,
   Nsisi zilindirabe, Koma mwa mavuto.

4. Mpando wachiweruzo Sungakane dziko?
   Anapfuula "Chotsa, Mumpachike Yesu!"

5. Si kwa ochimwa okha Funso linenetsa;
   Mvani Akhristu nomwe, Ora loyesedwa.

No. 263
MVANI MAU AMBUYE
H.L Gilmbur
Doh is F

1. Mvani mau a Ambuye wathuyo,
   Mudze nazo zachikhumi m'nkhokwe,
   Perekani ndi mitima yanuyo,
   Mulandire madalitso.

   CHORUS:
   Mudze nazo zachikhumi m'nkhokwe,
   Mndiyese 'ne, Ati Mbuyeyo.
   Ndizakupatsa madalitso,
   Ndipo mudzasowa nawotu malo.

2. Mukufuna kodi mphamvu Yakeyo?
   Mudze nazo zachikhumi m'nkhokwe.
   'Dzanitu chifupi ndi Ambuyeyo,
   Polandira madalitso.

3. Muli nako kanthu ndi Ambuye ko?
   Mudze nazo zachikhumi m'nkhokwe.
   Mudze nazo monga mwa lonjezo 'ke,
   Ndipo mudzadzlitsidwa.

4. Yamikani Mbuye pompemphera 'Ye,
   Podza nazo zachikhumi m'nkhokwe,
   Khulupiririrani mau Akewo,
   Ndi kumuthokoza Iye.

5. Yimbirani ndi chimwemwe nyimbozo,
   Mutabwera nazo zachikhumi,
   Tipfuule mokondwera tonsefe,
   Ka'mba tinadalitsidwa.

No. 264
PACHIYAMBI MLUNGUYO
F.E Belden
Doh is G

1. Pachiyambi Mlunguyo Analenga dzikoli,
   Tsono napumuladi Lachisanu nchiwiri.

   CHORUS:
   Tikondwera, Tikondwera,
   Tikondwera podza pa Tsiku la Sabatalo.

2. Mlungu napatulanso Tsiku lakupumalo,
   Nalipatsa kwa ife Ndi Sabata Lakelo.

3. Anthu Ake kalelo Anasunga tsikulo,
   Ndi pobwera Yesuyo Iye anasunganso.

4. Osanthula m'bukhumo, Akuona kutitu
   Mlungu sanathei, Tsiku Ndake lomweli.

5. Ndipo ati m'bukhumo Podzabwera Yesuyo
   Anthu adzasungabe Tsiku la Sabatalo.

No. 265
MTENDEREWO
Arr.by Charles J. Vincent
Doh is C

1. Mtenderewo, m’dziko la mdimali; Mwazi wa Yesu unong’oneza.
2. Mtenderewo,m’ntchito zochuruka; Ntchito ya Yesu ndiko kupuma.
3. Mtenderewo, m’bvuto lotizinga; Mtendere uli mwa Yesu yekha.
4. Mtenderewo, anga ali m’tari; Yesu asunga Ine ndi iwo.
5. Mtenderewo, uli m’tsogolomo; Tidziwa Yesu ali pa mpando.

No. 266
NDIDZAKUTSATANI
H.Rosecrans
Doh is A

1. Yesu nditsata Inu, Ndamva mundutana;
   Nkonda Inu, ndidzadi, Munditsogolere.

   CHORUS:
   Ndikutsatani, ndikutsatani,
   Ndikutsatani komwe muntsogoza.

2. Timaso tiphophonya, Mapazi asochera;
   Ndifooka mwinamo, Mundilimbikitsa.

3. Zisoni zindipinga, Ndipusa ndi zoipa,
   Ndidzalimbikitsidwa, Potsatira Inu.

No. 267
FESA  MBEU ZA CHIKONDI
S.J Vail
Doh is G

1. Tisonkhanitse zabwino, M’njira mwathu monsemo;
   Tisunge tirigu yekha, Titaye zachabezo;
   Tipeze zokondweretsa M’madalitso a lero,
   Mwa chipiriro tichotse Minga yokhumudwitsa.

   CHORUS:
   Ufese zachifundo, Ufese zachifundo,
   Ufese zachifundo, Zomwe tidzakolola.

2. Sitisamala maluwa Ndi mbalame poyimba,
   Mpaka mbalame ndiponso maluwa zitachoka;
   Dzuwa sitilisamala Pa nthawi ya chilimwe,
   Akafikanso mazizi Nthawiyo tiifuna.

3. Mwana akachita ngozi Poswa chikho chomwera
   Kodi mukalipo ko’psya Poturutsa tsinyalo?
   Mukadziwa kuti mawa adzakhala wakufa,
   Kodi pakukwiya naye Mupsya mtima leroli?

4. Poganizira za m’mbuyo Za zomwe tinachita,
   Za mauwo okalipo Okhumudwitsa ena,
   Ndi ntchito zosaganiza; Izi zitikumbutsa
   Kufesatu zachifundo Zomwe tidzakolola.

No. 268
BATA NDU!
Horatio R. Palmer
Doh is C

1. Mbuye, nyanga yakalipa, Mafunde akweretsa!
   Mlengalenga nawonso wada; Kodi tifere m'madzi;
   Kodi simukusamala, Mugoneranjiko?
   Pamene ife tiri ndi mantha, Kodi tifre m'madzi?

   CHORUS:
   Namondweyo andimvera Ine, Bata ndu! (Bata ndu!)
   Ngakhale nyanja zikalipe,
   Ziwanda, anthu, ngakhale zinazo,
   Madzi sangamize bwato Mwini,
   Nyanja ndi mtunda ali momwemo;
   Zonse zingondimvera Ine; Bata ndu, bata ndu!
   Zonse zingondimvera Ine, Batadi ndu!

2. Mbuye bvuto mu mtimamu Landibvuta leroli;
   Kuchirimika konse kwatha; Ndipulumutsenitu
   Nkhwenkhwe ya tchimo yozunza, Inditsirizitsa;
   Ndamuka ine, ndamuka, Mbuye! Dzandipulumutseni.

3. Mbuye zobvutazo zatha, Kwagwa bata tsopano,
   Kwawala ngati kalirole, Ngati ndiri kumwamba;
   Msandisiyenso Ambuye, Tikhale pamodzi;
   Ndikafike ku gombe lodala, Mukandipulumutse.

No. 269
MPULUMUTSI WOZIZWITSA NDI YESU
William J. Kirkpatrick
Doh is D

1. Mpulumutsi wozizwitsa ndi Yesu,
   Mpulumutsi wozizwitsa,
   Andibisira moyo wanga m'thanthwe,
   Ndiona zokondweretsa.

   CHORUS:
   Andibisira moyo wanga m'thanthwe,
   Aphimba dziko louma;
   Moyo wanga aika pobisika,
   An'phimba ndi dzanja Lake,
   An'phimba ndi dzanja Lake.

2. Mpulumutsi wozizwitsa ndi Yesu,
   Anditulitsa katundu,
   Andichirikiza sindidzasowa,
   Wondipatsa mphamvu ndiye.

3. Apatsa madalitso ochuruka,
   An'dzazanso umulungu,
   Ndiyimba mokondwa ndilemekeza
   Mpulumutsi ndi wangadi.

4. Ndikabvekedwa zowala ndiyera,
   Kukomana naye m'mwamba,
   Ndapulumukadi m'chikondi Chake,
   'dzapfuula ndi anzanga.

No. 270
NKHOSWE YATHU
J.H Dykes
Doh is E flat

1. Mpulumutsi potsazika, Ndi mau okonda,
   Msangalatsi, adzakhala Nkhoswe yathu.

2. Anadza kudzatikonza, Wansisi, wolola
   Kupeza mmodzi wodekha Apumemo.

3. Timva mau'ke odekha Ochokera m'mwamba,
   Otsutsa tchimo odekha Aitana.

4. Okoma wonse ndi Wake, Chigonjetso chonse,
   Ganizo lachiyesero, Zonse nzake.

5. Mzimu wanu wachiyero, Mtimvere nsisitu;
   Mukhale m'mitima mwathu, Ana anu.

No. 271
NKANA TCHIMO NLALIKURU
W.H Doane
Doh is A flat

1. Nkana tchimo nlikuru, lingakanganulidwe;
   Nkana tchimo nlikuru, lingakanganiludwe,
   Nkana machimo ngofi'ra,ayeretsedwa;
   Nkana tchimo nlikuru, Nkana tchimo nlikuru,
   Lingakanganiludwe; Lingakanganulidwe.

2. Imva liu lipempha, "Bweranso kwa Mlunguyo;"
   Imva liu lipempha, "Bweranso kwa Mlunguyo."
   Ali ndi nsisi zambiri, ndi chikondicho.
   Imva liu lipeempha, Imva liu lipempha,
   "Bweranso kwa Mlunguyo; Bweranso kwa Mlunguyo."

3. Akukhulululukira, sadzakumbukiranso;
   Akukhulululukira, sadzakumbukiranso;
   "Ndiyang'aneni anthuni," ati Mbuyeyo;
   Akukhulululukira, Akukhulululukira,
   Sadzakumbukiranso, Sadzakumbukiranso.

No. 272
PONYA CHINGWE CHA MOYO
Arr. By Geo. C. Stebbins
Doh is G

1. Pabvuta pa nyanja, ponya chingwe,
   Pali mbale apulumutsidwe;
   Mbale wa mnzathu, ndani angathe
   Kuponya chingwecho, kumpulumutsa.

   CHORUS:
   Ponya chingwecho! Chingwe cha moyo!
   Alikunka ndi madzi!
   Ponya chingwecho! Chingwe cha moyo!
   Wina amira lero.

2. Ponya chingwecho mofulumira;
   Uchedweranji ndi kujejema?
   Ona amira, fulumiratu,
   Ukampulumutse msanga, msangatu.

3. Ponya anthuwo azunzikatu,
   Athatha koopsya sungafike;
   Mphepo za bvuto ndi z matsoka,
   Msanga ziwatsitsa kwakuya kwa bi.

4. Nyengo yowapulumutsa itha,
   Atifera posachedwa pano;
   Kangaza m'bale usachedwetse,
   Ingoponya chingwe apulumuke.

No. 273
TSAMIRA PA MANJA A YESU
L.E Jones
Doh is G

1. Tsamira pa manja a Yesu, Akuthangate athangata;
   Ukamkhulupira ndithu, Adzakusangalatsa.

   CHORUS: (Sop. & Tenor):
   Tsamiratu m'chikondi Chake; Tsamirayu, yesa chifundo:
   Tsamiratu, yang'ana m'mwamba, Tsamira Mpulumutsi.

   (Bass& Alto):
   Tsamiratu Iye, m'chikondi Chake. Tsamiratu Iye, yesa chifundo;
   Tsamiratu, yang'ana m'mwamba. Tsamira Mpulumutsi.

2. Tsamira pa manja a Yesu, 'Dzauza njira, adzauza;
   Ingotsata mokondwera, Pomvera mau Ake.

3. Tsamira pa manja a Yesu, 'Dzakusamala, kusamala!
   Katundu wolemeretsa Mpereke kwa Ambuye.

4. Tsamira pa manja a Yesu, Msiyire zonse, zonsezodi!
   Mtima Wake ngwachikondi, Maso Ake sasinza.

No. 274
NDIRI NDI MBUYE
Ira D. Sankey
Doh is G

1. Ndiri ndi Mbuye wodandaulira,
   Akonda Iyeyu kuposa dziko;
   Pano andiyang'anira mwachifundo,
   Ndifunatu akhale wa inunso!

   CHORUS:
   Ndipempherera'nu, Ndipempherera'nu,
   Ndipempherera'nu, Ndipempherera'nu.

2. Ndiri ndi Tate andipatsa Ine
   Chiyembekezo cha moyo wosatha;
   Sachedwa kuitana tipite kwathu;
   Ndifuna adzalandire inunso!

3. Ndiri n'zobvala,zopanda mabanga
   Zindilindira mu ulemerero;
   Wowala monsemo konko n'dzalandira,
   Bwenzi ndifuna ukalandirenso!

4. Pamene Yesu wakupeza iwe,
   Tauzatu ena za mtenderewo
   Mwini ndiye Khristu yemweyo apatsa,
   Mtendere ndifuna mulandirenso!

No. 275
KOSATHA!-N’KUTI?
Jno. R Sweney
Doh is E

1. “Kosatha! –n’kuti?” Ndilo funsolo;
   Konse komwe uli liri komweko!
   Udzakhala kuti nthawi zosatha?
   Udzakhala kuti nthawi zosatha?

2. ”kosatha! N’kuti?” ”Kosatha n’kuti?”
   Ndi oomboledwa? Ndi otaika?
   Mbali izi njiti- ”Kosatha! N’kuti?”
   Mbali izi njiti- ”Kosatha! N’kuti?”

3. ”Kosatha! N’kuti?” Uchitiranji
   Zokondwa za dziko mosaganiza?
   Popanda kusankha- Kosatha ! N’kuti?”
   Popanda kusankha-Kosatha!N’kuti?”

4. ”Kosatha! N’kuti?” Bwenzi samala;
   Adzaweruzatu Mulungu msanga.
   Lero linganene-”kosatha! N’kuti?”
   Lero linganene-”kosatha!N’kuti?”

5. ”kosatha! N’kuti?” ”Kosatha! N’kuti?”
   Bwenzi usagone, lekana m’dziko.
   Mpaka utayankha-”Kosatha! N’kuti?”
   Mpaka utayankha- ”Kosatha!N’kuti?”

No. 276
M’KHOLA MWA NG’OMBE
E. E Hasty
Doh is G

1. M’khola mwa ng’ombe mu Betlemumo, Anabadwamo Ambuyangayo,
   Etu, ndidziwa, natsikirako, Kufuna Inetu.
   Afuna Inetu, Akufuna Inetu.
   Etu, ndizizwa, natsikirako, Afuna Inetu.

2. Popachikidwa pa Kalvarepo, Yesu anandiombolerako,
   Inde, ndidziwa, nakondaneko, Nafera Inetu.
   Nafera Inetu, Nafera Inetu.
   Inde ndizizwa nakondaneko, Nafera Inetu.

3. Mbusa wokoma ndi Mbuyangayo, Nandiitana posocherapo,
   Konse koipa nalondaneko. Kubweza inetu.
   Abweza Inetu, Abweza Inetu.
   Konse koipa nalondaneko, Abweza Inetu.

4. Uko kumwambako, Mbuyangayo, Nandikonzera mokhaliramo,
   Tsiku linalo adzabweranso, Kutenga Inetu.
   Atenga Inetu, Atenga Inetu.
   Tsiku linalo adzabweranso, Kutenga Inetu.

No. 277
TSOGOLERE MUUNI
John B. Dykes
Doh is A flat

1. Tsogolere muuni mu mdima, Tsogolere;
   Kwada ndiri kutari ndi kwathu; Tsogolere.
   Sindipempha kuona za m’tari,
   Phazi langa limodzi likwana.

2. Sindinali wotere wokhoza kupempha;
   Ndinakonda njira’nga; Tsogolere;
   Ndinakonda zinthu zachibwana, Tsogolere
   Ndinanyada,musazikumbuke.

3. Mphamvu yanu yandidalitsadi;Intsogoza
   Mu malo monse moipa mpaka mdima watha;
   M’mawa ‘ngelo andisekerera;
   Amenewo ndawakonda kale.

No. 278
SINJIRA YANGA
F.E Belden
Doh is D flat

1. Sinjira yanga bi, Ngakhale ide bi;
   Tsogolerenitu, Mndisankhire njira.
   Ndisasankhe ndekha; Msandilekere;
   Sankhireni Mbuye, Ndiyendemo bwino.

2. Ufumu ndifuna wanu, M'patse njira
   Yofitsa ku moyo Yolunjika kwanu.
   Mndisungire chikho chodzaza ndi moyo,
   Sankhire abwenzi, Chuma pena tsoka.

3. Sankhire abwenzi, Nthenda pena thanzi;
   Musankhire Ine chondiyeneracho;
   Ndisadzisankhire chokula-chochepa;
   Tsogolerenitu, Mndikwanire Mbuye.

No. 279
"IDZANI KUNO KWA INE"
F.E Belden
Doh is C

1. Ha! Mtima wachisoni maso osaona,
   Mungathe kukondwera mwa Yesu, Mbuyathu.

   CHORUS:
   Idzani kwa Ine nonsenu
   Inu akutodwa ndiwo mudzapume,
   Senza gori langa, phunzira
   Ndiri wofatsa mumtimamo,
   Mudzapumula m'myoyo yanu.

   Bass,Tenor & Alto:
   'Dzanitu, 'dzani kuno 'dzanitu, nonsenu otodwa

   Alto:
   Inu akutodwa ndipo mudzapume,

   Bass & Tenor:
   'Dzanitu akutodwa ndipo mudzapumula.

   Alto, Tenor & Bass:
   'Dzanitu, senza gori,'Dzanitu, phunziratu,

   Tenor & Bass:
   Ndi wofatsa mumtimamo, Mudzapumula m'yoyo yanu.

2. Chimwemwe cha m'dzikoli sichikwanitsa'fe,
   Chikondi chikondwetsa, chikondi cha Yesu.

3. Chisomo chopambana cha Yesu Khristuyo
   Chidzakhulululukira olapa onsewo.

4. Mtendere ngati mtsinje, chikondi ndi nyimbo
   Ndi gori lakufewa tipeza mwa Yesu.

No. 280
MFUMU YATHU
Chas. H. Gabriel
Doh is F

1. Nyimbo zathu zokoma, Tadza nazo lero.
   Kudzayamika Mbuye, Njira ndi moyowo.

   CHORUS:
   Tiyimbatu kutamanda Mfumu (Mfumu)
   Tiyimbatu Ulemu kwa Mfumu.

2. Anakonda tiana pokhala pansipo.
   Ngakhale ali m'mwamba Amatikondabe.

3. Tikonda kumyimbira, Ndi kumva za Iye,
   Pamene anakhala pa dziko kalelo.

4. Mpulumutsi wodala, Tikugwadirani,
   Kuti mutithandize kukhulupira 'Nu.

No. 281
NYENYEZI YABWINO
F.E Belden
Doh is C

1. Nyenyezi yabwino yowala ndi ulemerero wa m'mwamba
   Kuwala kwake kutsogoza anzeru napeza Mwana.

   CHORUS:
   Yowalayo, yowalayo, Nyenyezi yabwino m'phiri,
   Yowalayo, yowalayo, Chipulumutso cha Mlungu.

2. Mau anawadziwitsadi nthawi yafika ya nyenyezi,
   Anaitsata yowalayo- Ndi " Khristu nthanda ya m'mawa."

3. Nafe titsafe monga iwo, Muni wa dziko wonenedwa;
   Titsafe mpaka tikafike, Ku mpumulo wa kumwamba.

No. 282
MINGOLI ZIKWI KHUMI
Lowell Mason
Doh is G

1. Ha! Mingoli ndi maunso Alemekeza m’mwamba;
   Yesu m’mwambamo akondwa; Alamula ponsepo;
   Ali pa mpando uko; Yesu alamulira.
   Aliluya! Aliluya!aliluya! Amen.

2. Krona wanu savulidwa, Mfumu yolemerera;
   Chikondi chanu chosatha, Kwa anthu anu onse;
   Anthu anu okondwa Adzaona nkhopeyo.
   Aliluya! Aliluya!aliluya! amen.

3. Ambuye idzani msanga Tsikulo tilisowa
   Kudzamvetsera tsikulo, m’mwamba ndi dziko zatha!
   Tidzaliza mingoli Ulemu kwa Mfumuyo
   Aliluya! Aliluya! Aliluya! Amen.

No. 283
KODI NDIWE? KODI NDINE?
James McGranahan
Doh is F

1. Wina adzalowa pakhomo, Msanga posachedwa,
   Adzadya za ulemerero, Kodi ndiwe? Kodi ndine?
   Wina adzayenda m'miseu, Nadzakhala ndi masomphenya
   Podzakondwerera kosatha: Kodi ndiwe? Kodi ndine?

2. Wina adzatula katundu, Msanga posachedwa,
   Nadzalandiratu korona, Kodi ndiwe? Kodi ndine?
   Wina adzaonatu Mfumu, Atamasuka ku zadziko,
   Nadzakondwa naye kosatha: Kodi ndiwe? Kodi ndine?

3. Wina 'dzagogoda chitseko, Msanga posachedwa,
   Nadzamvatu, Sindikudziwa, Kodi ndiwe? Kodi ndine?
   Poitana sadzamuyankha, Chitseko chitatsekedwatu,
   Ndipo sadzalandira mphotho: Kodi ndiwe? Kodi ndine?

4. Wina adzaimbatu nyimbo, Msanga posachedwa,
   Pamodzi ndi owomboledwa, Kodi ndiwe? Kodi ndine?
   Wina adzakakondwerera, Ndi okondedwa pa dokolo,
   Ataomboledwa kosatha: Kodi ndiwe? Kodi ndine?

No. 284
POPITA MASIKUWA
Ira D. Sankey
Doh is A flat.

1. Kuli anthu obvutika, Popita masikuwa,
   Kuli anthu akutopa, Popita masikuwa;
   Ngati tiwakondwetsa,Poyenda ulendowu
   Zabwino tichitetu, popita masikuwa.

   CHORUS:
   Masiku apita, Masiku apita,
   Zabwino tichitetu! Popita masikuwa.

2. Kulibe nthawi yotaya, Popita masikuwa;
   Mukhale osangalala, Popita masikuwa;
   Dziko liri m'chisoni, Misozi ndi maliro;
   Thandiza obvutika, Popita masikuwa.

3. Zotimanga tizisiya, Popita masikuwa;
   Mmodzi ndi mmodzi atsala. Popita masikuwa
   Zabwino tikadzala, Ponse ponse zimera;
   Tidzakhala okondwa, Popita masikuwa.

No. 285
ALIPO MALO OPUMA
C.B Mcfee
Doh is D flat

1. Alipo malo opuma, Mfupi ndi Mulungu,
   Kumene tchimo kulibe, Mfupi ndi Mulungu.

   CHORUS:
   O! yesu Mpulumutsi, Mtima wa Mulungu,
   Tisungeni pompano, Mfupi ndi Mulungu.

2. Alipo malo okoma, Mfupi ndi Mulungu,
   Pakukomana ndi Mbuye Mfupi ndi Mulungu.

3. Alipo malo okwana, Mfupi ndi Mulungu;
   Chimwemwe ndi mtenderewo, Mfupi ndi Mulungu

No. 286
NDITENGENI
Arranged
Doh is D

1. Ndifuna kuona nthawi Yonkha ku Ziyoni,
   Komwe tidzakhala bwino, Ku mudzi wa Yesu.

   CHORUS:
   Nditengeni tengeni, Ku Ziyoni
   Ku mudzi wachikondiwo. Ku mudzi wa Yesu.

2. Ndidzamva Aliluyayo Kwa khamu ‘likuru;
   Ndikayimba nao nyimbo, Ya oomboledwa.

3. Ndidzakamwone Israel Ndi Yesu Kalonga,
   Ndi mpando wa mfumu yanga Yemwe ’natilenga.

4. Ndifuna ku Yerusalemu, Ku mudzi wa Mfumu,
   Ndifuna n’kadye zipatso Zotipatsa moyo.

No. 287
M’MAYESERO ANGA
Spencer Lane
Doh is C

1. M’mayesero anga, Tate mndisunge;
   Ndisakukaneni, Kukusiyani.
   Pondenguma ine, Kumbukireni,
   Nsalekane nanu, Musanditaye.

2. Za dziko nzachabe, Ndisatengeko;
   Cuma ca poyera, Cisandikope.
   Kusunga kwanu sisi, Ndikubvomera.
   Ndikana zoipa Zolakalaka.

3. Matsoka si anu, Zolabadira;
   Zowawa zikadza Kusokonzera:
   Ndikupemphanitu Ndisachimwe bi;
   Nkhawa zanga zonse, Ndikupatsani.

No. 288
ANADZATU KWA YESU
Joseph Garrison
Doh is F

1. Anadzatu kwa Yesu ndi mphatso zaozo,
   Ndi mtima wa chikondi Natula zonsezo.
   Zokoma mtima nchito Zothandizanatu,
   Ndi zopereka zao Ndizo za mtengotu.

   CHORUS:
   Tulani mphatso zanu Kwa Yesu Mbuyeyo,
   Pereka mtima wanu Pa guwa lacelo.

2. Pakati pa opatsa Naima mlendoyo
   Naona anthu ena Napatsa zaozo.
   Naye nalakalaka Kupatsa zacezo,
   Analibetu kanthu Kopatsa Mbuyeyo.

3. Nalira, Mbuye wanga, Wokoma mtima ‘Nu.
   Tengani mtima wanga Wodzaza chimolo.
   Ambuye namuyankha Usati yacepa;
   Yakoyo, mwana wanga Yaposa zonsezo.

No. 289
MUNDILNDIRETU
J.H. Stockton
Doh is A flat

1. Kwa Inu Yesu ndilira; Wopanda Inu ndidzafa;
   Mundipulumutse Mbuye Mundilandiretu.

   CHORUS:
   Mundilandire, mundilandire
   Mundipulumutse Mbuye, mndilandiretu.

2. Ndine wocimwa kwambiri, Koma munafera ine;
   Mutha konse kundikonza, Mundilandiretu.

3. Sinditha kudzikonzatu, Ndingodzipereka ndekha;
   Ndipulumutseni nokha, Mundilandiretu.

4. Ndigwadira nsisi zanu, Ndioneni Ambuyanga;
   Yayambidwa nchito yanu Mundilandiretu.

No. 290
TIKONDWERA PAKUGWIRA NTCHITO
W.A. Ogden
Doh is A

1. Tikondwera pakugwira nchito ya Ambuye mofunitsatu,
   Yomwe Mbuye wathu watipatsa, Tidzacita molimbikatu.

   CHORUS:
   Pogwira nchito, timakondwatu, timakondwatu,
   Pogwira nchito m'munda wa Ambuyeyo.

   (Tenor ndi Bass):
   Pakugwira nchito yace, timakondatu, E, timakondatu,
   Pakugwira nchito yace m'munda wa Ambuyeyo.

2. Mokondwera tidzanena nthano ya cikondi cace m'dzikoli.
   Mu ulemerero wa Atate atipatsa madalitso 'ce.

3. Pomtsatira Mbuye wathu Yesu, Pakuyenda naye m'njiramo,
   Tidzatsogolera otaika, kuti anke kwa Ambuyeyo.

No. 291
AYENERA YESUYO
Arranged
Doh is D.

1. Ayenera Yesuyo, Ayenera Yesuyo,
   Ayenera Yesuyo, Wophedwa.

   CHORUS:
   Yimba aliluya! Tama aliluya!
   ‘Lemu aliluya! Wophedwa!

2. Mpulumutsi idzani, Wonongani ucimo,
   Zaka cikwi zifike, Yesuyo.

3. Timve conco m’mtimamu, Kumyamika, kumkonda,
   Mpaka tilowe m’Mwamba Kum’wona.

No. 292
TIMANJA TIWIRI
W.A Ogden
Doh is D

1. Timanja tigwire nchito yace, Lilime limlemekeze,
   Makutu amve mau ace, Mau ayimbetu nyimbo.

   CHORUS:
   Tidzatu, Ambuye, Tidzatu tikali ana,
   Tidzatu, Ambuye, Kumva za Inu.

2. Timapazi tiyende m'njirayo, Yopita nayo kumwamba:
   Timaso tiwerenge Bible, Linena cikondi cace.

3. Kamtima ndipereka kwa Yesu, Apulumutse moyowu
   Kuti ndigwire nchito yace, Ndikhaletu wace konse.

No. 293
AGOGODA NDANIYO?
F.E. Belden
Doh is G

1. Agogoda ndaniyo?
   Alindira, Abwino!
   Ndiye mlendo wacifundo,
   Wina palibe mnzace,
   Ine ndiri wozizwadi
   Nditsegulire khomo;
   Nditsegulire khomo.

2. Agogoda pompobe,
   Alindira, Abwino!
   Citseko cilimbiranji
   Zitsotso zomelera
   Zomatirira zakuda,
   Zomamatira zonse,
   Zomamatira zonse.

3. Agogoda, catani?
   Alindira Abwino;
   Indetu agogodabe
   Ndi cisoti ca minga,
   Mpulumutsi lindabe.
   Kodi sungamlowetse;
   Kodi sungamlowetse?

No. 294
YANG'ANA YESU
F.E. Belden
Doh is E flat

1. Yang'ana Yesu wosacimwa; Tate wampatsa moyo wace.
   Moyo wa imfa, ndi wa tsoka, Wandibveka ndi moyo wace.

   CHORUS:
   Moyo wacewu, Woyeretsa; Ine ndadziwa moyo wace;
   Moyo wa tsoka ndi wa imfa Moyo wangwiro ndabvekedwa.

2. Zocimwa zanga zinampweteka, Chimo nloopsa lofiira,
   Mundibvundikire Inu Yesu, Ndipulumuke ciweruzo!

3. Ndilakalaka akhulululuke Yesu ambveke zoyera;
   Ndatembenuka zanga ntaya, Ndalandiridwa mokondwera.

4. Ndayanjanadi ndi Mulungu, Ndayesedwatu wolungama;
   Ndayeretsedwa ndi mauwo Ndalemerera mwa Ambuye.

No. 295
MEMA NKHONDO
William F. Sherwin
Doh is B flat

1. Mema nkhondoyo, wadza mdaniyo,
   Kweza mbendera ya Mbuye.
   Konza zidazo, yimba nyimboyo,
   Khazikikatu pa Mulungu.

   CHORUS:
   Haya! ’nzathu, itilinda nkhondo,
   Limbanitu, nkhondo nja Yesu.
   Musafoke, M’thyole linga lao,
   Mbuye ndi kazembe wathuyo.

2. M’lake mdaniyo, m’yimbe m’njoramo,
   Mpaka nkhondoyo ileka.
   Zida bvalani, mantha tayani,
   Pitikitsani adaniwo.

3. Mlungu, mumvefe, m’patse mphamvuyo,
   M’tithandizetu, tipempha.
   Nkhondo itatha, titagonjetsa,
   Mutipatse krona wa moyo.

No. 296
MUNDITSOGOLERE, MBUYE
Frank M. Davis
Doh is D flat

1. Mbuye, tsogolereni, Bwino, bwino panjira;
   Ndipezamo mtendere, Ndidzakhala wokondwa
   Mkatsogola. Ndiopa kutaika (Mbuye),
   Poti moyo uzunza (zunza), Tsogolereni Mbuye (Ambuye).

2. Thanthwe langa ndi Inu, Ndikabvutika m'moyo;
   Mukakhala pafupi, Sindimaopa kanthu
   Mkatsogola. Ndiopa kutaika (Mbuye),
   Poti moyo uzunza (zunza), tsogolereni Mbuye (Ambuye).

3. Mtsogole mpaka komwe, Kudzathera zobvuta,
   Dzikolo la usana, Misozi adzacotsa
   Mkatsogola. Ndiopa kutaika (Mbuye),
   Poti moyo uzunza (zunza), Tsogolereni Mbuye (Ambuye).

No. 297
MACIMO ATSALA PA MTANDA
Grant Colfax Tullar
Doh is F

1. Mmodzi nalola kufa m'malo mwa ine,
   Wosayenera'ne ndikhale,
   Njira yopita ku mtanda anayenda,
   Anandikhulukiradi.

   CHORUS:
   Zocimwa pa mtanda, Zocimwa pa mtanda,
   Anapirira koposadi! Nasauka nafa,
   Pa mtandapo Yesu! Anasenza macimo anga.

2. Wondikonda inetu, wacifundoyo,
   Potsuka mtima wanga woda,
   Ndiribenso mulandu ndamasulidwa,
   Macimo atsala pa mtanda.

3. Mpulumutsi wangayu ndiumirira,
   Nkamayenda tsiku ndi tsiku,
   Nyimbo iri pakamwa ndi mu mtimanso,
   Kuti macimo acotsedwa.

No. 298
NDIRIBE ZANGA, ZONSE NZANU
James McGranahan
Doh is C

1. Ndinali nayotu nthawi Yowawa yacisoni,
   Ndinauza Yesu “Zonse nzanga ndiribe zanu,”
   Ine ndiribe canu Ine ndiribe canu,
   Monyada ndinati “Zonse nzanga ndiribe canu.”

2. Nandipeza, ndinamwona pa mtanda wopwetekwa,
   Mtimabe unati, “Zina n’zangatu zina n’zanu,”
   Zina n’zanga ndi zanu, Zina n’zanga ndi zanu
   Mtimabe unati “Zina n’zanga zina ndi zanu.

3. Tsiku ndi tsiku cifundo cace cinanditsits,
   Ndipo ndinati, “Ndicepe ndithu mukule Inu,”
   Ndicepe ine ndithu, mukule Inu Mbuye,
   Ndipo ndinati, “ndicepe ndithu, mukule Inu.”

4. Cokwera  kuposa myamba, Kuya kuposa nyanja,
   Cikondi canu caposa Tiribe kathu n’zanu.
   Ndiribe zanga, n’zanu, Ndiribe zanga n’zanu.
   Cikondi canu caposa, “Tiribe kathu n’zanu.”

No. 299
TIKONDWERE NTHAWI ZONSE
Robert Lowry
Doh is E

1. Tikondwere nthawi zonse; tidandauliranji
   Kwina ‘Tate wathu Mlungu, Atisamalirafe?

   CHORUS:
   Tikondwere nthawi zonse Ponse dzuwa liwala,
   Njira ya nchitoyi ndi yokoma
   Tikondwere konseko.

2. Dzanja lace litsogoza, Ngati chimo lidzatu,
   Nsisi zace zithandiza, satisiya tokha bi.

3. Tikaleka nchito yathu, Tidzacita mcimo;
   Ndipo mtambo wa cison, Udzaletsa cimwemwe.

4. Abwinowo akondwere, Ndi mtendere wosatha;
   Timveretu mau ace, Tikonde zokomazo.

No. 300
MPUMULO KWA OTOPA
J.W. Dadmun, arr.
Doh is C

1. Kwao Mkristu kwa ulemu, Ndi malo a mpumulo;
   Mpulumutsi anapita Komwe mtima ufuna.

   CHORUS:
   Mpumulo kwa otopa, Mpumulo kwa otopa,
   Mpumulo kwa ototpa; Mukapumadi;
   Patsidya pa Yordan, M'minda ya Edeneyo,
   Muli mtengo wa moyo, Mukapumadi.

2. Akundimangira nyumba-Idzakhala muyay,
   Ndidzakhalitsatu uko, M'dzikolo la cimwemwe.

3. Zowawa sizidzalowa, Cisoni kulibenso;
   Koma m'kati mwa mtendere, Ndidzabvala korona.

4. Imfa idzamarizidwa, Tsoka lidzacotsedwa;
   Adzapfuula mokondwa Pa tsiku la mdzukiro.

5. Yimbani olowa m'Mwamba, Yimbani cigonjetso,
   Mukadzalowa m'Ziyoni, Khomo mudzaliona.

No. 301
AMBUYE ALI PAFUPI KUDZA

1. Ambuye ali pafupi kudza, Ndikumvaconcodi.
   Ndiponso nyenyezi zikuzima, Tsopano ndi mbanda kucatu.

   CHORUS:
   Ee! Tsopano ndi mbanfa kucatu!
   Ee! Tsopano ndi mabanda kuca ndithu!
   Usiku wathandi! Usana wadzanso.
   Ee! Tsopno ndi mbanda kucatu!

2. Zizindikiro za mlengalenga Zilalikiradi;
   Ndi za pa dziko zinena kuti, Ambuye wayandikiratu.

3. Ndi nthawi yoti kunyada kuthe Mu mpingo wonsewo,
   Ukhale wofulumira nchito, Ukhale woyang'aniratu.

4. Pitani msanga kukalalika kwa osaukawo:
   Ndi kwa omveka a dziko lino; Onsewo afulumirenso.

No. 302
MULUNGU WA KUMWAMBA

1. Mulungu wa kumwamba, tabwera kunoku,
   Ndi mtima wokondera kulowa m'nyumbayi,
   Cifukwa ca zabwino mwaticitirazi,
   Titokuyamikirani leroli.

   CHORUS:
   Inde tikuyamikani Atate, leroli,
   Mwatimangira 'fe kuno kacisi wanuyu!
   Ndi ulemerero wanu mudzaze m'myumbayi;
   Muyeretse, mudalitse, munomu.

2. Tikondwa tonse ndi kukuthokozani 'Nu,
   Poyamba kupemphera ndi kuyimbiramu,
   Mom'muno nsiku zonse mukhale nafetu.
   Monga ndi angelo anu m'mwambamo.

3. Ikhale ngati nyali, yowala m'nyumbayi.
   Yakutsogoza onse opunthwa m'mdima bii.
   Akunja ndi Akristu mwapulumutse ndi
   Kuunika koturuka munomu.

No. 303
KALE ANTHU M'KHOLAMO

1. Kale anthu m'kholamo, Napembedza Mwanayo.

   CHORUS:
   Ndiye Mbuye, Mfumu yanga, Ndiye Mbuye, wakumwamba.
   Amgwadire anthuwo, Timtamande Mfumuyo.

2. Wosauka Iyedi, Anagwira nchitozi.

3. Ndani kodi munthuyo. Woyeretsedwa m'bwinjamo?

4. Analira ndaniyo, Pomwalira bwenzilo?

5. M'munda muja ndaniyo, Mwazi wace dontho do?

6. Iye ndani m'mtandamo, Anafera 'daniwo?

7. Mkuca wace ndaniyo, Waturuka m'mandamo?

8. Ndani alikudzako, M'mpando wakuyeramo?

No. 304
ATATE WA KUMWAMBAKO

1. Atate wa kumwambako, Munaombola ife ndi
   Cikondi canu cijaco, Tiyamikira inutu.

2. Ambuye Yesu ndinutu, Munabadwira anthu ‘fe,
   Munatifera tonse ‘fe, Tiyamikira Inutu.

3. Mzimu Woyera m’mtimamo, Tiyeretsedwe ndinunso,
   Munatisunga bwinoli, Tiyamikira Inutu.

4. Atate, Mwana, Mzimunso, Ndinu atatu mmodzitu,
   Ocimwa tinipemphako, Mutikhulululukire ‘fe.

No. 305
DZUWA LAPITA

1. Dzuwa lapita, dzuwa lapita,
   Mlungu mutigonetse phe!

2. Mdima wafika, mdima wafika,
   Mutisunge tonse bwino.

3. Tibvomereze, tibvomereze,
   Zakucimwa zathu zonse.

4. Mkhulululukire, mkhulululukire,
   Zoipazi zathu zonse.

5. Lero tigone lero tigone,
   Tigonemo mu mtendere.

6. Ndife ananu, ndife ananu,
   ‘Tate Mlungu wotikonda.

No. 306
YESU ADZAWERUZATU

1. Yesu adzaweruzatu Pomwe liwala dzuwapo.
   Wace ufumu ukhala Mpaka ku nthawi zonsezo.

2. Anthu m'mitundu yonseyo Adzayimbira dzinalo.
   Ndi ana onse ayimba, Hosana kwa Mulunguyo.

3. Kwa Iye apempheratu Kulemekeza Mbuyeyo.
   Ndi dzina lace likwera Mongatu nsembe mmwambamo.

4. Ndi anthu onse pansipo Alemekeze Mfumuyo,
   Ndipo angelo ayimba, Ayankhe onsewo, Amen.

No. 307
MUNTHU WA ZISONIYO

1. Munthu wa zisoniyo, Timucha dzina lacelo,
   Mpulumutsi dzinanso, Aleluya, ndinu Yesu.

2. Anapeputsidwako, Nandifera m'mtandamo.
   Anandiombolayo, Aleluya, ndinu Yesu.

3. Anapacikidwatu, Natha nchito yace myu!
   Anakwera mmwamba du! Aleluya, ndinu Yesu.

4. Adzabwera Iyenso, Kudzatenga acewo,
   Nyimbo tidzayimbanso, Aleluya, ndinu Yesu.

No. 308
POLENGA DZIKOLI

1. Polenga dzikoli, Pakumva Inudi, Kwayeratu;
   Mumve pempheroli, Ndipo pamenepo, Palibe mauwo,
   Muwaletu.

2. Inu wakudzatu Kuwaciritsadi A nthendawo;
   Kupatsa moyowo, Kuona m'masomo, Pa anthu onsewo,
   Muwaletu.

3. Mzimu woonadi, Ndi wa cikondico, Idzanitu.
   Mmwamba mulengemo, Pali za mdimazo, Pa dziko ponsepo,
   Muwaletu.

4. Inu Atatuwo, Wodala Mlunguyo, Timveretu,
   Ku malengedwewo, Mdima ukhalamo, Mutume mauwo,
   Muwaletu.

No. 309
NDIYENDA NAYE YESU MBUYE

1. Ndiyenda naye Yesu Mbuye, Ndikondwa nthawi zonsezo,
   Ndipeza ciyanjano caceco, Ndikwanitsidwa ndi Iye.

   CHORUS:
   Ndiyenda naye Yesu Mbuye, Ndifuna atsogoze 'ne.
   Pokangamir pa Mplumutsiyo Sinditaika konse bi.

2. Ndiyenda naye Yesu Mbuye, Ndicite cifuniro 'ce.
   Analonjeza kuthangata 'be, Adzakwanitsa zonsezo.

3. Ndiyenda naye Yesu Mbuye, Ndabvomerereza chimolo.
   Pamodzi tidayenda konseko, Mu ciyanjano caceco.

No. 310
NDIFUNA KUKHALA NDI YESU

1. Ndifuna kukhala ndi Yesu, Kuyang'ana nkhope yace,
   Adzaze mtimanga cisomo cace, Ndifuna kukhala naye.

   CHORUS:
   Khala pafupi, mfupi ndi Yesu pa mbali ya Iyeyo;
   Kuyang'ana pa nkhope yabwinoyo, Ndifuna kukhala naye.

2. Ndifuna kukhala ndi Yesu, Kumtsata pafupifupi,
   Ndi kuti ndimvetse polankhula 'Ye, Ponena lonjezo lace.

3. Ndifuna kukhala ndi Yesu, Pafupi masiku onse.
   Pogwiratu dzanja la mphamvu yace, Nkalowa m'ufumu wace.

No. 311
E, MZIMU WA MULUNGU ‘NU

1. E, Mzimu wa Mulungu, ‘Nu, Mukhale m’mtimanga;
   Ndi zangazo ndipatsatu Kwa Inu, Mbuyanga.

   CHORUS:
   Mdzaze ‘ne, mdzaze ‘ne, Mdzaze Mzimu Woyera ‘Nu.
   Mdzaze ‘ne,mdzaze ‘ne, Wanu ndikhaletu.

2. Ndifunatu kucitadi kufuna kwanuko;
   Sin’funa kanthu kena bi, Mndidzaze, mtimamo.

3. Ndiribe kanthu kabwino, Kopatsa Inuyo;
   Mutsuke mtima wangawo, Ndi mwazi wanuwo.

No. 312
TAITANIDWA KUBATIZIDWA

1. Taitanidwatu, Kuli mtsinje Yordan:
   Ife tinamvadi Mau mcipulumo.

   CHORUS:
   Ife tafikadi Kubatizidwamo,
   Kuti titsukidwe Mphulupulu zathuzo.

2. Tamva Uthengawo, Wa cikondi caceco.
   Lapani m'mtimamo, Yesu ali kudzanso.

3. Yesu anenanso, Yemwe akhulupira,
   Nabatizidwa 'ye, Adzapulumukadi.

4. Tiyamikiratu Nsisi zace Yesuyo;
   Watiturutsadi Mdima wa zoipazo.

No. 313
PA UBATIZO

1. Atate muwapenye Anzathu onsewo;
   Abvomereza dzina La Yesu Kristuyo;
   Alonjezetsa lero Kutsata Mbuyeyo,
   Mwthangatire iwo Asabwererenso.

2. Onsewa afa ndithu M’zoipa zawozo;
   Tsopano aikidwa Ndi Kristu m’mandamo;
   Auke iwo onse Kuyenda nayeyo;
   Apemphe nthawi zonse Ndi kudya mauwo.

3. Muwalimbitse, Mbuye, Kuyenda m’njiryi,
   Ndi kugonjetsa mdani Masiku onsewo;
   Muwathangate iwo Kukopa enawo,
   Amene ali kufa M’zoipa zawozo.

No. 314
ANYAMATA INU

1. Anyamata inutu, Atsikana inunso,
   Muti, Tingacitenji, Ang'ono ndifetu,
   Kuthandiza ufumu Wa Yesu?

2. Aphunzitse anthuwo, Awalalikiredi,
   Akukhala moipa Mu mdima wakunja,
   Alowetu m'ufumu Wa Yesu.

3. E! ang'ono ndifetu, Nzeru sizimafika,
   Kuti tingaphunzitse. Titani tonse 'fe,
   Kuthandiza ufumu Wa Yesu?

4. Inu nonse, anzanga, Titoganiza bwino,
   Tinganene mofatsa, Timverenso, Mbuye,
   Kuthandiza ufumu Wa Yesu.

5. Pothandiza amathu, Pakwakonda anzathu,
   Pakusiya zoipa, Pokhaladi bwino,
   Tithandiza ufumu Wa Yesu.

No. 315
MMENE INE NDIRI MWANA

1. Mmene ine ndiri mwana Ndzaphunzira zacezo;
   Ndidzamtsata Yesu yekha, M'njira ya mabvutoyo.

   CHORUS:
   Inde, Yesu andikonda, Ine ndikudziwadi
   Kuti Yeu andikonda, Nandifera kalelo.

2. Ndzanka komwe andiuza Sinnacepe konse bi.
   Pakuyenda m'njira yace, Pena mcifuniro 'ce.

3. Iye Mpopulumukira Kwa zoipa zathuzo,
   Iye anditsogolera, Ndikalowe mmwambamo.

No. 316
TIRI OTUMIKA

1. Tiri otumika A Yesu Kristuyo,
   Tapangana tidzagwira nchito ya Ambuye.

   CHORUS:
   Ndifetu! Ndifetu! Otumikawo,
   Ndifetu! Ndifetu! A Ambuyeyo.
   Tsiku liri lonseli, caka ncakanso,
   Tidzagwira nchito yace, otumika ‘fe.

2. Anyamata onsewo, atsikananso,
   Tisatsate dziko lino, koma Yesu mwini.

3. Akufuna onsewo m’nchito yaceyo,
   Tionetse za cikondi ndi cisomo cace.

4. Mpaka Yesu adzanso, tidzagwirabe,
   Tifuna kudzamva mau, “ Munacitaa bwino.”

No. 317
ANAKWATIRA KALE

1. Anakwatira kale pa Eden pajapo;
   Ulipo lero lino, Mdalitso womwewo.

2. Awiri aimamu, Mwana ndi mkaziyu,
   O! Mzimu wakuyera Mdalitso mpatsetu.

3. Mulunzanitse awa, Atate leroli;
   Munakwatits' Adamu ndi Hava kalelo.

4. Mukhale nawo Yesu Mongatukaleko,
   Ukwati mnadalitsa Pa Kana pajapo.

5. Mwasunge, mwayendetse Mu njira yanuyo,
   Akhale ndi kudala Pa banja pawopo.

No. 318
TSIKU LA SABATA

1. Tsiku la Sabatalo, Mlungu nalipatula;
   Atalenga zonsezo, Mbuye napumulanso.

   CHORUS:
   Tsiku la Sabatalo, Mlungu nalidalitsa;
   Kukumbutsa ife za Mphamvu ya kulengayo.

2. Musafune za dziko, Ndi zokondweretsazo,
   Kuli zopambanadi M'dziko la kumwambako.

3. Pakuyamba tsikulo, loweruka madzulo,
   Tisonkhane tonsefe, Kuyambira Mbuyeyo.

4. Tipemphere nsisizo, ndi gonjetso lacelo,
   Kuti athangate, 'fe Kulisunga tsikulo.

No. 319
NDIDZAYIMBA ZA MULUNGU

1. Ndidzayimba za Mulungu, Za kukonda kwaceko,
   Watumiza mwana wace, Kundifera kalelo.

   CHORUS:
   Inde ndidzayimba nyimbo, Ya kukonda, kondako kwaceko,
   Ndidzayimba ndi angelo, Akukhala m’mwambamo.

   (Bass, Alto, ndi Tenor ):
   Yimbatu, ndiyimba nyimbo; Kondako, kondako, yimbatu;
   Angelo omwe, Akukhala m’mwambamo. E, M’mwambamo.

2. Ndinacita mphulupulu, Waiwala zonsezo,
   Ndinakhala ndi zoipa, Wazicotsa zonsezo.

3. Wandipatsa moyo wace, Moyo wakuyera mbu,
   Ine ndiri mwana wace, Wandilera inetu.

4. Ndiyamika Mbuye wanga, Ndidzamlemekezatu,
   Ndipititsa mbiri yace, Ya kukonda kwaceku.

No. 320
YESU WATHU MBUYEYO

1. Yesu wathu Mbuyeyo alandira onsewo,
   Akuipa omwewo, osocera mtarimo.

   CHORUS:
   Yimba kawiri ndi kawirinso, Yesu Ambuye sakanatu,
   Mvetsa uthenga wabwinowo, Wakucimwa adzetu.

   (Bass ndi Tenor):
   Yimba, yimbatu, Yimba, yimbatu,
   Yesu Ambuye, indetu, sakanatu, sakanatu;
   Mvetsa,mvetsadi, E, wabwinowo,Wakucimwa adzetu.

2. Idzatu kwa Yesuyo, apumitsa inunso,
   Inde m’mtima mwanumo ndi mtendere wacewo.

3. Walandira inetu tsiku lija kalelo,
   Wanditsuka ine mbu m’mtima mwanga momwemo.

4. Wandifera Yesuyo pansi pano kalelo,
   Sindiopa mlanduwo pakubwera Iyeyo.

No. 321
MWAMVA MAU A MULUNGU

1. Mwamva mau a Mulungu, Mukabvomeranjiko?
   Kodi musanduka mtima, Ndikumvera Yesuyo?

   CHORUS:
   Bvomerani, bvomerani, Bvomerani msangatu (etu)
   Musacedweranso ai, Landira Yesuyo.

2. Munacita nthantha kale, Musacedweransobi;
   Yesu ali kulindira, Inu sadzakanai.

3. Musaope kaamba zinthu Zakuipa zanuzo;
   Mukakhulupira Yesu, Akacotsa zonsezo.

4. Perekani mtima wanu, Kwa Mulungu wathuyo,
   Mkhulupire kuti Yesu, Watifera kalelo.

No. 322
MAU NGONYOZEKATU

1. Mau ngonyozekatu, Anenedwa msanganso;
   Timawaiwaladi, Komabe pa mlanduwo
   Adzatinenezafe, Poweruza Mlunguyo.

2. Ife timalankhula, Mosaganiziratu,
   Mau akunyadawo, Ndi obisa chimolo,
   Mau akukwiyanso, Ndi onena enawo.

3. Mbuye, tipatsenife, Mphamvu yodikirayo,
   Mtitsogoze, Mbuye'Nu, Tisacimwe m'mauwo,
   Mmwamba tidzaimbetu, Nyimbo zoyamika'Nu.

No. 323
MBUYE NDAPANGANA

1. Mbuye ndapangana M’njir yanuyi,
   Kuti ndidzayenda Osalekai.
   Mundipatse mtima Wopiriramo,
   Wakukana zonse Zondipingazo.

2. Mzimu wakuipa Undiyesa ‘ne,
   Mundithangatire Kuthawitsabe.
   Akandisautsa Kumdzi kunoku.
   Mulowetse mphamvu M’mtima mwangamu.

3. Akathira nsembe Ku mizimuyo,
   Ndipenyere kwanu Ee, kumwambako.
   Tsoka ndi zonyenga Za ufitizo
   Yesu, mndilimbitse, Ndisaopezo.

4. Pena kumwa nao, Ndisateroko,
   Pena kukaona Za kubvinazo.
   Pena kuombeza Sindifunai;
   Yesu mndithandize Kuzikanazi.

5. Ndinu Mbusa wanga, Mndithandizetu,
   Ndisaipse nazo Mtima wangawu.
   Osaopa konse, Osacimwa bi,
   Mndiyendetse Yesu M’njira yanuyi.

No. 324
T’YIMBE NYIMBO YOTIKONDWETSA

1. T’yimbe nyimbo yotikondwets m’njiramo,
   Tidzafika kwathu msangatu;
   Ndipo posacedwa usiku ‘dzapita,
   Posacedwa tidzafikako.

   CHORUS:
   Posacedwatu posacedwatu,
   Tidzafika tsidyalo.
   “Dzakomana” fe potha anamondwewa.
   Posacedwa tidzafikako.

2. Tidzagwira nchito imene tipeza,
   Tidzafika kwathu msangatu,
   Adzatilimbitsa mwa nsisi zacezo,
   Posacedwa tidzafikako.

3. Tidzakonza njira kwa anthu otopa,
   Tidzafika kwathu msangatu.
   Tidzakopa anthu m’cikondi caceco,
   Posacedw tidzafikako.

4. Tidzapumuladi pa tsidya la myanja.
   Tidzafika kwathu msangatu.
   Anthu sadzalira mu mzinda wowala,
   Posacedwa tidzafikako.

No. 325
PAKUPEMPHA IFE PANO

1. Pakupemphera ife pano, pakwitana ’Tateyo,
   Podziwitsa m’mtima mwanga, bweratu kwa Mbuyeyo.

   CHORUS:
   Idzatu, idzatu,kwa Mbuyathu Yesudi,
   Idzatu, idzatu, iwe bwera leroli.

2. Unacimwacimwa ndithu, wasocera mtarimo,
   Unacedweranji kudza pa kulinda yesuyo?

3. M’dziko lino pansi pano sukapeza kanthumo
   Kokwanitsa mtima wako, bweratu kwa Mbuyeyo.

4. Bvumbulutsa zonse zako zobisika m’mtimamo,
   Ayeretsa moyo wako nao mwazi wacewo.

No.326
MPINGO WA AKRISTU ‘FE

1. Mpingo wa Akristu ‘fe, tikondwera mwa Ambuye.
   Tinka m’dziko labwino, tikondwera mwa Ambuye.

   CHORUS:
   Mpulumutsi, Mtitsogoze bwino bwino,
   Pakupita kunka mmwambamo.

2. Timayenda bwinotu, tikondwera mwa Ambuye,
   Tigonjetsa mdaniyo, tikondwera mwa Ambuye.

3. Msanga tidzapumadi, tikondwera mwa Ambuye.
   Tidzabvala kronayo, tikondwera mwa Ambuye.

No. 327
ALIKUITANA UKO TSIDYALO

1. Alikuitana uko tsidyalo, Tumiza mauwo,
   Iwo akufuna Mpulumutsiyo, Tumiza mauwo.

   CHORUS(Bass):
   Tibukitse mau acewo, ndi mitima yonseyo,
   Pakumlemekeza Mlunguyo, Ndi kusunga mauwo,
   Tuma mau a uthengawo, Kuli konse amvetu,
   Tuma mau a uthengawo, osalema konse bi.

   (Soprano, Alto, ndi Tenor):
   Tibukitse mau acewo, Ndi mitima yakufunatu,
   Pakumlemekeza Mlunguyo, Ndi kusunga mau acewo.
   Tuma mau a uthengawo, Kuli konse amvetu,
   Tuma mau a uthengawo, Osaleka konse bi.

2. Tamva kuitana tsidya lijalo, Tumiza mauwo.
   Tipereke za cifundo zathuzo, Tumiza mauwo.

3. Tipempheretu cisomo caceco, Tumiza mauwo,
   Mzimu wa Ambuye anke ponsepo, Tumiza mauwo.

4. Tisaleme pakucita zabwino, Tumiza mauwo,
   Pakukopa anthu osocerawo, Tumiza mauwo.

No.328
NATIONAL ANTHEM (Chichewa)

1. Mlungu dalitsani Malawi,
   Mumsunge m'mtendere.
   Gonjetsani adani onse,
   Njala, nthenda, nsanje.
   Lunzitsani mitima yathu,
   Kuti tisaope.
   Mdalitse mtsogoleri nafe,
   Ndi Mayi Malawi.

2. Malawi dziko lokongola,
   Lachonde ndi ufulu,
   Nyanja  ndi mphepo ya m'mapiri,
   Ndithudi tadala.
   Zigwa, mapiri, nthaka, Dzinthu
   Mphatso zaulere.
   Nkhalango, madambo abwino.
   Ngokoma Malawi.

3. O'Ufulu tigwirizane,
   Kukweza Malawi.
   Ndi cikondi, khama, kumvera,
   Timutumikire.
   Pa nkhondo nkana pa mtendere
   Cholinga n'chimodzi
   Mayi, bambo, tidzipereke,
   Pokweza Malawi.

No. 329
NDIKONDWA KUTI ATATE

1. Ndikondwa kuti Atate wathu, Atidziwitsa cikondi cace.
   Pakuwerenga m'kalata mwace, Yesu, amati akonda ine.

   CHORUS:
   Ndikondwerera kuti Yesu Akonda 'ne, akonda 'ne.
   Ndikondwerera kuti Yesu Akonda inenso.

2. Nkana ndingamuiwale Iye, Ndikusocera kutritari,
   Andikondabe masiku onse Ndikabwereranso kwa Iyeyo

3. Pakudzamona Ambuyangayo M'ulemerero wa kumwambako.
   Ndzayimba kosalekeza konse, ndikondwa Yesu akonda ine.

No. 330
LEMEKEZ MLUNGU TATE

1. Lemekeza mlungu ’tate, lemekeza Mwananso,
   Lemekeza, Mlungu Mzimu, mlungu Mmodzi mkuruyo;
   Lemekeza, lemekeza, Mlungu wathu yemweyo.

2. Mlemekeze, anakonda, Natitsuka m’mtimamo,
   Anatiombola ife, Tikakhale nayeyo;
   Lemekeza, lemekeza, Yesu Mbuye nsembeyo.

3. Lemekeza Mfumu yathu, Mfumu, Mlengi wathuyo,
   Apambana anthu onse, Pansi ndi kumwambako;
   Lemekeza, lemekeza, Mfumu ya mafumuyo.

No. 331

TAMANI MLUNGU MTIMAMO

1. Tamani Mlungu mtimamo, Wandifera pansipo,
   Nafafaniza chimolo, Nanditengera dipolo.

   CHORUS:
   Wandiombola inetu, Potaya mwazi wacewo,
   Timlemekeza Iyetu, Wotilipira dipolo.

2. Ndinacosera kalelo, Ndamkana Iye Yesuyo,
   Koma ndiyimba leroli, Wandiombola inedi.

3. Cikondwerero ciripo, Popenyetsetsa Yesuyo.
   Pa mtanda pace pomwepo, Pakundifera inenso.

4. Ndiribe nchito zangazo, Kukoma mtima wangawo,
   Anandiyesa inetu, Wakulungama Yesuyo.

5. Tsono mubwere inunso, Mombolo wanu ndiyedi,
   Apulumutsa onsewo, Okhulupira Yesuyo.

No. 332
PAKUKHALA PA MGONERO

1. Pakukhala pa mgonero, Wa Ambuye wathuyo,
   Tionetu mwazi wanu, Muja unakheramu.
   Nkana singaone Inu, Muli mfupi nafedi,
   Mutisangalatse, Mbuye, Mcotse makaikowo.

2. Mutiuze ife nthano Ya mabvuto anuwo,
   Pakuyembekeza Inu, tisendeza kwanuko.
   Mtikokere mfupi ndi ‘Nu, Ndi ku mtanda wanuwo,
   Mpaka tidzione tokha, Monga mumaona ‘fe.

3. Pakucoka pa mgonera, Wa Ambuye wathuyo,
   Moyo wathu ufanane, Ndi wa Mbuye wathuyo.
   Pakutsanza moyo wace, Tisanduka Iyeyo,
   Timuchula Mbuye wathu, pakumvera mau’ce.

No. 333
TIKAGWIDWA NDI CISONI

1. Tikagwidwa ndi cisoni, Ikayendanso misozi,
   Poliratu abale, Yesu mutimveretu.

2. Munabvala thupi lathu, Munadziwa masauko,
   Mnalirira bwenzi lanu, Yesu mutimveretu.

3. Mmene imfa yathu idza, Mweya wathu ukaleka,
   Mmene ife timwalira, Yesu mutimveretu.

4. Mnamwalira Inu paja, Mwazi wanu munataya,
   Inu munagona m’manda, Yesu mutimveretu.

No. 334
MMENE INE NDISAUKA

1. Mmene ine ndisauka Ndi zoipa zangazo,
   Ndidzapita kwa Mulungu, Adzandilandiratu.

   CHORUS:
   Mlungu adzandilandira, Iye ndiye Atate wanga,
   Watumiza Mwana wace, Andifera kalelo.

2. Ngati atsamwali anga Sandikonda ine bi,
   Ndikhulupire Mlungu, Iye sandikanai.

3. Pansi pano ndiri mlendo, Kwathu ndi kumwambako,
   Mmene adzabwera Yesu Ndidzapita komweko.

No. 335
POFUNAFUNA M’MALEMBO ACE

1. Pofunafuna m’malembo ace, Pofuna Mpulumutsiyo,
   Momwe tikumva za Ambuye, Bible amati c’ani ko?

   CHORUS:
   Pita, kafunse, ati Mfumu, Ka’mba ka iwe, ndinetu.
   Pita, gogoda khomo lace, Komwe udzapumulako.

2. Pofunafuna m’malembo ace, Tiri kufuna njirayo
   Yonka ku mzinda wopambana, Bible amati c’ani ko?

3. Pofunafuna m’malembo ace, Pofuna otaikawo.
   Kuwatsogoza kwa Ambuye, Bible amati c’ani ko?

No. 336
USIKUWO WOYERAWO

1. Usikuwo woyerawo, Mwana adamlerayo,
   Akakhale Mfumuyo, Anabadwa m'kholamo.
   Mfumu ya Mafumu. Ndi ya anthuwo.

2. Mwanayo wa Mulunguyo, Andikonda inetu,
   Nantayira cumaco, Nadzagona m'udzumo,
   Ndiyamika Mbuye Wanga Yesuyo.

3. Usikuwo woyerawo, Nudzatu mtenderewo,
   Ife tonse anthuwo, Atitenga Mlunguyo;
   Mlemekeze 'Tate, Mwana, Mzimunso.

No. 337
PAMENE NDIDZAUKANSO

1. Pamene ndidzaukanso tsikulo, komwe kulibe mdima konse bi.
   Ee! Ulemerero ’dzawaliramo, Ndidzakwnitsidwatu.

   CHORUS:
   Ndidzakwanitsidwatu Ndidzakwanitsidwatu.
   Pamene ndidzaukanso tsikulo, Ndidzakwanitsidwatu.

2. Pamene ndidzamuona Iyeyo, Nandilandira mokondweratu,
   Pakumva cisomo ca Ambuyeyo, Ndidzakwanitsidwatu.

3. Pokomana nawo okondedwawo Omwe mwa imfa nandisiy ’ne,
   Pomwepo ineyo ndidzamtama ’Ye, Ndidzakwanitsidwatu.

4. Ndidzamona Yesu posacedwatu, Iye amene nandifera ’ne.
   Ndidzamuyimbira kosalekadi, ndidzakwanitsidwatu.

No. 338
UTSEGULE PA KHOMO

1. Utsegule pa khomo, kuti Yesu alowe;
   Ndi ngati ulola ’dzacotsa chimo.
   Tsegulatu mtimawo.

No. 339
MPATSE YESUU MTIMA WAKO

1. Mpatse Yesu mtima wako wonsewo,
   Alikuitana iwe Mbuyeyo;
   Mpatse Yesu mtima wako leroli;
   Mpatsetu mtimawo.

No.340
TAYA ZOBVUTA ZAKO

1. Taya zobvuta zako, Taya zobvuta zako.
   Ambuye adzacotsa zonsezo, Taya zobvuta zako.

No. 341
MDZAZE ‘NE NDI MZIMU

Mdzaze’ne ndi Mzimu, Mzimu wanu, Mbuye.
Mundipange wanuyo, Mdzaze’ne ndi Mzimu.

No. 342
MBUYE, MUMVETU PEMPHO LATHU

Mbuye, mumvetu Pempho lathulo,
Mtipatse tonsefe Mtendere wanu. Amen.

No. 343
MTICITIRE CIFUNDO

Mticitire cifundo, Ambuye,
Mtithandize kusunga lamulo. Amen.

No. 344
USIKU UNOWU

Usiku unowu, Mtisunge Mbuyathu,
Angelo asamale’fe, Kufikira mawa. Amen.

No. 345

MMENE TIPITA KWATHU

Mmene tipita kwathu, Mbuye, Mutidalitse m’njira zathu;
Mtitsogolere tsiku lonse, Kuti tilowe kumwambako.

No. 346

# AMBUYE ALI M'NYUMBA YACE

Ambuye ali m'nyumba yace, M'kacisi wace wakuyera,
Akhale cete onse, Akhale cete pa maso pace.
Akhale mwa cete, mu nyumbayi. Amen.

No. 347
PATSENI WINA,MBUYANGA

Patseni wina, Mbuyanga, Yosowa Inuyo;
Ndicite mbali yangatu, Kumkopa iyeyo.
Kumkopa iyeyo; Kumkopa iyeyo;
Ndicite mbali yangatu, Kumkopa iyeyo.

No. 348
YANG’ANA KWA YESU

Yang’ana kwa Yesu, Ee! Yang’anitsitsani ‘Ye!
Ndipo za pa dziko zizimadi, Pakuona kuwala kwace.

No. 349
MU MTIMANGA

Mu mtimanga, mu mtimanga, Lowanu, ambuye Yesu
Lowanitu, mukhalemo, Lowani, Ambuye Yesu.

No. 350
MUTITSITSIMUTSE

Mutitsitsimutse, Ambuyathu Yesu,
Mutitsitsimutse, Muyambire ineyo.